# MALAMULO OYENDETSERA DZIKO LA MALAWI

# CHIDZIWITSO PAKUSINTHA KWINA PA KONSITUSHONI

Bukhu la malamulolo (konsitushoni) lakhala likusinthidwa mbali zina kuchokera pamene lidayamba kugwira ntchito mu 1995. Zina zosinthazo zaganiziridwa m'bukuli koma zina zomwe zasinthidwa posachedwapa sitinathe kuziikamo. Mwachitsanzo, lamulo lokhazikitsa nyumba ya 'Seneti' lomwe linali mbali ina ya gawo 6 ya konsitushoni lidachotsedwa. Kotero, zones zotchula Nyumba ya 'Seneti' mgawo limeneliu ndi magawo ena m'bukhuli nzosagwiranso ntchito.

Nkoyenera kuwerenga bukhuli mozindikira makamaka zomwe nyumba ya malamulo ikuchita posintha zina ndi zina.

# MALAMULO OYENDETSERA DZIKO LA MALAWI

Bukhu la malamulo oyendetsera Boma ndi Bukhu Limodzi Limene lili lofunika kwambiri ku dziko lililonse. Bukhu limanena mfundo zopangidwa ndi olilemba ndipo limafungatira chikhulupiliro cha atsogoleri ache ndiponso kuunika kwa mbadwazonse zadziko m'mene zingakhalire.

Mwakupempha kwa a Supikala wa ku nyumba yamalamulo ndi Kalaliki wa nyumba yamalamulo ndi kalaliki wa nyumba yamalamulo, a National Democratic Institute for International Affairs (NDI) adzipereka kuti apereka bukhu lamalamuloli lolembedwa m'chingerezi ndi m'chichewa kwa aphungu onse anyumba yamalamulo. A National Democratic Institute for International Affairs alinso ndi chikhulupiliro kuti mtsogolomu aperekanso bukhuli lolembedwa m'chitumbuka ndi m'chiyao.

Ntchito yonseyi sinakakhala yotheka kupanda kuzipoereka, kulimbikira ndi kuikapo mtima kwa anthu awa:

- Olemekeka a Louis Chimango, phungu wa nyumba yamalamulo
- Foster Mijiga waku National Democratic Institute ndi
- Ken Manda waku National Democratic Institute

Tili ndi chikhulupiliro kuti bukhuli likhala lofunikira kwa inu popitiliza ntchiyo yanu ngati aphungu akunyumba yamalamulo. Tilinso ndichikhulupiliro kuti pazikhala nthawi yoti mudziwadziwitsa anthu zolembedwa m'bukhuli kumadela omwe mukuchokera.

# ANTHU A MUNO M’MALAWI

Pozindikira kuti moyo wamunthu ndiponso umodzi pakati pa anthu onse olengedwa ndi zinthu za mtengo wapatali;

*Motsogozedwa* m’maganizo awo atadzisanthula komanso pofuna nzeru za iwo onse;

*Pofuna* kuti ubwino pamiyoyo ya anthu onse ndi chitukuko pa iwo zizakhazikike, kuphatikiza mtima wakuti ndife a Malawi ndipo pafunika mtendere pakati pa mayiko;

*Pofunitsitsa* kuti tikhazikitse Malamulo okhazikika oyendetsera Boma la Malawi lochita zinthu poyera, lotumikira olamulidwa ndi losabisira anthu;

PANO tikukhazikitsa Malamulo awa oyendetsera Dziko la Malawi.

## MUTU 1

## DZIKO LA MALAWI

1. Dziko la Malawi ndi Boma palokha ndipo lili ndi ufulu onse komanso lidzamvera Malamulo Akulu a Maiko onse a dziko lapansi.

2. Malawi adzakhala ndi Mbendera ya chizindikiro cha dziko, chizindikiro cha Maulemu, Nyimbo ya Mtundu wake ndiponso Chidindo cha Boma.

3. Dziko la Malawi ndilo mitunda yonse, kuphatikiza mlengalenga, Nyanja, mitsinje ndi zilumba zomwe zinali zadziko la Malaw Malamulo oyendetsera Boma awa asanayambe kugwira ntchito, ndiponso mitunda imene ingadzalandiridwe motsata malamulo polonzanso malire kapena kusintha kulikonse.

4. Gawo la Mutu wa Boma, Gawo lopanga Malamulo ndi Gawo la Chiweruzo, onsewa agonjere Malamulo oyendetsera Boma ndipo a Malawi onse adzitetezedwa ndi Malamulo amenewa komanso ndi Malamulo ena onse mosakondera.

5. Zochitika ndi Boma kaya lamulo lililonsezidzakhala zopanda mphamvu ngati zitsutsana ndi Malamulo ano.

6. Pokhapokha ngati Malamulo ano anenera mwina, mphamvu yolamula ichokera kwa a Malawi podzera nkaundula wa chisankho cha onse mosasankha pachisankho chochitika motsata malamulo ano mogwirizana ndi ndondomeko za Malamulo ena.

7. Gawo la Mutu wa Boma lidzakhala ndi ntchito yokonza mfundo ndi malamulo ndi udindo wogwiritsa ntchito Malamulo ofuna opititsa mtsogolo mfundo za Malamulo ano.

8. Pomakhazikitsa malamulo, Gawo Lopanga Malamulo, lizionetsetsandikuganizira zofunaza anthu onse m'Malawi muno ndiponso lizipititsa mtsogolo ubwino umene Malamulo ano afuna

9. Gawo lachiweruzo ntchito yake ndikutanthauzira, kutchinjiriza ndi kugwiritsa ntchito malamulo ano ndi malamulo ena onse motsatana ndi malamulo ano. Potero, lichite mwaiol lokha mopanda kuganizira za umo ena angafunire, koma poganizira kuti nkhani yagona pati, nanga malamulo pankhaniyo akuti bwanji.

## <u>MUTUII</u>

## KAGWIRITSIDWE NDIKAMASULIDWE

10.

(1) Potanthauzira malamulo onse ndiponso kuti kusiyana maganizo chifukwa cha ndale kuthe, Malamulo ano adzakhala mathero a nkhani yonse.

(2) Pogwiritsa ntchito kapena kuganizira lamulo komanso pogwiritsa ntchito malamulo akale kapena okhudza miyambo yathu, magawo a Boma adzitsatira ndondomeko za malamulo ano.

11.

(1) Mfundo zotanthauzira Malamulo ano zidzakhazikitsidwa ndi kugwiritsidwa ntchito ndi oweruza omwe adzaonetsetsa kuti zikugwirizana ndi m'mene mphamvu za Malamulo ano zilili.

(2) Pomasulira zimene zalembedwa mu malamulo ano bwalo loweruza-

a) Lizipititsa mtsogolo mkhalidwe wochita zinthu poyera komanso mokomera anthu:

b) Lizitsatira mfundo zimene zakhazikitsidwa pa Mutu III ndi Mutu IV; komanso
c) Ngati kungatheke, liziganizira mwambo wa mayiko onse ndi kugwirizana ndi m'mene mabwalo oweruza m'mayiko adagamulira pa nkhani za mtundu womwewo.

(3) Bwalo la chiweruzo likagamula kuti zimene lachita gawo la Mutu wa Boma kapena lamulo lomwe lagwira ntchito zilibe mphamvu chifukwa zasiyana ndi malamulo ano, bwalolo lingathe kutanthauzira ndi kugwiritsa ntchito zochitikazo kapena lamulolo mogwirizana ndi Malamulo ano.

(4) Lamulo sililoledwa kulanda mphamvu ndipo silidzagwira ntchito ngati lichotsamphamvu za mabwalo a milandu pa nkhani za malamulo ano.

## MUTUIII

## MFUNDO ZOKHAZIKIKA

12. Malamulo ano ndi wokhazikika pa maziko awa:

Mphamvu za malamulo ndi ulamuliro wa Boma ndizochokera kwa eni ake a Malawi ndipo zigwire ntchito motsata Malamulo ano kuti zithandize ndi kuteteza zofuna zawo.

Onse amene ali ndi udindo woyendetsa Boma alamula m'malo mwa amalawi ndipo ayendetse Boma motsata lamulo ndi udindo umene ali nawo kwa aMalawi.

Mphamvu yoyendetsa Boma ingakhalepo ngati chikhulupiliro cha anthu chikupitirira pa Boma, ndipo chikhulupilirochitha kupitirira ngati zinthu zikuchitika poyera, motsata zofuna anthu popanda kuwabisira.

Popeza kuti munthu aliyense adababadwa ndi ulemu wake, Boma ndi anthu onse azindikire ichi ndikuteteza ufulu wachikhalirewu ndipo nkofunika kuteteza mokwana ufulu ndizoyankhula za anthu onse, mabungwe ndi ena ngakhale ali mbali yaying'ono chabe yachiwerengero cha cha anthu ngakhale apande kuloledwa kuchita nawo voti.

Poti anthu onse ndiwofanana pa maso pa lamulo, palibe chonyozera ufulu koma kuti anthu adzikhala mwa bata ndi mtendere popanda chobisika komanso molemekeza chifuniro chawo.

Mabungwe ndi anthu onse agwiritse ntchito ndikulemekeza Malamulo ano ndikuopa mphamvu za malamulo, palibe bungwe kapena munthu uyo angapambane mphamvu za lamulo.

13. Boma lidzapititsa patsogolo ubwino pa umoyo wa anthu ndi chitukuko cha Amalawi pogwiritsa ntchito mfundondi malamulo amene angathandize kuti zinthu izi zikwaniritsidwe.

***(a) Kuti anthu onse akhale ofanana***

Amayi apeze mwayi umene amuna ali nawo poonetsetsa kuti:

i) Amayi ali akuchita nawo ntchito zones zomwe Amalawi anzawo akuchita popanda tsankho pakati pa iwo ndi amuna;

ii) Pogwiritsa ntchito mfundo zokanatsankho ndi zina;

iii) Pogwiritsa ntchito mfundo zokonza zabwinopa umoyo wa anthu monga kuti pasamakhale ndewu ndi phokoso pa anthu, kuona kuti anthu salikukhala mwa chewuchewu, amayi sakusowa chithandizo pa ubereki, anthu asapsinjidwe pa nkhani ya chuma kapena kulandidwa mwayi wokhala ndi zinthu zawozawo.

***(b) Kudya bwino***

Kuonetsetsa kuti anthu onse akudya bwino kuti azidzidalira pa nkhani ya zakudya.

***(c) Umoyo***

Kupereka chithandizo chokwana pa za umoyo mofanana ndi zofunika pa umoyo wa aMalawi, komanso potsatira mfundo za mayiko onse pa nkhaniyi.

(d) Kusamala za chilengedwe

Kusamala zachilengedwe moyenera:

(i) Kuti zachilengedwezo zitetezedwe ku zinthu zoononga;

(ii) Kupereka mwayi oti anthu azikhala ndi moyo wathanzi ndikugwira ntchito zawo mwaubwino m'Malawi;

(iii) Kupereka ufulu ndi mwayi kwa mibadwo ilinkudza poteteza zachilengedwe ndi kuonetsetsa kuti chitukuko cha zolengedwa chili kupita mtsogolo;

(iv) Kusungitsa ndikupititsa mtsogolo mitundu yonse yachilengedwe m'Malawi.

***(e) Moyo wa anthu kumidzi***

Kupititsa mtsogolo umoyo wa anthu kumidzi ndi kuzindikira kuti mfundo za Boma zingadziwike kuti zili kugwira ntchito ngati miyoyo ya anthu kumidzi isintha.

**(f)** ***Maphunziro***

Kupereka chithandizo ndi zipangizo zokwanira kumbali ya maphunziro ndikukonza ndondomeko kuti:

(i) Umbuli uthe m'Malawi

(ii) Aliyense ayenera kuphunzira ndipo maphunziro a pulayimale akhale osalipira kwa nzika za m'Malawi zonse;

(iii) Kupereka mwayi oti anthu ambiri achite nawo maphunziro apamwamba ndikuzindikira kuti sukulu siitha, komanso;

(iv) Kupititsa mtsogolo mfundo zothandiza umodzi ndikuthetsa kusagwirizana chifukwa chakusiyana pa ndale, chipembedzo, khungu kapena mtundu.

***(g) Olumala***

Kuthandiza olumala poona:

i) Kuti azikhala ndi mwayi pa malo alionse pokumana anthu;

ii) Kuti ali ndi mwayi wonse wopeza ntchito, komanso

iii) Akhale ndi mwayi ochita nawo kapena kukhala nawo pa zones zochitika m'Malawi.

***(h) Ana***

Kulimbikitsa ndi kupititsa mtsogolo zones zothandiza ana kuti akule ndi moyo wabwino namadzipezera zinthu ngati nzika zodzidalira.

***(i) Banja***

Kuzindikira ndikuteteza banja chifukwa ndilo maziko ofunika pa umunthu.

***(j) Okalamba***

Kulemekeza ndikuthandiza okalamba powapatsa mwayi ndipowalimbikitsa kutiazichita nawo zones pakati pa anthu awo akukhala nawo.

***(k) Zokhudza Mayiko ena onse***

Kuyendetsa Boma motsata malamulo a maiko ena onse a dziko lapansi, ndi potsogoza malamulo pazochitika, ndiponso popititsa mtsogolo m'gwirizano wa mayiko oyandikana nawo ndi mayiko ena onse.

***(l) Kuthetsa mkangano potsata njira zodzetsa bata***

Kuonetsetsa kuti njira zothandiza kuti kusiyana maganizo kuthe zikupezeka, monga pokambirana, pogwiritsa ntchito amkhalapakati, poweruza, pokhululukirana ndiponso polola ena kuti agamule nkhaniyo mosakondera.

***(m) Kulondoloza chilungamo***

Kupititsa mtsogolo bata ndi mtendere ndi kulemekezana pakati pa anthu onse powaphuzitsa, posonyeza kukhulupirika m'Boma, popereka chithandizo cha chuma mokwana, ndiponso pogwiritsa ntchito malamulo moyenera.

***(n) Kuyendetsa nkhani za chuma***

Kuonetsetsa kuti chuma chikupangika ndipo chikuperekedwa mosatsekeleza malonda kapena kupsinja mitengo, popititsa mtsogolo ntchito ya umoyo, maphunziro, chuma komanso chitukuko.

***(o) Kukhulupirika kwa anthu onse ndi ulamuliro wabwino***

Kukhazikitsa nfundo zolimbikitsa mchitidwe wosabisa, wokhulupirika makamaka pa ndalama, zinthu zimene zitagwira ntchito bwino anthu namakhutira, zingathandize kuti azidalira mabungwe owathandiza.

14. Mfundo zakayendetsedwe kadziko zili pamutu umodzi zizakhala zolondolerapa zofunika kuchitika koma a chiweruzo angazigwiritse ntchito pamene akutanthauzira ndi kugwiritsa ntchito malamulo ano ngakhale malamulo ena, kapena pogamula ngati izo alamula a Gawo La Mutu wa Boma ndizololedwa,ngakhalenso potanthauzira ndondomeko za Malamulo ano.

# <u>MUTU IV</u>

# UFULU WA ANTHU

15.

(1) Malamulo woteteza kumasuka ndi ufulu wa munthu aliyense amene ali pa Mutu uno ngofunika a Gawo la mutu wa Boma, a Gawo lopanga malamulo, mabwalo a za malamulo ndiponso mabungwe ndi nthambi zones za boma ndi onse okhuzidwa malinga ndi Malamulo m'Malawi aziwalemekeza ndi kuwagwiritsa ntchito motsata mutu uno.

(2) Malamulo oteteza ufulu wa anthu ndi zonse zothandiza malinga ndi mutu uno alemekezedwe ndi kugwiritsidwa ntchito ndi oweruza, Ombudzimani, Bungwe loteteza ufulu ndi kumasuka kwa anthu, komanso ndi nthambi zonse  za Boma kuti ufulu ndikumasuka kwa aliyense kupite mtsogolo, kutetezedwa ndikuona kuti aliyense womulakwira wakhutira kuti apititsidwa mtsogolo, pali chitetezo ndiponso chiweruzo pakakhala dandaulo lokhudza ufuluwo.

16. Munthu aliyense ali ndi ufulu wokhala ndi moyo ndipo wina aliyense saloledwa kuononga moyowo mwachifuniro chake kapena popanda chifukwa; koma sikulakwira lamuloli kuti munthu anyongedwe motsatira chiweruzo cha bwalo la milandu lolondola malamulo amene amagwira ntchito muno m'Malawi munthu akalakwira Boma.

17. Kupha anthu mwachisawawa sikuloledwa ndipo kudzaletsedwa. Wolakwira lamuloli adzalangidwa.

18. Munthu aliyense ali ndi ufulu aw iye mwini.

19.

(1) Palibe munthu adzaloledwa kuchotsa ulemu  wa mnzake.

(2) Pozenga mlandu m'bwalo loweruza kaya pa mlandu wozengedwa ndi nthambi  ya Boma, komanso polanga munthu wolakwa sikuloledwa kumuchotsera ulemu wake munthuyo.

(3) Munthu asazunguzidwe mnjira iliyonse kapena kupatsidwa chilango chozunza chosayenera kapena chomunyazitsa.

(4) Munthu asakwapulidwe chifukwa chachiweruzo cha ogamula mlandu kapena cha nthambi iliyonse ya Boma.

(5) Achipatala saloledwa kugwiritsa thupi la munthu pa ntchito yofufuzira pazaukatswiri wawo popanda kuvomerezedwa ndi mwini thupiyo.

(6) Pokhapokha ngati Malamulo ano angavomere, munthu aliyense adzikhala mwaufulu ndi mosazunzidwa, ndipo ufuluwu utanthauza kuti munthu:

a) Asamangidwe popanda kuimbidwa mlandu;

b) Asamangidwe pa chifukwa cha maganizo ake pa nkhani za ndale kapena pa zinthu zina;

c) Kuikidwa mndende chifukwa cholephera kapena kukwanitsa pangano

20.

(1) Sikuloledwa kumusala munthu mwamtundu uliwonse, ndipo malamulo adzateteza onse mokwana popanda tsankho chifukwa cha mtundu, khungu, chifukwa chakuti ndi mwamuna kapena mkazi, kapena chifukwa chachiyankhulidwen chipembedzo, maganizo ake pankhani za ndale kapena pankhani zina, kapena kuti ndi m'Malawi kapena ai, kapena chifukwa cha mtundu wake ndi kumene akuchokera, kulumala, chuma, chibadwidwe, kaya umo aonekera pakati pa anzake.

(2) Lamulo litha kuikidwa pa nkhani yoti anthu asamawasiyanitse pakati pawo ndikuthetsa mkhalidwe kapena mchitidwe otero ndipo lamulolo lingathe kugamula kuti wochita motero azilangidwa akaimbidwa mlandu ndi achiweruzo.

21. Munthu aliyense azikhala ndi zinsinsi zake, ndipo mwaizo zitanthauze kuti sikuloledwa:

(a) Kufufuzafufuza pa thupi lake, nyumba yake kapena chuma chake;

(b) Kumulanda katundu wake; kapena

(c) Kumvera kapena kuwwerenga mauthenga ake kaya ali m'makalata kapena odzera mu lamya.

22.

(1) Banja ndilo maziko okhazikika pakati pa anthu ndipo lifunika kutetezedwa ndi anthu komanso Dziko.

(2) Aliyense m'banja azilemekezedwa ndi kutetezedwa ku kumulekerera, kumuzunza, kapena kumupsinjiriza.

(3) Amuna ndi akazi onse azikhala ndi ufulu kukwatira kapena kukwatiwa ndi kulowa m'banja.

(4) Palibe munthu uyo adzakakamizidwa kulowa m'banja.

(5) Mfundo (3) ndi (4) zikhudza ukwati wosiyanasiyana, kaya womabgitsa ku Boma, wachinkhoswe, wongolowana kapena wontsuka mapoto malingana kuti anthuwo akhala limodzi panthawi yaitali.

(6) Munthu wobzyola zaka 18 zakubadwa asaletsedwe kulowa m'banja ngati akufuna.

(7) Ukwati wa amene wobzyola zaka 15 zakubadwa koma osafika 18 ululoledwa ngati makolo kapena awalera awuvomereza.

(8) Boma lili ndi udindo woletsa ukwati ngati mmodzi mwa ofuna kulowa m'banjawo ali ndi zaka zakubadwa zochepera 15.

23.

(1) Ana onse alandire chithandizo chofanana pankhani ya malamulo kosawasala chifukwa cha kuti abadwira mchikwati kapena ayi.

(2) Ana onse azikhala ndi dzina ndipo azipatsidwa dzina lawolawo komanso lamakolo ndipo azidziwika kuti ndi nzika kuno kapena kwina.

(3) Ana azidziwa makolo awomndipo azileredwa ndi makolo.

(4) Ana azitetezedwa ku ntchito zonga ngati izi ndi akapolo ndipo lamulo sililola kuwazunza kapena kuwalanga m'jira yomwe:

a) Ingawaononge matupi;

b) Ingawalepheretse maphunziro;

c) Ingawaonongere umoyo kapena kapena kakulidwe ka m'thupi, mu uzimu ndi mu umunthu wawo.

(5) Ana pa ndime iyi akutanthauza anthu osabzola zaka 16 zakubadwa.

24.

(1) Amayi ali ndi ufulu wolandira chitetezo chokwanira mosasankha pamalamulo, ndipo sikuloledwa kuti aziwasala chifukwa choti ndi amayi kaya kuti ali pa banja kapena ayi ndipo ufuluwo utanthauza kuti:

(a) Azilandira ufulu wonga wa amuna malinga ndi malamulo, komanso aziloledwa kuchita kapena kukhala nawo pa:

(i) Kupanga mgwirizano;

(ii) Kupeza ndi kukhala ndi katundu kapena chuma paokha kapena mogwirizana ndi anthu ena kaya ali pabanja kapena ayi;

(iii) Kupeza ndi kusunga ana amene si awo ndiponso kukhala ndi ufulu wonse pamaganizo a momwe angawalerere; ndiponso

(iv) Kupeza ndikukhala ndi mwayi wakuti ndi nzika ya m'Malawi

(b) Pakutha pa ukwati:

i) Katundu wa m'banjamo azigawidwa mokomera onse ndipo;

ii) Azilandira chithandizo choyenera monga mmene zinthu zingakhalire makamaka podziwa kuti bamboo alekana ndi mayiwo ali ndi chuma chotani ndipo chithandizo chofunika ku ana chingakhale chotani.

(2) Lamulo la mtundu uliwonse ilo lingasale chithandizo kwa amayi chifukwa chakuti si amuna  kapena chifukwa choti alibe banja ndi lopanda mphamvu ndipo malamulo adzakhazikitsidwa ochotsa mkhalidwe ndi mchitidwe wosala amayi makamaka m'njira azi:

a) Kuwagwirira chikwati, kuwachitira nkhaza ndi kuwamenya;

b) Kuwasala pa mwayi wa ntchito, bizinesi kapena pa ntchito za boma; ndiponso

c) Kuwalanda chuma chawo, kapena chuma cha masiye chomwe angachipeze.

25.

(1) Anthu onse adzilandira maphunziro

(2) Maphunziro a Pulayimale azikhala osachepera zaka 5 pasukulu

(3) Sukulu izo sizaboma komanso mabungwe amaphunziro apamwamba ziloledwa ngati:

a) Sukuluzo kapena mabungwewo zilowa m'kaundula ku Boma movomerezedwand malamulo;

b) Ngati zonse zochitika m'masukulumo kapena m'mabungwemo sizili pansi pa muyeso umene ukhazikitsidwa pokhudza m'sukulu za boma.

26. Munthu aliyense ali ndi ufulu wogwiritsa ntchito chinenero komanso chikhalidwe cha mtundu monga mwachifuniro chake.

27.

(1) Sikuloledwa kumsunga munthu muukapolo kaya mopsyinjidwa

(2) Ukapolo komanso malonda a ukapolo saloledwa

(3) Sikuloledwa kumugwiritsa ntchito munthu momokakamiza.

(4) Munthu asagwire ntchito imene saifuna mwa ukapolo.

28.

(1) Munthu aliyense ali ndi ufulu wopeza katundu kapena chuma mwa iye yekha kapena mogwirizana ndi ena

(2) Palibe munthu uyo adzamulande chuma chake mwankhaza

29. Munthu aliyense adzikhala ndi ufulu wodzipezera pogwiritsa ntchito ndi manja ake, kugwira ntchito ndi kupeza zofuna pamoyo wake kwina kulikonse m'Malawi muno.

30.

(1) Anthu onse azikhala ndi ufulu wopititsa mtsogolo miyoyo yawo ndipo adzidyerera pa chuma, pa mkhalidwe ndi pa ndale, makamaka amayi, ana ndi onse olumala apatsidwe chithandizo chapadera popititsa mtsogolo ufulu umenewu.

(2) Bomalidzipereke kuti ufulu wopititsa mtsogolo chitukuko uzioneka kuti ulipodi. Ndipo pa mfundo zothandiza pa ntchitoyi pakhalenso kuonetsetsa kuti onse mosakondera ali ndi mwayi wopezera chuma, maphunziro, chithandizo pa umoyo wabwino, chakudya, pogona pabwino, mwayi wokhala pa ntchito, komanso zithandizo zina monga misika, madzi ndi misewu.

(3) Boma lichitepo kanthu pakusintha zinthu kuti ena asatsalire m'mbuyo pothetsa zopelewera pa miyoyo ya anthu.

(4) Boma lili ndi udindo wolemekeza ufulu wa chitukuko ndipo lidziyenereza mfundo zoyendetsera dziko pakuchita chitukuko.

31.

(1) Munthu aliyennse ali ndi ufulu wokhala mwaubwino ndimosamalidwa pa ntchito komanso azilipidwa mtengo woyenera.

(2) Anthu onse ali ndi ufulu kukhazikitsa ndi kukhala membala wa bungwe loteteza mtendere pantchito kapena kusakhala membala ndikukana kupanga bungwe loteteza mtendere pa ntchito.

(3) Munthu aliyense azilandira mtengo woyenera pa ntchito ndiponso molingana ndi mtengo wantchitoyo mosasiyanitsa kapena kusala kwa mtundu uliwonse, makamaka pasakhale kusankha chifukwa chakuti munthuyo ndi mwamuna kapena mkazi, wolumala kapena wakhungu la mtundu wina.

(4) Boma likhazikitse mfundo zolola ufulu wakuti anthu angathe kunyanyala ntchito.

32.

(1) Munthu aliyense ali ndi ufulu wokhala m'bungwe lililonse, zimene zitanthauza kuti alinso ndi ufulu wopanga mabungwe.

(2) Palibe wina akakamize munthu kuti akhale m'bungwe lililonse.

33. Munthu aliyense ali ndi ufulu wokhala ndi maganizo ake , chippembedzo chake ndi chikhulupliro chake, zolingalira komanso nzeru za maphunziro ake.

34. Munthu aliyense ali ndi ufulu woganiza monga mwa kufuna kwake ndipo angathe kusunga zakukhosi kwake osamukakamiza kuti amve izi kapena aganize izi.

35. Munthu aliyense ali ndi ufulu wolankhula izo afuna.

36. Ofalitsa nkhani ali ndi ufulu wotola nkhani ndikuzifalitsa momasuka, muno m'Malawi kapena kunja kwa dziko lino, ndipo adzipatsidwa ufulu onse opeza nkhani kuti athe kugwira ntchito yawo.

37. Pokhapokha ngati lamulo linganenere mwina, aliyense ali ndi ufulu wopeza nkhani iliyonse yosungidwa ndi boma kapena nthambi yake iliyonse ngati nkhaniyo njofunika kuti munthu agwiritse ntchito ufulu wake.

38. Munthu aliyense ali ndiufulu wokumana ndi anzake pagulu ndikuchita nawo chionetsero choti sakukhutitsidwa ndi nkhani iliyonse mogwirizana ndi anzakewo  koma mopanda phokoso ndiponso mosagwiritsa ntchito zida

39.

(1) Munthu aliyense ali ndi ufulu kaya kupita kwina kulikonse ndi kukhala pa malo aliwonse m'Malawi muno.

(2) Munthu aliyense ali ndi ufulu wotuluka kunja kwa Malawi ndikubwererakonso.

40.

(1) Mogwirizana ndi malamulo ano, munthu aliyense ali ndi ufulu;

a) Wokhazikitsa, kulowa ndi kuchita nawo zonse ndiponso kukopa mamembala a chipani cha ndale.

b) Kuchita kampeni m'malo mwa chipani cha ndale kapena pa nkhani ina;

c) Kuchita nawo mwaufulu za ndale kuti kukhale kusintha pa olamula m'boma kapena a mfundo zaboma.

d) Kusankha mwaufulu pankhani zandale

(2) Ngati nkofunika, Boma lizipatula ndalama kuti liwonetsetse kuti panthawi imene apatsidwa n'Nyumba ya Malamulo, chipani chilichose chimene chidapeza gawo limodzi pamagawo khumi anthu onse pa voti yolimbirana mipando ya m'Nyumbayo chikhale ndi ndalama zokwanira kuti agwirire ntchito imene anthu adachisankhira.

(3) Kupatula umo malamulo ano anganenere munthu aliyense azikhala ndi ufulu woponya nawo voti yakudziwa mwini ndikukhala nawo pagulu la anthu oti asankhidwe pa udindo oimira anthu m'Boma.

41.

(1) Munthu aliyense azikhala ndi ufulu woti adziwike ngati munthu woima payekha malinga ndilamulo.

(2) Munthu aliyense ali ndi ufulu odandaila ku bwalo loweruza lililonse kapena ku bungwe lililonse lofufuza ndi kuweruza mlandu kuti nkhani ithe.

(3) Munthu aliyense azilandira chiweruzo mothandiza ndichokwana m'bwalo lamilandu kapena m'bungwe loweruza pakakhala kulakwira ufulu ndi mwayi wonse womwe munthu wapatsidwa ndi Malamulo ena.

42.

(1) Munthu aliyense osungidwa mundende, komanso womangidwa chifukwa cha chiweruzo pa mlandu uliwonse ali ndi ufulu:

a) Woti adziuzidwa mwansanga chifukwa chimene amuikira m'ndende, mchiyankhulo chomwe iye amamva;

b) Aikidwe m'ndende momwe azimusunga monga munthu ndiponso mukhale mwayi wowerenga ndi zolembera, chakudya choyenera komanso chithandizo cha chipatala choperekedwa ndi boma.

c) Akhale ndi mwayi wowonana aliyekha ndi katswiri wa Malamulo wodzisankhira yekha ndipo aziuzidwa mwansanga za mwayi umenewu, komanso ngati chilungamo chikutero, Boma ndilo limupezere katswiri waMalamulo kuti amuthandize.

d) Apatsidwe malo ndi mwayi wokambirana, komanso kuonedwa ndi banja lake, bwenzi lake lapamtima, a chinansi, achibale kapena abusa, ndiponso akuchipatala omuthandiza akadwala amene iye angafune.

e) Kukana kuti sayenera kumangidwa ngati wamangidwa popanda lamulo mwayekha kapena mothandizidwa ndi katswiri wa Malamulo m'bwalo lachiweruzo, ndi

f) Kumasulidwa ngati adamangidwa molakwira lamulo.

(2) Munthu akamangidwa kapena akamuzenga mlandu chifukwa chomunenera kuti walakwira lamulo, pamwamba pa ufulu umene ali nawo, alinso ndi ufulu:

a) Wouzidwa mwachangu m'chinenero chimene akuchidziwa kuti ali ndi ufulu wosayankhula chilichonse ndikudziwa zimene zingachitike ngati asankha kuti ayankhulepo;

b) Kubweretsedwa mwansanga, monga zinthu zingakhale koma pasanapite maola 48, kapena ngati nthawiyi ithe oweruza ataweruka kapena patsiku losaweruza, tsiku loyamba loweruza itatha nthawiyo, kubwalo loweruza losakondera mbaliu iliyonse namuimba mlandu komanso namuuza chifukwa chake akumusunga mu ukaidi, apo ayi ndiye kuti amasulidwe.

c) Asakakamizidwe kuti avomere zolakwa zimene zingagwiritsidwe ngati kutero umboni kumbali yomuimba mlandu,

d) Kupatula pa zifukwa zoyenera asamusunge pamodzi ndi anthu amene analowa kale mu ukaidi ndipo amsunge mosamala chifukwa oweruza sanamupeze ndi mlandu,

e) Kumasulidwa kundende atalipira ndalama zakuti abadikira mlandu kumudzi kapena popanda kuchita izi pokhapokha ngati kutero sikusamala chilungamo ndiponso

f) Ngati munthu woimbidwa mlandu, alandire chiweruzo mwachilungamo, kutanthauza kuti mwa zina:

i) Azengedwe mlandu poyera, ndipo oweruza akhale anthu olungama ndiponso osakondera mbali, pasanapite nthawi yaitali atamuimba mlanduwo;

ii) Auzidwe mokwana kuti tchimo limene akuimbidwa nalo mlandu ndi chani;

iii) Atengedwe ngati munthu wosalakwa malinga kuti mwa malamulo iye simunthu wolakwa ndipo atha kukhala chete osavomera

kapena kuukana mlandu poyankhakapena nthawi ina iliyonse pa mlanduwo ndi kuti atha kungokhala osapereka umboni pa mlanduwo;

iv) Kutulutsa ndi kutsutsa umboni ndipo sayenera kukakamizidwa kuti apereka umboni wompachika iye mwini;

v) Kuthandizidwa pankhaniyo ndi katswiri wamalamulo uyo wafuna iye, ndipo ngati chilungamo chifunike kutero, kulandira chithandizo cha katswiri amene Boma limulipire, ndipo nkofunika kumuuza woimbidwa mlanduyo ufulu wonsewo;

vi) Kusagamulidwa kuti ndiwolakwira lamulo ngati cholakwacho sichinali kulakwira nthawi imene chinachitika kapenasichinachitike ndiponso kusalandira chilango chobzyola muyeso uwo udalipo pa nthawi imene adalakwayo;

vii) Kusazengedwa mlandu kawiri ngati nkhaniyo ndiyomwe idaweluzidwa kale ndikupeza kuti adalakwadi kapena ayi;

viii) Kukhala ndi mwayi wa apilo kuti nkhaniyo akaizengeso kapena kuunika ngati chilungamo chidachitika pamene idaweruzidwa koyamba.

ix) Kuzengedwa mlandu mchinenero icho adachidziwa, apo ayi, kukhala ndi munthu womasulira chilankhulidwecho kuti azimva bwino, koma munthuyo wolipidwa ndi Boma, ndiponso

x) Kugamulidwa nsanga mlanduwo ukazengedwa napezeka kuti walakwadi.

g) Kuonjezera apo, ngati woimbidwa mlandu ndi mwana, kulandira chilango choyenera mwana zimene zitanthauza:

(i) Kusamulamula kuti akhale kundende moyo wake wonse popanda mwayi wotulukako;

(ii) Kuikidwa mundende pokhapokha palibe chilango china, koma ngakhale zitero kwanthawi yaifupi monga kungatheke;

(iii) Kusakhala pamodzi ndi akulu mndende, pokhapokha ngati kutero sikumuthandiza ndiponso kukhala ndi mwayi wokumana ndi makolo m'kalata kapena pomuchezera.

(iv) Kumusunga momuthandiza kuti ulemu ndi umunthu wake usungidwe zimene zimathandizanso kuti iye adzilemekeza ufulu wa anthu ena.

(v) Kusungidwa molemekezanso ubwana wake kuti athandizidwe kuti bwino lake azakhalenso m'modzi pakati pa anthu akwawo nakhala othandiza;

(vi) Kugwira naye ntchito pomuweruza mlandu munjira imene iha kusamala ubwino pamene tikulemekezanso ufulu ndi chilungamo mokwanira ndinso

43. Munthu aliyense ali ndi ufulu:

a) Wolandira chilungamo molondoloza ndondomeko zonse zakachitidwe malingana ndi zifukwa zake ngati paoneka bvuto paufulu wake pa, zomwe amayenera kuyembekeza kapena zofuna kaya zomukhudza ; ndi

b) Kupatsidwa zifukwa mchikalata pazimene ogwira ntchito ya Boma achita ngati kutero kukhuza ufulu wake, mwayi uli wonse, kaya ngati zikudziwika.

44.

(1) Sikuloledwa kuchotsera kapena kuchepetsa kapena kusintha:

a) Ufulu woti munthu azikhala ndi moyo

b) Kuletsa chilango chozunza, chankhaza, chodzera nkunyoza;

c) Kuletsa kupha wanthu mwachisawawa;

d) Kuletsa ukapolo, malonda a ukapolo komanso mchitidwe wofanana ndi ukapolo;

e) Kuletsa kumangidwa ndi kuikidwa m'ndende chifukwa choti munthu waphwanya pangano chabe.

f) Kuletsa zomuimba munthu mlandu chifukwa cha kuchimwira lamulo ilo lidaali lisanapangidwe nthawi imene adalakwayo kapena kumulanga kubzola muyeso umene unali nthawi imene ankalakwayo ndi

g) Ufulu wodzisungira zamu mtima, chikhulupiliro chake, maganizo, chipembedzo ndiponso nzeru zamaphunziro ake.

(1) Ufulu wotulutsidwa kuti mwa thupi aonekele pa maso pa bwalo la chiweruzo osamangosungidwa m'ndende.

(2) Kuchotsera zili pa ndime yoyamba (1) sikuloledwa kuletsa za ufulu ndi mwayi umene Malamulo ano akupereka pokhapo lamulo litero, ngati kuteloko sinkhaza ndipo kuloledwa ndi Malamulo a mayiko onse ra nkhani ya ufulu wa anthu kuti ndipo ngofunika m'dziko lopanda m'chitidwe wobisala ndi m'boma lomvera za anthu

(3) Malamulo okhazikitsa zoletsa kapena kuimitsa nkhani ya ufuluukutchulidwawo, koma angokhala opaza.

(4) Ndikutheka kumulanda chuma munthu ngati pangakhale chifukwa chothandiza anthu komanso ngati mwiniyo amuuza kwa nthawi yokwana ndipo walipidwa mokwanira, koma wolandidwayoali ndi ufulu wokwana nkhaniyo kubwalo loweruza.

(5) Ngati malamulo ano agamula kuti munthu ali ndi ufulu kuthandizidwa ndi katswiri wa Malamulo kapena wachipatala wodzisankhira iye mwini, ufulu umenewu wofuna katswiriyo sudzachepetsedwa kupatula pamene kukuloledwa kuti Nyumba ya Malamulo inganene kuti wosankhidwayo angokhala katswiri amene adalembedwa ntchito ndi Boma.

45.

(1) Sikudzatheka kuchotsera ufulu wotchukidwa pa mutu uno pokhapokha ngati kuteroko kungaloredwe ndi ndime ino ndipo kuchotserako kusachitike pokhapo kwaikidwa lamulo lamphamvu motsata ndime ino.

(2) Pulezidenti angathe kuikitsa ulamuliro wamphamvu:

a) Motsata ndime ino kusaonjezera;

b) Pokhapokha ngati waloledwa ndi komiti yokhazikitsidwa ndi Nyumba ya Malamulo kuti aziyang'anira chitetezo.

c) M'nthawi ya nkhondo yokha, kapena pamena pali kuoneka kuti nkhondo kapena kumenyana pakati pamitundu kungchitike kapena ngati pagwa ngozi yaikulu;

d) Mongokhudza kumbali yokhayo kumene kwaoneka mabvuto, komanso alengeze kuti kumeneko kwakhazikitsidwa ulamuliro wamphamvu; ndipo

e) Atalengeza kuti kwakhazikitsidwaulamuliro wamphamvu.

(3) Kuchotsera kungaloledwa pa nthawi imene kuli ulamuliro wamphamvuwo:

a) Kumbali ya ufulu wolangula, ufulu wouzidwa zimene zachitika, ufulu woyenda, ufulu wosonkhana ndi ufulu umene ukupezeka pa ndime 19(6)(a) komansopa ndime 42(2)(b);

b) Pokhapokha ngati kuchotserako sikuli kutsutsana ndi udindo umene dziko la Malawi lili nawo pa Malamulo obvomerezedwa ndi maiko ena onse; ndipo;

c) Kufikira kuti:

(i) Ngati pali nkhondo kapena kuti kubwera nkhondo, nkofunika kuonetsetsa kuti miyoyo ya gulu la asilikali amene akumenyana nkhondo moteteza dziko ndi zolinga za nkhondo zitetezedwe; kapena

(ii) Ngati kuli ngozi yokhudza anthu kapena Madera ambiri, ndipo nkofunika kuti anthu ali pangozi m'deralo atetezedwe.

(4) Ulamuliro wamphamvu wolengezedwa ndiponso chilichonse chochitika pokhudza ichizikhalepo kwanthawi yosapitilira masiku 21 pokhapokha ngati kwaloledwa kutalikitsa nthawiyo kosabzolera miyezi itatu pa nthawi pa nthawi imodzi atamanga mfundo m'Nyumba ya Malamulo yomwe yabvomerezedwa ndi aphungu osachepa 2/3 a m'Nyumbayo.

(5) Bwalo lalikulu la milandu (High Court) lili ndi mphamvu yolandira ndi kugamula pa nkhani yotsutsa kuti ulamuliro wa mphamvuzo siwoyenera kukhazikitsidwa kaya kutsutsa kuti sikoyenera kuchita chilichonse pansi pa ulamulirowo.

(6) Ngati munthu wamangidwa chifukwa cha ulamuliro wamphamvu kumangidwako kungatheke ngati:

a) M'modzi wamkulu wa m'banja laomangidwayo kapena mzake, auzidwe zakumangidwako msanga pasanapite maola 48 kaya zivute bwanji.

b) Dzina la aliyense la omangidwayo ndiponso mfundo zomumangirazo azirengeze mu GAZETI yaboma asanathe masiku asanu kuchokera nthawi imene adamangidwayo.

c) Ufulu umene unakhazikitsidwa mu ndime 19(6)(a) kapena ndime 42(2)(b) ukachotsedwa:

(i) Oweruza aunike za kumangidwakwa munthuyo mwansanga ndikuona ngati n'loyenera pasanapite masiku khumi kuchokera nthawi yom'mangayo ndipo bwalo loweruzayo ligamule kuti womangidwayo amasulidwe ngati likukhutira kuti kuchita choncho n'kofunika kuti bata ndi mtendere zibwerere m'malo;

(ii) Womangidwa ali ndi ufulu wopemphaa chiweruzo kuti azengeso mlandu wake ndipo a chiweruzowo agamule kuti amtulutse ku ndende ngati akukhutira kuti kumangidwako sikofunikando pankhani yosungitsa bata ndi mtendere, ndipo oweruza angafunsidwe kutero nthawi iliyonse pakatha masiku asanu mlanduwo atauunika malinga ndi ndime (i)

d) Pofunika kutsimikizira ngati nkofunikadi kuti munthu akhale muukaidi chifukwa cha nkhani yomwe ili pa ndime (c) Boma lipereke zifukwa zolembedwa kufotokoza chifukwa chimene munthuyo apitilire kukhala m'ndende ndipo ampatse woimbidwa mlanduyo zifukwazo pasanapite masiku awiri mlanduwo usanalowenso m'bwalo lamilandu.

(7) Ngati oweruza apeza kuti zifukwa zomusungira munthuyo m'ndende sizokwana kapena kuti sizogwirizana ndi malamulo, bwalolo ligamule kuti munthuyo amasulidwe ndipo sayenera kumangidwanso pa nkhani yomweyo pokhapokha Boma lipereke chifukwa chokwanira asanamumangenso.

(8) Kaya zivute zitani, sukutheka kuthetsa mphamvu yamalamulo ano kapena gawo lake, kapena nthambi iliyonse pokhapokha ngati kwaloledwa ndi Malamulo ano.

46.

(1) Pokhapokha ngati kungaloledwe kutero ndi Malamulo ano, Nyumba ya Malamulo kapena ena wololedwa kupanga lamulo saloledwa kupanga lamulo lililonse ndiponso Gawo la mutu wa Boma lisachite chirichonse chothetsa kapena kuchepetsa ufulu ndi mwayi wokhazikika ndi mutu uno, ndipo lamulo lililonse kaya chirichonse icho chidzatsutsana ndi izi sichidzakhala ndi mphamvu kumbali yotsutsanayo.

(2) Munthu aliyense amene aona kuti ufulu ndi mwayi umene wakhazikitsidwa ndi Malamulo ano waswedwa kapena waopsyezedwa adzakhala ndi ufulu:

a) Kupempha oweruza kuti agamule kuti ufuluwo ugwire ntchito kapena kuti utetezedwa;

b) Kupempha Mkulu womva madandaulo (Ombudzimani) kapena Bungwe loona ufulu (Human Rights Commission) kuti amuthandize umo angathele.

(3) Ngati bwalo la milandu latchulidwa pa ndime 2(a) liona kuti ufulu umene Malamulo ano akunena aphwanyidwa kapena sanatsatidwe, bwalolo liri ndi mphamvu kugamula monga kungafunike kuti ufuluwo ugwile ntchito, ndipo ngati bwalo lipeza kuti mwina ufuluwo uphwanyidwa bwalolo lidzakhala ndi mphamvu kugamula muli monse kuti mwina asaphwanye ndondomeko ya ufuluwo.

(4) Bwalo la milandu limene latchulidwa pa ndime 2(a) liri ndi mphamvu kugamula kuti munthu amene amulakwilayo amulipire ngati bwalolo liganiza kuti nkoyenera kutero malinga ndi umo nkhaniyo ingakhalire.
(5) Malamulo apangidwe ndikukhazikitsa kuti wophwanya ali pa ndime 44(1) amene saloledwa kuwaphwanyidwa, alangidwe.

# MUTU V
# ZOKHUDZA NZIKA

47.

(1) Munthu aliyense amene ali nzika lisanafike tsiku lakuti malamulo ano akhazikitsidwe malinga ndi lamulo, ameneyo apitilire kukhala nzuka ya mono m'Malawi.

(2) Lamulo litha kukhazikitsa ndondomeko ya umo munthu angakhalire kapena kutayira unzika wa Malawi wa aliyense kuchokera pa 18 Meyi 1994 koma unzikawu usamanidwe kwa munthu popanda chifukwa chokwanira.

*(3) Malinga ndi ndime ino, tikati:*

(a) "*Kulandira unzika*" tikukhudzanso mbadwa ya dzikolo, amene ali nzika chifukwa cha makolo, ukwati, kulembetsa, kungopatsidwa komanso chifukwa cha njira ina iliyonse yololedwa ndi lamulo loikidwa ndi Nyumba ya Malamulo, ndipo

(b) "*Kutaya Unzika*" kutanthauza kulandidwa, kuuvula unzika mwawekha kapena mwanjira ina iliyonse yoikidwa ndi lamulo la Nyumba ya Malamulo.

# MUTU VI
# GAWO LA BOMA LOPANGA MALAMULO

48.

(1) Mphamvu yonse yopanga malamulo a Boma idzakhala m'manja mwa Nyumba ya Malamulo imene idzakhale ndi mphamvu komanso udindo umene wafotokozedwa mu Malamulo ano.

(2) Lamulo lopangidwa ndi Nyumba ya Malamulo lidzapambana malamulo ena onse koma lili pansi pa Malamulo ano.

(3) Mfundo iliyonse imene idzapita ku Nyumba ya malamulo kapena ku Seneti kutiigamule, idzagamulidwa pa voti ndipo mamembala ochuluka pa mamembala amene ali mnyumbayo ndipo aloledwa kuvota ndiwo agamule, pokhapokha Malamulo ano kapena Malamulo ena anenera mwina.

49.

(1) Tikati "Nyumba ya Malamulo" mu malamulo ano, pokhapokha pali kutanthauzira kwina tikunena Nyumba ya Malamulo ya Phungu, Seneti ndi Pulezidenti ngati mutu wa Boma.

(2) Pokhapokha ngati Malamulo ano anenera mwina, lamulo litanthauza Bilo yomwe:

(i) Yalowa m'Nyumbayo ndipo yabvomerezedwa ndi anthu ochuluka m'Nyumba ya Malamulo;

(ii) Yalowa m'Nyumba ya Seneti ndikubvomerezedwa ndi mamembala ambiri mu Seneti;

(iii) Ndikubvomerezedwa ndi Pulezidenti motsata zolembedwam'Mutu uno.

(3) "Tchemba" itanthauza Nyumba ya Malamulo kapena Seneti.

50.

(1) Kuti Tchemba iyambe kukambirana payenera kupezeka poyamba za zonse zochitika 2/3 ya mamembala a tchembayo amene aloledwa kuwerengedwa nawo pavoti koma osaphatikizapo Sipikala kapena amene wagwilizila pa mpando m'Nyumbayo.

(2) Ngati Sipikala kapena mkhalapampando wauzidwa ndi nthumwi m'Tchemba kuti mamembala sakukwanira kuti ayambe ntchito yawo malinga ndi Malamulo oyendetsa zinthu m'Tchembamo ndipo papita mphindi malinga ndi malamulo a Tchembawo Sipikala kapena mkhalapampando ayimitse zokambirana akatsimikiza kuti nthumwi sizikukwanirabe malinga ndi malamulo.

51.

(1) Palibe munthu angasankhidwe kukhala m'Nyumba ya Malamulo pokhapokha iyeyo:

a) Ndi nzika ya muno amene anali atakwanitsa panthawi ankamutchula;

(i) Zaka 21 zakubadwa ngati ndi m'Nyumba ya Malamulo, kapena

(ii) Zaka 35 zakubadwa ngati ndi mu Seneti;

b) Atha kulankhula ndi kuwerenga chingerezi moti moti angathe kuchita nawo zonse m'Nyumba ya Malamulo; ndipo

c) Ali mkaundula wa voti mdera la phungu

(2) Ngakhale ndime (1) ikutero, munthu saloledwa kusankhidwa kuti apite ku Nyumba ya Malamulo kapena kukhala phungu ngati:

a) Ndi nzika ya dziko lina;

b) Kapena adapezeka kuti ndiwozungulira muti malinga ndi malamulo a dziko la Malawi;

c) Adapezeka ndi oweruza kuti ali ndi mlandu wolakwira Boma wokhudzana ndi kusakhulupilika kapena opanda mkhalidwe wa umunthu;

d) Akadali pa bankalapu atagamulidwa kuti wolowa bankalapu malingana ndi lamulo lomwe likugwiritsa ntchito mu Boma.

e) Ali pa mpando wa Boma kapena akugwirizira,pokhapokha Malamulo ano akunena kuti munthuyo saletsedwa kuima nawo pachisankho chifukwa choti ali pampando umenewo kapena ngati atula pansi mpandowo kuti aime nawo pa masankhowo;

f) Ndi m'modzi mwa,ndipo akugwira ntchito ya usilikali wa nkhondo kapena wa Polisi ya m'Malawi; ndiposo

g) Adapezeka ndi oweruzakuti adalakwira lamulo lokhudza chisankho cha Pulezidenti, kapena cha mamembala a ku Nyumba ya Malamulo.

52. Munthu aliyense wogwira ntchito ku Nyumba ya Malamulo kapena membala wa Nyumbayo asanakhale pampando wake m'Nyumbayo kapena asanayambe ntchito yake azilumbira pa maso pawamkulu wa oweruza (Chief Justice) m'Tchembamo:

a) Kuti ndiwogonjera ndipop atero monga lamulo lifunira, ndipo

b) Alumbirenso monga malamulo afunirakuti adzagwira ntchito pampando wake bwino.

53.

(1) Pazikhala Sipikala wa Nyumba ya Malamulo komanso wa Seneti. Iye adzasankhidwa pa voti n'Tchemba m'mene amakhala pamene Tchembayo ikakumananso pakakhala kuti adaimitsa.

(2) Mamembala a Tchemba ili yonse asankheso munthu m'modzi kapena angapo kuti akhale wachiwiri kwa Sipikala nthumwizo zikangokumana koyamba pakapita chisankho chokhudza Nyumba ya Malamulo kapena nthawi iliyonse pakakhala popanda wachiwiri kwa Sipikala.

(3) Mpando wa Sipikala udzakhala wopanda munthu;

a) Ngati Sipikala amwalira kapena kutula pansi udindo;

b) Ngati Sipikala aleka kukhala membala wa m'Tchemba m'mene amakhala;

c) Ngati Sipikala akhala Pulezidenti, Nduna kapena Nduna yaing'ono, kapena membala wa Seneti; kapena

d) Ngti Tchemba m'mene amakhala lamanga mfundo kuti Sipikala achoke, koma izi zingatheke pokhapokha mfundoyo yavomerezedwa ndi mavoti osachepera 2/3 ya mamembala onse a m'Tchembayo. Koma ngakhale zitero Sipikala ali ndi ufulu wokamba pa mfundo yokhudzana ndi zoti achoke m'Tchembamo ngati afuna.

(4) Sipikala wa Tchemba iliyonse kapena wachiwiri wake amene adalozedwa ngati iye palibe, ndiye azikhala pa mpando m'Tchembamo pa zokambirana zonse. Koma ngati Sipikala kapena wachiwiri wake palibe Tchemba litha kusankha m'modzi mwa membala akhale ngati Sipikala kwa nthawi akukumanayo.

(5) Munthu aliyense wosankhidwa kukhala Sipikala kaya wogwirizira udindo azigwira ntchito yake ndikuyang'anira udindo payekha popanda kugwedezedwa ndi munthu wina kapena mpando wina koma alondoloze chifuniro cha m'Tchembamo motsata malamulo.

(6) Angakhale kuti Sipikala kaya wongogwirizira mpando wa Sipikala wasankhidwa ngati nthumwi ya chipani cha ndale kukhala m'Tchembamo asalamulidwe kapena kukhala pansi pa mwambo, mphanvu kapena kutsogozedwa ndi chipanicho kapena chipani cha ndale china pamene akugwira ntchito ndikukhala paudindo kapena kugwiritsa ntchito mpandowo.

(7) Ngati pali nkhani yokhudza dera limene amaimila m'Tchembamo ndipo nkhaniyo siyikukhudza zina, Sipikala ali ndi ufulu ochokapo pa mpando pa kanthawi ndi kulankhulapo ngati nthumwi yoimira anthu ngakhalenso kuchita nawo voti ngati pali kugawanikana pa nkhaniyo.

54.

(1) Kupatula zimene zalembedwa pa ndime 53(7) Sipikala asachite nawo voti m'Tchemba koma ngati ma voti ngofanana pa nkhani iliyonse iye atha kugamula nkhaniyo ndi voti yake.

(2) Membala aliyense wa m'Nyumba ya Malamulo kapena Seneti, kupatula Sipikala kapena wachiwiri wake, ali ndi ufulu kuchita nawo voti kuyambankuyamba pa nkhaniyo ngati nthumwi pamene akuongolera zochitika m'Tchembamo ngofanana.

55. Padzakhala Mlembi wa Nyumba ya Malamulo ndiponso Mlembi wa Seneti amene ndi ogwira ntchito Boma; iwowa azithandiza Sipikala wa Nyumba ya m'mene aikidwa ndi kugwira ntchito zonse komanso azikhala ndi udindo wonse monga Sipikala anganenere.

56.

(1) Motsata malamulo ano nyumba ya Malamulo ndi Seneti atha kupanga lamulo lolongosola machitidwe a zonse m'Nyumbayo.

(2) Kupatula umo anenera m'Malamulo ano, Nyumba ya Malamulo ndi Seneti zitha kugwira ntchito yawo koma sangatero mipando yobzyola 2/3 ilibe anthu.

(3) Ngakhale papezeka kuti anthu ena amene sanayenera kukhala nawo m'Tchembamo achita nawo zonse, zochitikazo sizidzakhala zopanda mphamvu chifikwa cha anthu apaderawo.

(4) Tchemba iliyonse izilola atolankhani ndi anthu wamba kukhalapo pa zokambirana kuti anthu azidziwa zomwe zikukambidwa pokhapokha ngati pali mfundo yosawalola yabvomerezedwa ndipo zifukwa zake ndi zoyenela.

(5) Zokambirana m'Nyumba ya Malamulo zizichitika m'chingerezi ndiponso mziyankhulo izo Tchemba lingakonze kuti lizigwira ntchito mzokambirana zao m'Tchembamo.

(6) Bwalo la malamulo litha kukhazikitsa makomiti a membala kapena makomiti wokhudza ma tchemba onse kuti azisanthula malamulo ndikugwira ntchito zonse koma osati kuti azichita voti pa mfundo ndi pa Bilo.

(7) Kuonjezera pa komiti zokhazikitsidwa pa ndime (6), padzikhalanso komiti yoona alembedwa ntchito za Boma (*Public Appointments Committee*) ndiponso komiti yoona za malamulo m'Nyumba ya Malamulo zimene:

a) Zizisankhidwa ndi Nyumba ya Malamulo moyelekeza ndi umo chiwerengero cha nthumwi za zipani zonse chilili m'Nyumbayo;

b) Komiti zisankhidwa pasanapite masiku 30 pamene Nyumba ya Malamulo ikukumana koyamba chitangotha chisankho cha aphungu ndiponso pakatha chaka choyamba cha Nyumbayo.

c) Komitizi zidzagwira ntchito zimene Malamulo ena anganene kuti zigwire.

57.

(1) Ngati nduna ya za Chuma siidapereke langizo m'chikalata Nyumba ya Malamulo:

a) Isagwepo pa Bilo kapena pankhani yosintha Bilo imene wapampando m'Nyumbayo akuona kuti lili ndi ntchito iyi:

(i) Kukhazikitsa kapena kusintha msonkho;

(ii) Kutapa ndalama kuchokera ku thumba lapadera lotchedwa "Consolidated Fund" kapena kusintha katapidwe ka ndalamazo.

(iii) Kulipira kapena kutulutsa ku thumba lapaderalo ndalama zili zonse pomwe palibe dongosolonso loti azitape, kapena kuonjeza ndalama zolipilirazo kaya kutulutsa, kapena kuti

(iv) Alipire ngongole ya Boma.

b) Isakambirane mfundo kapena kusintha mfondo imene m'maganizo a wapampandoyo ikukhudza zimene  zimene zatchulidwa pandime (a); kapena

c) Kulandira pempho limene wapampando akuona kuti litha kugwira ntchito zotchulidwazi.

(2) Seneti ilibe mphamvu zokambirana kapena kuchita voti pa  mfundo kapena kugwapo pa Bilo imene ikukhudzidwa ndi ndime ino, pokhapokha Nduna yoona za Chuma yabvomereza mchikalata, koma ngakhale zitero sikuloledwa kusintha kapena kuikana mfundo  kapena Biloyo.

58.

(1) Nyumba ya Malamulo itha kupatsira gawo la mutu wa Boma kapena oweruza mphamvu yoti apange malamulo mogwirizana ndi motsata m'mene zonse zimayendera m'Nyumbayo.

(2) Ngakhale ndime (1) ikunena, nyumba ya Malamulo ilibe mphamvu yopatsa ena kuti apange malamulo amene angaphwanye ufulu ndi mwayi umene malamulo ano awapereka

59.

(1) Nyumba ya Malamulo ndi Seneti izikumanirana kumalo komanso panthawi imene Sipikala atakambirana ndi Pulezidenti angatchule; ndipo Tchembalo likayamba ntchito yake lizikumana pa nthawi ndiponso pa masiku amene Tchembalo lagamula: koma

(a) Pulezidenti atakambirana ndi Sipikala wa Tchembalo atha kuitana Nyumba ya Malamulo kapena Seneti kuti ikumane pakakhala chinthu chodzidzimutsa;

(b) Pulezidenti atakambirana ndi Sipikala wa m'Tchembamo, angathe kuimitsa Nyumba ya Malamulo kapena Seneti.

(2) Nyumba ya Malamulo ndi Seneti udzakumana kosachepera kawiri pa chaka.

60.

(1) Sikuloledwa kuti Sipikala, wachiwiri wake, Membala wa Nyumba ya Malamulo komanso Membala wa Seneti amangidwe ali pa ulendo wopita kapena wochokera ku Nyumba ya Malamulo kapena Seneti kapena ali pafupi ndi Nyumbayo pokhapokha ali ndi mlandu woukira Boma ndipo asakhudzidwe kapena kutengedwa kubwalo loweruza kapena ku chiweruzo chili chonse kupatula Nyumba ya Malamulo chifukwa cha zimene walankhulapa nkhani za m'Nyumba ya Malamulo kapena Seneti.

(2) Sikuloledwa kugwiritsa ntchito malipoti ndi zolembedwa kukhudza Nyumba ya Malamulo kapena zokambirana m'menemo kapena m'komiti ya Nyumbayo ndipo zolankhula m'Nyumba ya Malamulo kapena m'komiti zikhudzana ndi kutetezedwa kwathunthu.

(3) Nyumba ya Malamulo ndi Seneti paokha ali ndi mphamvu yolondola mkhani iliyonse komanso kumuitana munthu kaya wogwira ntchito ya Boma aliyense yemwe angafunike kuti adzapereke umboni ndi cholinga chakuti padziwike ngati ntchito za Tchembalo zili kugwilika mwachilungamo.

61.

(1) Ngati phungu wa Nyumba ya malamulo akukhudzidwa pa nkhani zomwe ikukambirana Tchemba yomwe iye ndi Phungu:

a) Aziulula ku Tchembalo kuti akukhuzidwa; ndipo

b) Saloledwa kuchita nawo voti popanda chilolezo cha tchembalo.

(2) Ngati phungu wa Nyumba ya Malamulo alephera kuulula kuti akukhuzidwa pa nkhani malinga ndi ndime (1) Phunguyo walakwa ndipo akuchitira mwano Tchembalo.

62.

(1) Nyumba ya Malamulo idzakhala ndi mipando yoimira magawo m'Malawi omwe Bungwe loyendetsera chisankho likakonze.

(2) Gawo lililonse lidzisankha munthu, motsata Malamulo ano kapena lamulo, kuti adziriimira ngati nthumwi ya Nyumba ya malamulo monga m'mene malamulo ano kapena lamulo lingakonze.

63.

(1) Mpando wa Phungu wa Nyumba ya malamulo udzakhala wopanda munthu:

a) Ngati Nyumba ya Malamulo aithetsa;

b) Ngati Phunguyo amwalira kapena atula pansi mpando wake;

c) Ngati Phunguyo aleka kukhala nzika ya Malawi;

d) Ngati Phunguyo akhala Pulezidenti kapena wachiwiri kwa pulezidenti kapena wasankhidwa kukhala membala wa Seneti;

e) Ngati paoneka zina zakuti akadapanda kukhala membala wa Nyumba ya Malamulo ndiye kuti sakadakhoza kusankhidwa malinga ndi malamulo ano kapena lamulo lili lonse.

f) Ngati Nyumba ya malamulo agamula kuti mpando wa Phunguyo ulibe munthu potsata malamulo oyendetsera zinthu m'Nyumbayo kapena agamula kuti achoke pachifukwa chokwanira motsata chilungamo chenicheni ndiponso;

g) Ngati Phunguyo wabwezedwa ndi anthu mchigawo chake monga momwe anenera malamulo ano kapena lamulo lina lililonse.

(2) Sipikala wa Nyumba ya Malamulo alengeze mu Gazette ngati mpando wa phungu wakhala wopanda munthu malinga ndi ndime ino komabe:

a) Nyumba ya Malamulo ikonze ndondo meko zoti pakhalenso chisankho chapadera kuti mpandowo usangokhala;

b) Chisankho chapadera chizichitika mofulumira ndithu malinga ndi m'mene ziliri zinthu koma pasanapite nasiku 60 mpandowo ulibe munthu;

c) Munthu amene asankhidwa pa chisankho chapadera adzagwira ntcito mpaka mpandowo udzakhalenso wopanda munthu malinga ndi ndime (1)

(3) Ngati Nyumba ya Malamulo imanga mfundo yotero, Sipikala angathe kuchedwetsa zolengeza kuti mpando ulibe munthu kwa nthawi motsata mfundoyo kuti membala akhale ndi mwayi wochita apilo ku bwalo la milandu kapena kwina kuli konse kumene kuli mphamvu yoti abweze zoti phunguyo achoke pa mpando.

64.

65.

(1) Sipikala alamule kuti mpando ulibe munthu ngati membala amene pachisankho anali wa chipani chandale choti chili ndi mpando m'Nyumbayo kupatula phungu yekhayo ndipo mwachifuniro chake wasiya kukhala membala wa chipanicho ndikulowa mchipani china chomwe chili ndi nthumwi m'Nyumba ya malamulo.

(2) Ngakhale ndime (1) ikutero, mamembala a chipani cha ndale ali ndi ufulu wonse pa voti pa nkhani iliyonse m'nyumbayo ndipo sikutheka kugamula kuti mpando ulibe munthu pa chifukwa chokhacho choti pa voti yake phungu watsutsana ndi m'mene chipani chake chimafunira.

66.

(1) Nyumba ya malamulo ndi Tchenba yosankhidwa ndi anthu eni kuti izipanga malamulo ndipo ili idzakhalandi mphamvu pansi pa malamulo ano.

a) Kulandira, kuchotsera, kubvomereza kapena kukana ma Bilo a Boma kapena ma bilo ena;

b) Kulowetsa ma Bilo a anthu wamba ngati phungu wina wayambitsa, komanso kusinthapo, kutsutsa kapena kubvomereza;

c) Kukambako ndi kuchita voti pa mfundo zokhudza nkhani iliyonse kuphatikiza mfundo yozenga mlandu ndi kufuna kumanga Pulezidenti kapena wachiwiri wake;

d) Kulandira, kukonza kapena kubvomereza, ngakhale kukana, maBilo ochokera ku Seneti;

e) Kugwira ntchito ina iliyonse ndi kugwiritsa ntchito mphamvu zonse zimene Malamulo ano azipereka; ndiponso

f) Kuchita zonse zofunika ndizoyenera kuti ntchito iyende bwino.

(2) Pogwiritsa ntchito malamulo ano;

a) Bilo ya Boma ndi Bilo yomwe Boma lakonza ndi kupereka m'Nyumba ya malamulo motumikira Boma;

b) Bilo wamba itanthauza:

(i) Kuti yabwera ndi munthu kapena gulu kapena nthambi imene si ya Boma; ndipo

(ii) Yadza m'Nyumba ya Malamulo mothandiza kapena kuimira gululo ngati nthambiyo idapatsidwa mphamvu ndi ndi lamulo.

c) Bilo ya Membala wamba

(i) Idzatulidwa m'Nyumna ya Malamulo ndi Phungu wa ku Nyumba ya Malamulo; ndipo

(ii) Membala wa m'menemo motsatira dongosolo la kachitidwe ka zinthu m'Tchembamo ndiye adzafotokozere za Biloyo

67.

(1) Nyumba ya Malamulo idzigwira ntchito yake zaka zisanu kuchokera pa tsiku limene inalumbitsidwa mkoma kuchokera apo idzaima.

(2) Nyumba ya malamulo ikatha, chisankho cha mamembala a Nyumbayo chizichitika pasanathe masiku 60 kuchokera patsikulo ndipo tsiku lokumananso a phungu lidzatchulidwa ndi Pulezidenti kuti likhale pasanathe masiku 45 kuchokera patsiku lomwe bungwe loyendetsa chisankho lasankha kuti ndipamene voti idzachitike, ndipo ngati pakhala masiku angapo achitira voti tsikulo likhale mkati mwa masiku 45 kuchokera pa tsiku lotsiriza voti.

68.

(1) Seneti idzakhala ndi mamembala 80 motere:

a) Seneta m’modzi kuchokera m’boma lililonse yemwe dzina lake liri mkaundula wa voti, wosankhidwa ndi khonsolo ya Boma m’bomalo oa voti ya chinsinsi pasanapite masiku 30 chikatha chisankho cha makhonsolo.

b) Seneta m’modzi kuchokera m’boma lililonse yemwe ndi mfumu ya mpando ngati dzina lake lili mkaundulawa voti m’bomamo ndipo wasankhidwa mwachinsinsi ndi wupu wa mafumu onse a m’bomalo pasanapite masiku 30 chikatha chisankho cha makhonsolo;

c) Ma Seneta 32 ena amene adzasankhidwa ndi gulu la anthu osachepera 2/3 ya anthu amene ali kale m’Seneti molozedwa atalandira maina kuchokera ku komiti yotchula maina yomwe yaikidwa ndi ndime (2) koma anthu ake ochokera ku mbali izi:

(i) Anthu ochokera m’magulu oimira mabungwe a mayi, a olumala, a zachipatala, a maphunziro, a ulimi, ndi ogwira ntchito za bizinesi ndiponso a mabungwe a anthu ogwira ntchito za malonda;

(ii) Anthu oimira anzao komwe amkhala, anthu omwe ndi otchuka chifukwa cha kudzipereka kwawo ku anthu kapena chifukwa cha ntchito zao potukula miyoyo, chikhalidwe komanso ntchito za luso losiyanasiyana mdziko muno;ndiponso

(iii) A chipembedzo, amene achokera ku mabungwe azipembedzo zotchuka m’Malawi muno.

(2) Padzakhala komiti yotchula mainaya Seneti imene idzakhazikitsidwe pasanapite masiku 45 chikangotha chisankho cha makhonsolo yomwe ntchito yake ndikupereka maina a anthu amene ndime 1 (c) akuwatchula. Mukomitiyo mudzakhala Sipikala wa Nyumba ya Malamulo, Ombudzimani ndi mamembala 7, omwe ndi ma Seneta ochita kusankhidwa malinga bdi ndime 1 (a) kapena 1 (b) wolozedwa ndi Nyumba ya Malamulo pa mfundo yoperekedwa ndi Sipikala m’Nyumbayo.

(3) Seneta atha kusankhidwa kapena kulozedwa kangapo pokhapokha ngati sangaloledwe kukhala Seneta pa zifukwa zina kapena wachotsedwa.

(4) Komiti yotchula maina aziyesetsa poganizira maina kuti mu Seneti mukhale anthuoimira magulu osiyanasiyana moyerekeza ndi kuchuluka kwao pakati pa a Malawi potero tsono ayesetse malinga ndi umo zingakhalire kuti theka la ma membala a Seneti ndi amai.

69.

(1) Mpando wa Seneta udzakhala wopanda munthu:

a) Ngati Seneti aithetsa

b) Ngati membala amwalira kapena asiya mpando wake;

c) Ngati membala asiya kukhala nzika ya Boma;

d) Ngati membala akhala pulezidenti,wachiwiri wa Pulezidenti, Nduna kapena Nduna yaing'ono kapena ngati akhala Phungu wa Nyumba ya Malamulo;

e) Ngati pataoneka zina ndi kuti munthu si membala wa Seneti kapena kuti sayenera kulozedwa kapena kusankhidwa Seneta malinga ndi Malamulo ano kapena lamulo lina lililonse.

f) Ngati Seneta igamula kuti mpando wa Senetawo ulibe munthum potsata malamulo akagwiritsidwe ka ntchito mu Senetimo kapena igamula kuti achoke pachifukwa chokwanira koma motsata chilungamo chenicheni.

(2) Sipikala wa Seneti alengeze ku Bungwe loona za chisankho mu Gazette pa nthawi yoti mpando wa Seneta ukhala wopanda munthu malinga ndi ndime ino.

(3) Ngati mpando wa membala wa Seneti wakhala wopanda munthu maliga ndi ndime ino:

a) Ngati membalayo anasankhidwa ndi Khonsolo ya Boma a Bungwe loona chisankho adziwitse Khonsolo ya m'Boma limene lidasankha membalayo kutialengeze kuti pakhala chisankho pasanapite masiku 30 mpandowu uli wopanda munthu;

b) Ngati membalayo adasankhidwa ndi mafumu, Sipikala wa Seneti adziwitse Mafumuwo m'boma limene kudasankhidwa membalayo kuti asonkhanitse gulu lamafumulo kuti asankhe membala wina;

c) Ngati membalayo amayimilira gulu lina, Sipikala wa Seneti aitanitse komiti yotchula maina imene ipereke maina amene angasankhepo Seneta.

70. Seneti idzakhala ya anthu olozedwa ndi cholinga chakuti izingokambirana, zokambirana zimene zidzakhala ndi mphamvu pansi pa malamulo;

a) Kulandira,kuunika ndikusintha ma Bilo wochokera ku Nyumba ya Malamulo;

b) Kuchita voti pa mfundo zofunika kuti azitsimikize kapena kutumiza ma Bilo amene Nyumba ya malamulo yabvomereza;

c) Kuikapo maganizo awo pa nkhani iliyonse, mwa iwo wokha kutulutsa Bilo ya munthu wamba ndikuchita voti pa mfundo yokhudza nkhani iliyonse kuphatikizapo mfundo yoti amuimbe mlandu kapena kumulanga Pulezidenti kapena wachiwiri wake;

d) Kugwira ntchito ina iliyonse ndi kugwiritsa ntchito mphamvu zonse zimene Malamulo ano azipereka;

e) Kugwira ntchito zina zonse akapemphedwa kutero ndi malamulo ano azipereka;

f) Kuchita zonse zofunika ndiponso zoyenera kuti ntchito iyende bwino.

71.

(1) Mabilo onse azitumizidwa ku Seneti

(2) Membala aliyense wa Seneti ali ndi mwayi pakakhala Bilo mu Seneti:

a) Pasanathe masiku 14 Biloyo akaipereka mu Seneti kukonza mfundo kuti biloyo aikambirane mokwana monga kumafunikira; kapena

b) Patatha masiku 14 koma asanakwane masiku 40, kukonza mfundo yoti biloyo ibwere ku Nyumba ya Malamulo.

(3) Ngati bilo yobwera ku Seneti siinafike poikambirana ngati mfundo monga ndime ino ikunenera asanathe masiku 40, biloyo aitumize kwa Pulezidenti kuti akaibvomereze.

(4) Ngati Bilo aikambirana monga ndime 2(a) inenera biloyo aitumizenso kwa Sipikala wa Nyumba ya malamuloamene atsimikize kuti:

a) Palibe kusintha ndipo ndiye kuti Sipikala aitumize kwa Pulezidenti kuti ikhale lamulo; kaya

b) Ngati pali zosintha, Biloyo aipereke ku Nyumba ya Malamulo mpaka pathe masiku 14, koma ngati membala satulutsa mfundo kuti biloyo aikambiranenso

nthawiyo ndiye kuti biloyo aitumize kwa pulezidenti kuphatikizapo zosinthazo kuti akaibvomereze.

(5) Ngati Bilo aibwenza a Seneti chifukwa choti ambiri a ma Seneta achita voti pa mfundo motsata ndime 2(b):

a) Seneti ipereke zifukwa zoibwezera; ndipo

b) Sipikala wa Nyumba ya malamulo afikitse Biloyo kuti kapena aikambiranenso koma ngati mamembala ambiri aibvomereza atha kuitumiza kwa pulezidenti kuti ikhale lamulo

(6) Ngati Bilo ya munthu wamba aipereka ku seneti ndipo yabvomerezedwa aitumize kwa Sipikala wa Nyumba ya Malamulo a, amene aitule m'Nyumbayo kuti athe kuikambirananso kapena kuikonzakonza, ndipo ngati mamembala ambiri m'Nyumba ya Malamulo aibvomereza Biloyo aitumize kwa Pulezidenti kuti ikhale lamulo.

72. Seneti idzagwira ntchito kuyambira tsiku loyamba kukumana, limene lidzakhala mkati mwa masiku 30 pakangochitika chisankho cha ma khonsolo, mpaka idzasiyeso ntchito masiku 60 chisanachitike chisankho china cha makhonsolo. Koma nthawi ya seneti isabzyole zaka zitatu mwa njira iliyonse.

73.

(1) Ngati Bilo aitumiza kwa pulezidenti kuti ikhale lamulo, Pulezidentiyo ali ndi ufulu kuikana kapena kuivomereza.

(2) Ngati Pulezidenti akana kubvomereza Bilo, biloyo idzabwezedwa kwa Sipika wa Nyumba ya Malamulo ndi chidziwitso choti sanaibvomereze ndi zifukwa zake,ndipo Nyumba ya malamulo isakambiranenso Biloyo mpaka patapita masiku 21 kuchokera tsiku lachidziwitso choti yabwezedwa.

(3) Ngati Biloyo aikambirananso ndipo aPhungu ambiri aibvomereza, aitumizenso kwa Pulezidenti kuti ikhale lamulo. Izi zichitike nthawi iliyonse patapita masiku 21 amene akutchulidwa mu ndime (2) koma pasanathe miyezi 6 kuchokera tsiku limenero.

(4) Ngati Biloyo adzaibwezanso kuti aivomereze monga mwa ndime (3) Pulezidenti ali ndi udindo wovomereza kuti Biloyo ndi lamulo pasanathe masiku 21 atailandira.

(5) Bilo ikakhala lamulo monga Malamulo ano anenera, nthawi yomweyo ailengeze mu Gazette.

74. Palibe lamulo lililonse lidzakhala ndi mphamvu mpaka litalengezedwa mu Gazette koma Nyumba ya malamulo ingathe kugamula kuti lamulo lisakhale ndi mphamvu mpaka patapita nthawi atailengeza m'Gazette.

# MUTU VII

# CHISANKHO

75.

(1) Padzakhala Bungwe loyendetsa chisankho. M'bungwemo mukhale wapampando wake amene ndi Oweruza m'Bwalo Lalikulu la Milandu. Iyeyo adzasankhidwa ndi Bungwe loona ntchiti za chiweruzo (Judicial Service Commission) ndi mamembala osachepera 6 amene adzasankhidwe motsata malamulo.

(2) Munthu saloledwa kukhala pa udindo m'Bungwe loyendetsa chisankho ngati ndi Nduna ya Boma, wachiwiri kwa nduna , Phungu wa Nyumba ya Malamulo kapena ngati ali pa udindo wa ntchito za Boma.

(3) Kupatula momwe ndime ino inenera, munthu asiye udindo woyendetsa nawo chisankho;

a) Pakatha zaka zinai (4) kuyambira nthawi imene adalozedwa pokhapokha ngati amusankhaso pa udindowo kwa zaka zinayi; kapena

b) Ngati paoneka zina ndipo kuti akadapanda kukhala membala wa Bungwe loyendetsa chisankho ndiye kuti sadakakwanitsa kusankhidwa kapena kutchulidwa pa udindowo.

(4) Membala wa Bungwe loyendetsa chisankho angachotsedwe pa mpando ndi Pulezidenti ngati komiti yoona olembedwa ntchito m'boma ipempha pachifukwa choti sangathe kugwira ntchitoyo kapena sadziwa udindo wake.

76.

(1) Bungwe loyendetsa chisankho lidzagwira ntchito zonse zokhudza chisankho zopatsaidwa ndi malamulo ano.

(2) Mwazina, ntchito ndi udindo wa Bungwe loyendetsa chisankho ndi izi:

a) Kulemba malire a zigawo za a Phungu mosakondera poonetsetsa kuti zigawozo zili ndi olowa mkaundula wa voti ofanana koma moganiziranso:

(i) Kuchuluka kwa anthu;

(ii) Kubvuta kwa mayendedwe;

(iii) Mapiri, mitsinje ndi zina zotere, komanso momwe alili malire malinga ndi ntchito ya Boma.

b) Kulondoloza malire amene alipo pakapita zaka 5 ndikuwakonza potsata mfundo zomwe zili pa ndime 2(a);

c) Kugamula milandu yakusakhutira ndi m'mene chisankho chayendera;

d) Kuonetsetsa kuti zonse zilondolozeke ndipo zichitike monga momwe Malamulo ano kapena malamulo ena akunenera;

e) Kugwira ntchito iliyonse imene ipatsidwa ndi malamulo ena.

(3) Munthu aliyense wodandaula ku Bungwe loona za chisankho azikhalanso ndi ufulu wochita apilo ku Bwalo la Likulu la Chiweruzo (High Court) ngati sagwirizana ndi m'mene aigamulira nkhaniyo pogwiritsa ntchito ndime 2(c) ndi 2(d).

(4) Pogwira ntchito kapena kuyendetsa udindo wawo malinga ndi ndime ino Bungwe loyendetsa chisankho silizikakamizidwa kapena kuopsezedwa ndi munthu aliyense.

(5) Motsata ndime (3):

a) Bwalo lalikulu lamilandu lizikhala ndi mphamvu kuti limve madandaulo ndikuona ngati Bungwe loyendetsa chisankho lagwira ntchito yake kapena lagwiritsa ntchito udindo wake molondoloza chilungamo chonse ndiponso motsata Malamulo ano kapena malamilo ena; ndiponso

b) Nyumba ya Malamulo iibvomereza zimene lagamula Bungwe loyendetsa chisankho pokhudza malire a zigawo za a Phungu koma lisasinthepo chilichonse chokhudza malire a gawo la phungu pokhapokha bgati Bungwelo litawapempha kuti atero.

77.

(1) Anthu onse ali ndi ufulu kuchita nawo voti pa chisankho cha dziko lonse, chapadera, cha Pulezidenti, cha ma khonsolo kapena Referendamu koma mosataya ndime ino.

(2) Molondola ndime (3) munthu atha kulembetsa m’kaundula wa voti m’chigawo cha Phungu malinga ngati panthawi yopempha kuti alowe m’kaundula iyeyo:

a) Ndi nzika ya Malawi koma ngati si nzika, wakhala ali muno mu Malawi zaka zokwana 7;

b) Wokwana zaka 18 zakubadwa;

c) Amakhala m’chigawo cha Phungu kapena anabadwira kumeneko kaya akugwira ntchito kapena kuchita bizinesi kumeneko.

(3) Munthu sakwanitsa kulowa m’kaundula wa voti mdera la Phungu ngati:

a) Malinga ndi malamulo a muno m’Malawi adagamulidwa kuti ngwamisala kapena kuti padapezeka kuti ndiwosalonhosoka m’mutu;

b) Ali pa chilango chakuti anyongedwe chimene bwalo la milandu motsata mphamvu yao adapereka  tsiku loyamba kugwira ntchito malamulo ano lisanafike kaya litabzyola; kapena

c) Saloledwa kuti alowe nawo m’kaundula wa voti chifukwa chakuti adapezeka ndi mlandu wophwanya kapena wokhudza Malamulo ano asanayambe kapena atayamba kugwira ntchito, koma kuletsedwaku kudzangokhudza kaundula wa chisankhocho ndipo munthu wosabvomeredwayo adzaloledwa kulowa nawo mkaundula wokhuza chisankho achi chingachitike mtsogolo.

(4) Ngati munyhu ayha kulowa m’kaundula wa voti m’zigawo zingapo za a Phungu iyeyo aone kuti walembetsa nchigawo chimodzi mwa zigawozo.

(5) Sikuloledwa kuponya voti kawiri pa chisankho chimodzi

# MUTU VIII
# GAWO LA MUTU WA BOMA

78. Padzakhala Pulezidenti wa Dziko lonse yemwe ndi Mutu wa Boma ndiponso Wamkulu olamula Gulu la a Nkhondo onse m'Malawi muno.

79. Pazikhalanso Wachiwiri kwa Pulezidenti kuti azithandiza Pulezidentiyo. Iyeyo azigwira ntchito mphamvu ndi udindo umene angamupatse malamulo ano, kapena malamulo ena Pulezidenti.

80.

(1) Pulezidenti adzasankhidwa motsata Malamulo ano komanso monga malamulo akhazikitsidwa ndi Nyumba ya Malamulo anganenere.

(2) Pulezidenti azisankhidwa ndi anthu pogwiritsa ntchito voti yokhudza onse popanda tsankho.

(3) Woima nawo pa chisankho cha Pulezidenti adzalengeza munthu amene akhale Woyamba wachiwiri wake ngati atasankhidwa panthawi yomwe akulembetsa dzina lake pa m'ndandanda wa maina pachisankho cha Pulezidenti.

(4) Woyamba Wachiwiri kwa Pulezidenti azisankhidwa nthawi yomwe Pulezidenti akusankhidwayo ndipo dzina la munthu woti adzakhale Woyamba Wachiwiriyo lizioneka pa kalata yoponyera voti monganso zimakhalira ndi dzina la munthu wofuna kukhala pulezidenti yemwe wamuyenerezayo.

(5) Pulezidenti atha kusankha kwa Wachiwiri wake nagti aona kuti nkofunika kutero poganizira zochitika mdziko, ndipo atha kutero pamene akumulumbiritsa pa mpando wake, kapena nthawi ina iliyonse ngati mpandowo ulibe munthu ndipo ngati palibe wosankhidwa pa mpandowu ndiye kuti:

a) Zonse zimene zalembedwa pa mutu uno zidzawerengedwa motsatana ndikuti mpando Wachiwiri kwa wa Pulezidenti palibe, ndipo

b) Mpando wa Oyamba Wachiwiri kwa Pulezidenti udzangotchulidwa kuti Wachiwiri kwa Pulezidenti ngatikuti ndime 79 idangobvomereza za wachiwri yekhayo basi:

Koma ngati Pulezidenti adasankhidwa atalozedwa ndi chipani cha ndale ndiye kuti asasankhe Wakawiri wa Chiwiri kwa Pulezidenti wochokera mchipanimo.

(6) Ngakhale malamulo ano anenele mwina munthu atha kusankhidwa ngati Woyamba Wachiwiri kwa Pulezidenti kapena Wakawiri Wachiwiri kwa Pulezidenti pokhapo ngati:

a) Ndi nzika pakubadwa kapena ngati makolo ake ali ndi nzika; ndipo

b) Anakwana zaka 35 zobadwa

(7) Munthu saloledwa kuima nawo pa chisankho cha Pulezidenti kapena Wachiwiri wake kaya kulozedwa pa mpando wa Woyamba Wachiwiri kwa Pulezidentikapena Wakawiri Wachiwiri wa Pulezidenti ngati:

a) Adagamula juti ndi wamisala

b) Adalowa bankalapu ndipo ngati chimutchulireni malinga ndi malamulo sanamasulidwe ubankalapuwo;

c) Adapezekapo ndi mlandu ndi oweruza woonetsa kusakhulupilika kapena kuti ndi wopanda mkhalidwe, mkati mwa zaka zisanu ndi ziwiri asanadze masankhowo;

d) Ngati adaoneka kuti ndi nzika ya dziko lina;

e) Ali pa mpando wa ntchito za Boma kapena ndi Phungu ku Nyumba ya Malamulo pokhapokha ayamba wasiya ntchito inayo;

f) Akugwira ntchito ngati membala wa Gulu la Chitetezo kapena ndi msilikali wapolisi kapena

g) Anapezeka mkati mwa zaka zisanu ndi ziwiri asanadze masankhowo ndi mlandu m'bwalo la milandu woti walakwira malamulo okhudza chisankho cha Pulezidenti kapena cha a Phungu a ku Nyumba ya Malamulo malinga ndi malamulo opangidwa ndi Nyumba ya Malamulo.

81.

(1) Asanayambe ntchito yake munthu amene wasankhidwa kukhala Pulezidenti kapena Wachiwiri kwa Pulezidenti kaya kulozedwa kuti ndi ndi Wachiwiri kwa Pulezidenti kaya Wachiwiri kwa Wachiwiri wake adzamulumbiritsa Mkulu wa Chiweruzo pamaso pa anthu onse motere:

*"Ine………………………………………………..ndikulumbira kuti ndidzagwira ntchito pa udindo waukulu wa Pulezidenti (kapena Wachiwiri kwa Pulezidenti) wa Dziko la Malawi ndipo ndidzasunga, ndikuteteza malamulo ano moyenera ndi moona mtima, ndikuchita chilungamo kwa munthu aliyense motsata malamulo, mangawa. Motero Mulungu mundithandize.*

(2) M'malo molumbira, Pulezidenti kapena Woyamba Wachiwiri kaya Wachiwiri kwa Wachiwiri wake atha nagti afuna kutsimikiza chabe monga nagti akulumbira koma m'malo moti "*ndikulumbira*" anene kuti "*ndikutsimikiza*", komanso asatchule mawu ali pa ndime yotsilizawo.

(3) Aliyensew wosankhidwa pa mpando wa Pulezidenti kaya kulozedwa kuti ndi Woyamba Wachiwiri wake kapena Wachiwiri kwa Wachiwiri wake adzamulumbiritsa motsata ndime (1) pasanathe masiku 30 atasankhidwa.

(4) Pulezidenti kapena Woyamba kaya Wachiwiri kwa Wachiwiri wake adzagwira ntchito yake mpaka munthu womulandira mpando atamulumbiritsanso.

82. Pulezidenti ndi Woyamba Wachiwiri kaya Wachiwiri kwa Wachiwiri wake adzalandira malipiro, ndalama za phoso, kapena peshoni yomwe Nyumba ya Malamulo idzakhazikitse atakambirana ndi Pulezidenti ndipo akhale ndi nyumba za boma zokwana komanso ntchito wolipidwa ndi Boma monga momwe ingakonzere Nyumba ya Malamulo.

83.

(1) Pulezidenti ndi Wachiwiri wake adzakhala pa mpando zaka 5.

(2) Pulezidenti kapena Woyamba Wachiwiri kaya Wachiwiri kwa Wachiwiri wake atha kukhala pa udindo mosankhidwa kwa zaka zisanu kawiri kokha motsatana.

(3) Pakakhala kuti mpando wa Pulezidenti palibe munthu Woyamba Wachiwiri kwa Pulezidenti alowe m'malo mwake mpaka nthawi yake yotsalayo itakwana ndipo iye asankhe Woyamba Wachiwiri wake kwa nthawi yotsalayo.

84. Ngati Wachiwiri kwa Pulezidenti kapena Wachiwiri kwa Wachiwiri wake atha kukhala pa udindo mosankhidwa ndi Pulezidenti mpaka nthawi yokhala pampandowo itatha.

*85.* Ngati mpando wa Pulezidenti ndi Woyamba Wachiwiri wake ukhala padera nthawi ina iliyonse kabineti (*Komiti ya Nduna za Boma)* idzasankha pakati pao munthu wogwilizira mpando wa Pulezidenti ndi Woyamba Wachiwiri wake amene akhale pa udindowo pa masiku osabzola 60 kapena mpaka nthawi yokhala pa mpando wa Pulezidenti itakwana ngati kwatha kale zaka 4 za nthawi yokhala pa mpando Pulezidenti.

*86.*

(1) Pulezidenti komanso Woyamba Wachiwiri wake adzachotsedwa pa mpando ngati Nyumba ya Malamulo yamuimba ndikumupeza ndi mulandu woti Pulezidenti kapena Wachiwiri wakeyo wachimwira Malamulo waukulu.

(2) Ndondomeko yakazengedwe ka mlandu waukulu wotere izakhazikitsidwa ndi dongosolo la m'Nyumba ya malamulo koma aonetsetse kuti alondoloza chilungamo chonse ndi kuti chiweruzo chizichitika poyera ndi kuti:

a) Kuimbidwa kaya kugamulidwa mlandu waukulu wotere kudzatheka pokhapokha ngati ataononga ndi kulakwira malamulo ano kapena malamulo ena a dziko lino kulakwira malamulo kumene kungachitike kaya kuonekera nthawi imene Pulezidentiyo kapena Wachiwiri wake ali pa mpando;

b) Kuti mlandu woterowo apezeke nawo pafunika voti yotsinikiza ya anthu 2/3 ya mamembala a Nyumba ya Malamulo mkomitiya Nyumba yonse;

c) Kuti patsimikizidwe kuti walakwiladi kwakukulu pakhale 2/3 ya mavoti ya mamembala otsimikiza m'Nyumba zonse ziwiri;

d) Sipikala ndiye azikhala wa pa mpando pakakhala mlandu waukulu wofuna kumchotsa Pulezidenti m'Nyumba ya Malamulo ndipo mkulu wa Oweruza (Chief Justice) ndiye adzakhale wa pa mpando ukakazengedwa m'bwalo lamilandu;

e) Munthu wopezeka ndi mlandu otere atha kuimbidwanso mlandu wamba pa nkhaniyo mu bwalo lalikulu la milandu.

87.

(1) Pakakhala kuti Pulezidenti sangathe kugwira ntchito ndikuyendetsa udindo wake, Wachiwiri wake achite zonse m'malo mwake mpaka Pulezidenti ayambenso ntchito yake ngati kungatheke nthawi yake ikadalipo.

(2) Pulezidenti sadzakhala okanika kugwira ntchito yake monga tikuneneramu mpaka:

a) Pali umboni m'chikalata chobvomerezedwa ndi a katswiri a mankhwala oima paokha kuti Pulezidenti sangathe kugwira ntchito yake.

b) Umboniwo autsimikizenso Wachiwiri wake ndi anthu opitirira theka la amene ali pa mpando mu Kabineti pa nthawiyo; ndipo

c) Umboniwo watulidwa ndi Wachiwiri kwa Pulezidenti kwa Sipikala wa Nyumba ya Malamulo.

(3) Sipikala akalandila umboniwo malinaga ndi ndime (2), Wachiwiri Woyamba kwa Pulezidenti pomwepo ayambe kugwira ntchito pa udindo wa Pulezidenti ngati Wogwirizila.

(4) Ngati Pulezidenti wapezeka kuti sangathe kugwira ntchito yake monga ndime (2) ikunenera nthawi ina iliyonse,kutatero atha kuoereka umboni mchikalata wotsimikizidwanso ndi bwalo la katswiri a chipatala oima paokha kunena kutiatha kugwira ntchito pa udindo wake ngati Pulezidenti: koma

a) Nyumba ya Malamuloikalandira umboni umenewo ili ndi mpata wa masiku 30 kuti itsimikize ngati Pulezidenti angathedi kapena sangathe kugwira ntchito pa udindo wake ngati Pulezidenti; ndipo

b) Ngati Nyumba ya Malamulo igamula Pulezidenti kuti sangathe kugwira ntchito pa udindowo pa voti 2/3 ya mamembala aibvomere,ndiye kuti Wachiwiri wake

adzapitirira kugwirizira udindo wa Pulezidenti mpaka Nyumba ya Malamulo itatsimikiza kuti Pulezidenti atha kugwiranso ntchito pa udindo wake; kapena

c) Ngati Nyumba ya Malamulo igamula ndi voti ya 2/3 ya mamembala ake kuti Pulezidenti sakulepheranso kugwira ntchito pa udindo wa Pulezidenti ndiye kuti Pulezidenti ayambenso kugwira ntchito yake pasanapite masiku 30 votiyo itachitika.

(5) Ngati papita miyezi 12 kuchokera patsiku limene sipikala wauzidwa kuti Pulezidenti satha kugwira ntchito yake ndipo Nyumba ya Malamulo siidatsimikize kuti Pulezidentiyo angagwirenso ntchito yake monga ndime (4) ikunenera ndiye kuti chisankho cha Pulezidenti chichitikenso.

(6) Zolembedwa pa ndime inozi zikhudzanso kugwira ntchito kwa Wachiwiri kwa pulezidenti mosasiyanitsa kupatula kuti umboni udzaperekedwa ndi Pulezidenti yemwe aitumize nkhaniyo kwa Sipikala ndipo ntchitoya udindo wa Woyamba Wachiwiri kwa Pulezidentiyo adzaigwire ndi m'modzi mwa Nduna za Boma amene Pulezidenti angamusankhe.

(7) Bungwe loima palokha la akatswiri a ntchito zachipatala limene likutchulidwa mndime ino lidzasankhidwa motsata ndondomeko zopangidwa ndi Nyunba ya Malamulo.

88.

(1) Pulezidenti ali ndi udindo kuonetsetsa kuti zonse zili m'Malamulo ano zikutsatidwa ndi Gawo la Mutu wa Boma, ndipo ngati Mutu wa Boma adzateteza ndi kutsata Malamulo ano chifukwa ndiwo mathelo onse a Malamulo muno m'Malawi.

(2) Pulezidenti aonetse utsogoleri weniweni pofunitsitsa umodzi monga Malamulo ano ndi malamulo ene mdziko muno afunira.

(3) Pulezidenti ndiponso nthumwi za Kabineti atasankhidwa , saloledwa kukhala pa mpando wina uliwonse wa Boma ndipo saloledwanso kugwira ntchito ina iliyonse yolipidwa kupatula ya udindo wawo ndipo saloledwanso kugwira ntchito ina iliyonse yolipidwa kupatula ya udindo wawo ndipo pasanathe miyezi itatu akasankhidwa alongosole ndikunena poyera umo chilili chuma chawo ,ngongole kapena bizinesi

zomwe ali nazo kapena zomwe amachita nawokapena za akazi awo kapena m’mene akuwayendetsera monga umo zilili pa nthawiyo; ndipo mpokhapokha kuti Nyumba ya Malamulo inenere mwina kalongoseledweko kakhale mchikalata cholembedwa chimene chiperekedwe kwa Sipikala wa Nyumba ya Malamulo yemwe akangochilandira nthawi yomweyo achitule mu ofesi ya Boma monga Nyumba ya Malamulo ilongosolele.

(4) Bizinesi iliyonse ya pulezidenti kapena ya Nduna ichitike m’malo mwa iwo mowasungira koma izichitika motsana mwambo umene uli pa ndime ino.

(5) Pulezidenti kapena Nduna saloledwa kugwiritsa ntchito udindo wawo kuti apezerepo phindu ndipo asapezeke kuti zofuna zawo zikukolana ndi zochitika pa ntchito ndi pa udindo wawo

89.

(1) Pulezidenti adzakhala ndi mphamnu komanso udindo:

a) Wobvomereza ma Bilo ndi kulamula kuti ma Bilo okhazikitsidwa ndi Nyumba ya Malamulo akhale lamulo;

b) Woitanitsa misonkhano ya Nduna zonse (Kabineti) ndikukhala wapampando pa misonkhano ya Kabineti;

c) Wopatsa anthu maulemu;

d) Wokhazikitsa anthu pa maudindo monga ziyenera malinga ndi mphamvu yopatsidwa ndi Malamulo ano kapena malamulo ena;

e) Motsata Malamulo ano, kusankha ndi kutumiza, komanso kulandira ndi kuzindikira akazembe ndi onse oimira kapena kugwira ntchito m’malo mwa maboma kapena mabungwe a kunja kwa dziko lino;

f) Wokambirana zoti agwirizane, kusindikiza, kulowa kapena kukhala nawo mu mgwirizano wa pakati pa maiko kapena kutuma nduna, kapena akazembe pantchitozi;

g) Wokhazika mabungwe ofufuza umo nkhani idayendera;

h) Woyumiza mkangano uliwonse wokhudza Malamulo ano kubwalo loweruza la pamwamba; ndipo

i) Woitanitsa Referendamu ndi kufunsa maganizo a anthu pa nkhani zofunika monga malamulo ano kapena malamulo ena afunira.

(2) Pulezidenti atha kukhululukira anthu wopezedwa mlandu ndi oweruza ndi kulamula kuti chilango chisagwire ntchito, ndikufupikitsanso masiku pa chilango chokhala m'ndende kapena kuchotsera kuti asakhale m'ndende:

Koma;

a) Zogamula malinga ndi m'ndime ino zidzachitika mogwirizana ndi Komiti ya anamkungwi pankhani zokhululukira chilango imene idzakhazikitsidwa ndi malamulo ano; ndiponso

b) Pulezidenti alibe mphamvu yokhululuka pa mlandu waukulu wakuti iye kapena wachiwiri wake walakwira malamulo ano.

(3) Chaka chilichonse dongosolo la chuma cha Boma lisanaperekedwe, Pulezidenti azipita ku Nyumba ya Malamulo ndi:

a) Kuwauza a Phungu momwe zinthu ziliri mdziko muno ndikuwadziwitsa za mfundo zimene Boma lakonza malinga ndi m'mene akuonera zinthu;

b) Kupereka lipoti la umo zinthu zayendera m'chaka chimene chatha ; ndi

c) Kuyankha mafunso.

(4) Pulezidenti adzamuitana ku Nyumba ya Malamulo kuti akayankhe mafuso panthawi imene dongosolo la kachitidwe ka zinthu m'Nyumba ya Malamulo linganenere kapena potsata mfundo ya Nyumba ya Malamulo kapena Seneti.

(5) Kupatula umo malamulo ano kapena ena anganenere, Pulezidenti adzagwiritsa ntchito mphamvu zones zofunika ndizothandiza kuti ntchito yake iyende monga Malamulo anoanenere.

(6) Mphamvu ndi ntchito ya Pulezidenti zidzagwiritsidwa ntchito ndi iye mwini kapena ndi Nduna kaoena mkulu wa m'Boma amene angamupatse mphamvu yotero mchikalata.

90.

(1) Zolamula Pulezidenti zinenedwe mchikalata chosindikizidwa ndi iye mwini.

(2) Pulezidenti akasindikiza pakhalenso chitsimikizo cha Boma.

91.

(1) Munthu amene ali paudindo wa Pulezidenti kapena akugwira ntchito ya Pulezidenti sayenera kumtengera kubwalo loweruza kuti akamuyimbe mlandu woti alipire, komabe mpando wa Pulezidenti ugonjere zomwe bwalo al milandu lalamula zokhudza ufulu wa anthu malinga ndi Malamulo ano.

(2) Munthu amene ali pa udindo wa Pulezidenti sadzamuimba mlandu wolakwira Boma m'bwalo la mlandu pa nthawi imene ali pa mpando pokhapokha ali kumuzenga mlandu waukulu woti walakwira Malamulo ano.

(3) Amene anali Pulezidenti akatula pansi udindo wake asazengedwe mlandu ngati munthu wamba chifukwa cha zimene iyeyu anachita pa udindowo pa nthawi imene anali pa mpando koma kutero sindiye kuti sangalakwire pa zina.

92.

(1) Pazikhala Bungwe la Nduna za Boma (Kabineti) momwe muzikhala Pulezidenti, Wachiwiri wake, Woyamba Wachiwiri kwa Wachiwiri wake, ndiponso Nduna ndi Achiwiri kwa nduna amene Pulezidenti angamathe kuwakhazikitsa nthawi ndi nthawi.

(2) Kabineti idzagwiritsa ntchito mphamvu ndi udindo umene Malamulo ano kapena Malamulo ena akupereka, ndipo idzalangiza Pulezidenti pa mfundo za Boma komanso pa nkhani zimene Pulezidenti angatulutse.

(3) Mkhalapampando wa kabineti ikakumana ndi:

a) Pulezidenti ; kapena

b) Ngati iye palibe, Woyamba Wachiwiri wake; kapena

c) Wachiwiri kwa Wachiwiri wa Pylezidenti ngati Pulezidentiyo di Woyamba wachiwiri wake palibe

(4) Pazikhala mlembi wa Kabineti amene adzasankhidwa ndi pulezidenti. Iyeyo akhale wa ntchito za Boma yemwe:

a) Aziyendetsa ntchito ya Kabineti;

b) Ali ndi udindo, pansi pa Kabineti, wokonza ntchito zones za kabineti ndi kusunga zolembedwa zones zokhudzana ndi Kabineti

c) Azituma mfundo kuchokera m'Kabineti kupita kwa anthu onse okhudzana ndi Kabineti;

d) Azitumiza mfundo kuchokera m'Kabineti kupita kwa anthu onse okhudzidwa kapena ofunikira malinga ndi mfundozo; ndiponso

e) Azigwira ntchito zina zonse monga Kabineti ingalamulire.

93.

(1) Pazikhala Nduna ndi Nduna zazing'ono zomwe zidzasankhidwa ndi Pulezidenti, ndipo osankhidwayo adzagwira ntchito, kuphatikiza kuyendetsa ma Gawo a boma, zomwe Pulezidenti angawapatse motsata Malamulo ano.

(2) Dipatimenti ili yonse ya Boma oyiyang'anira ndi mlembi wake yemwe adzakhala pansi pa Nduna kapena Nduna yaing'ono ndipo ntchito yake idzakhala ya Boma.

94.

(1) Pulezidenti adzakhala ndi mphamvu yosankha Nduna kapena Nduna zazing'ono ndiponso anthu oti akhale nawo m'Kabineti mipandoyo ikakhala yopanda anthu.

(2) Munthu asasankhidwe kukhala Nduna kapena Nduna Yaing'ono pokhapokha ngati iyeyo:

a) Ndi nzika ya mu Dziko amene wafika zaka 21 zakubadwa;

b) Angathe kuyankhula ndi kuwerenga Chingerezi; ndipo

c) Ali nawo mkaundula wa voti mchigawo cha phungu.

(3) Ngakhale ndime (2) ikutero munthu asasankhidwe Nduna kapena Nduna Yaing'ono ngati:

a) Iye ndi nzika ya dziko lina;

b) Ndi wosokonezeka mutu malingana ndi malamulo a muno mu Dziko;

c) Adamuzenga ndikumupeza ndi mlandu woonetsa kusakhulupirika kapena kusowa mkhalidwe mkati mwa zaka khumi ndi ziwiri izo zangopita;

d) Adalowa bankalapu ndipo sanamasulidwe malinga ndi malamulo muno m'Malawi;

e) Akugwira ntchito kapena ali ndi mpando wa ntchito za Boma pokhapokha ngati malamulo ano alola kutero ngakhale kuti ali pa mpando kapena pa ntchitoyo, kapena ngati watula pansi mpandowo kuti atje kuima nawo pachisankho.

f) Ndi Msilikali wa Nkhondo kapena wa Polisi muno m'Malawi.

g) Oweruza adamupeza ndi mlandu wolakwira malamulo wokhudza chisankho cha Pulezidenti kapena chisankho cha a Phungu malinga ndi malamulo.

95.

(1) Nduna kapena Nduna Yaing'ono isagwire ntchito yake mpaka italumbira kapena kutsimikizira poyera monga malamulo anganenere.

(2) Pulezidenti ali ndi mphamvu yochotsa Nduna kapena Nduna Yaing'ono pa mipando yao.

96.

(1) Mamembala a Kabineti adzagwira ntchito izi:

a) Kulangiza Pulzienti;

b) Kulondoloza ndi kutsogolera zochitika m'magawo a Boma kuphatikiza m'Mabungwe a Boma;

c) Kukonza ma Bilo kuti apite ku Nyumba ya Malamulo ndi kufotokozera za ma Bilowo;

d) Kukonza ndi kufotokozera Nyumba ya Malamulo ndondomeko ya chuma cha Dziko ndi dongosolo loyendetsera chitukuko cha chuma;

e) Kukhala nawo mu Nyumba ya Malamulo kuti ayankhe mafunso ndiponso kukambirana nawo mfundo zokhudzamomwe Boma liyendetsere dziko

f) Kuthandiza Pulezidenti za mgwirizano ndi mapangano oti tikhale nawo ndi maiko kapena mabungwe akunja ndi kufotokozera Nyumba ya Malamulo;

g) Kusenza udindo wogwiritsa ntchito malamulo; ndiponso

h) Kugwira ntchito iliyonse yofunika kuti ayendetsere udindo wawo motsata malamulo ano komanso monga malamulo ena kapena momwe Puulezidenti anganenere.

(2) Pogwira ntchito zimene zalongosoledwa mu ndime ino, kabineti idzakonza mfundo zoti zikhale malamulo m'nthawi yokwana kuti akatswiri pa ntchitozo ndiponso anthu aperekepo maganizo awo.

97. Nduna zones zili ndi udindo kwa Pulezidenti woyendetsera ma gawo a Boma amene zimayang'anira.

98.

(1) Padzakhala mpando wa katswiri wa Malamulo amene adzakhala mlangiziwa Boma pa Malamulo.

(2) Mphamvu zimene zapatsidwa kwa katswiri wa Malamulo zitha kugwiritsidwa ntchito ndi munthu wosankhidwayo kapena ndi munthu wina wa ntchito za Boma pansi pa katswiriyo motsata malangizo ake.

(3) Katswiri wa Malamulo adzasankhidwa ndi Pulezidenti.

(4) Mpando wa Katswiri wa Malamulo udzakhala wopanda munthungati mwiniyo wagwira ntchito zaka 5 kapena watula pansi udindo kapena walandira penshoni , malinga ndi chimene chingayambe kuonrka, koma munthuyu atha kumusankhanso kuti apitirize mpaka zaka zina osabzola zisanu, monga Puleziddenti angaganizire.

(5) Mpando wa Katswiri wa Malamulo utha kupatsidwa kwa munthu ngati nduna kapena kwa ogwira ntchito ya Boma.

99.

(1) Padzakhala Mkulu Wozenga Milandu ya Boma yemwe adzakhala wa ntchito ya Boma.

(2) Mkulu wozenga milanduyu adzakhala ndi mphamvu pamlandu wa Boma uliwonse ngati aganiza kutero:

a) Yotsegula ndi kuzenga munthu aliyense milandu , wolakwila Boma m'bwalo la milandu lirilonse (*kupatula m'bwalo lamalamulo a nkhondo)* chifukwa choti munthuyo walakwira lamulo;

b) Yolandira pa njira ndikupitiriza kuzenga mlandu wolakwira malamulo a Boma umene munthu wina kapena gawo linauyamba; ndiponso

c) Nthawi ina iliyonse angathe kuuletsa mlandu wolakwira Boma umene udatsegulidwa ndi iye kapena munthu wina, kapena gawo lina ngati usanafike pougamula.

(3) Mphamvu zimene zapatsidwa kwa Mkulu Wozenga milandu ya Boma ndi ndime (2)(b) ndi (c) ndi zakezake ndipo sizikhudza munthu wina kapena gawo lina; ndipo akazigwiritsa ntchito apereke zifukwa zofunika kutero kwa Komiti yoona za Malamulo kapena ku Nyumba ya Malamulo pasanapite masiku 10.

Koma ngati wina kapena gawo lina lazenga munthu mlandu wolakwira Boma palibe choletsa kuti eni akewo ausiye kapena kuuletsa mlanduwo ngati bwalo lamilandu lingabvomere.

(4) Malinga ndi ndime ino, apilo pa chiweruzo chokhudza mlandu wa Boma kapena zoti oweruza agamule pa nkhani yomasulira lamulo kuti zithandize pa mlandu ndi nkhanibe malinga ndi mlanduwo:

Koma Mkulu Wozenga Milandu ya Boma asagwiritse ntchito mphamvu zopatsidwa ndi ndime 2(c) kuti aletse mlandu wa apilo ngati munthu wapezeka kuti adalakwira boma pa mlandu uliwonse kapena ngati munthuyo adapempha chiweruzo kapena kupempha oweruza kuti apereka maganizo awo pa lamulo.

100.

(1) Kupatula m'mene anenera pa ndime 99(a) mphamvu zimene zipatsidwa kwa mkulu wozenga milandu zitha kugwiritsidwa ntchito ndi munthu amene adasankhidwa pa udindowo kapena ndi munthu wolembedwa m'Boma amene akugwira ntchitoyom'malo mwake koma motsata malangizo ake komanso motsata malamulo.

(2) Ngakhale ndime (1) kutero:

a) Munthu amene wasankhidwa pa mpandowa Mkulu Wozenga Milanduya Boma ali ndi udindo wotsimikizira Komiti yoona za Malamulo kuti akugwira ntchito yake bwino kuphatikizapo ena onse amene akugwira ntchitoyo m'malo mwake potsata ndime (1); ndiponso

b) Lamulo likonze dongosolo ndikuletsa kuti mphamvu zimene ndime ino likupereka zisapatsidwe kwa msilikali aliyese wa Polisi.

101.

(1) Pulezidenti ndiye adzasankha munthu kuti akhale mkulu wa milandu ya boma motsimikizidwa ndi Bungwe lolemba a ntchito za boma koma atsimikizire kuti munthuyi angathedi kugwira ntchitoyi ndikumazenga milandu mosamvera wina.

(2) Munthu anene asankhidwa kukhala Mkulu Wozenga Milandu ya Boma kapena kuti agwire ntchitoyo m'malo mwake, agwiritse ntchito mphamvu ndi zones zimene Malamulo ano kapena malamulo ena ampatsa mwayekha mosalamulidwa ndi munthu kapena wina aliyense komanso motsatira lamulo.

Komabe Mkulu Wozenga Milandu ya Boma kapena katswiri wa Malamulo atha kuitanidwa ndi Komiti yoona za malamulo ya Nyumba ya malamulo kuti afotokoze m'mene wagwiritsira ntchito udindo wake.

102.

(1) Mpando wa Mkulu Wozenga Milandu udzakhala wopanda munthu ngati mwini wake wagwira ntchitoyo zaka zisanu kapena watula pansi mpandowo kapena walandira penshoni malinga ndi chimene chingayambire kuchitika mwa zinthu zatchilidwazi:

(2) Munthu yemwe ali pa mpando wa Mkulu Wozenga Milandu ya Boma angachotsedwa pa mpando ndi Pulezidenti nthawi yake isanakwane ngati Pulezidenti akhutira kuti munthuyo:

a) Sakutha kugwira ntchito yake;

b) Pachitika china, kutero kuti sangathe kugwira ntchito yake ndi kusunga udindo wake mosakondera.

c) Sangathe kugwira ntchito pa zifukwa zina; kapena

d) Wakwanitsa zaka zoti alandire penshoni.

# MUTU IX

# GAWO LA OWERUZA

103.

(1) Mabwalo onse amilandu ndiponso onse oweruza adzagwira ntchito ndi kugwira ntchito mphamvu zao kapena kuyendetsa ma udindo awo mwaokha mosaopa munthu aliyense kapena gawo lililonse.

(2) Gawo la oweruza lidzakhala ndi mphamvu pa nkhani iliyonse ya milandu ndipo lokhalo lidzagamula ngati liri ndi mphamvu pa nkhaniyi.

(3) Sikuloledwa kukhala ndi Bwalo Loweruza Lapamwamba la Apilo kapena Bwalo Lalikulu la Milandu.

104.

(1) Pazikhala Bwalo Loweruza Lapamwamba la Apilo la Malawi limene lidzalhala ndi mphamvu zonse monga malamulo ano kapena malamulo ena anganenere.

(2) Bwalo Loweruza Lapamwamba la Apilo lidzakhala ndi mphamvu zotsiriza pa maapilo ndipo lidzakhala ndi mphamvu yogamula milandu ya apilo kuchokera ku Bwalo lamilandu lalikulu komanso kuchokera ku mabwalo a milandu amene lamulo lingakhazikitse.

105.

(1) Owerza m'Bwalo Lamilandu Lapamwamba la Apilo:

a) Mkulu wa Milandu (Chief justice)

b) Ena oweruza milandu ya apilo osachepera atatu monga m'menelamulo linganenere.

(2) Pamene bwaloli likumvera mlandu, kupatulako malndu wofuna chithandizo, chiweruzo pa nkhaniyo chisanadziwike pazikhala oweruza osachepera atatu motero kuti pogamula nkhaniyo mbali zones zisakhale zofanana.

(3) Oweruza pa apilo m'Bwaloli asankhidwe pogwiritsa ntchito ndime 111 basi.

106.

(1) Ngati pakhala oweruza ochepera chifukwa choti palibe munthu wina pa mpando kapena chifukwa cha momwe ndime 107 ikunenera, Pulezidenti atha kusnkha oweruza a m'Bwalo Lalikulu la Milandu kuti agwirizire mipando inayo molangizidwa ndi bungwe loona za ntchito za milandu.

(2) Wogwirizira mpando woweruza m'Bwalo la Apilo la pamwamba adzagwira ntchitoyo mpaka ngati asankhidwa kuti ndi Wamkulu wa Oweruza kapena aweruza m'Bwalo la Pamwamba la Milandu la Apilo monga ndime 111 ikunenera, koma adzaleka kugwira ntchito yoweruz m'Bwalo ngati:

a) M'Bwalolo muli oweruza odzyola atatu chifukwa chakuti asankhilapo owerza wina kapena ena monga momwe ikunenera ndime 111 kapena ngati oweruza pa apilo kapena ogwirizira amene sadathe kumaweruza nawo m'Bwalolo ayambanso ntchito zao monga kungatheke ndi ndime 107.

b) Waloledwa kusiya ntchito ya oweruza m'Bwalo la Apilo kapena wogwirizira oweruza potsata ndime 107.

107.

(1) Oweruza m'Bwalo la Apilo Lapamwamba kapena ogwirizira mpando wake atha kuloledwa kusiya udindo wogwira ntchitoyo pa nthawi imene ingafunikire:

a) Pa chifukwa chakuti oweruzayokapena mlowam'malo wake anakhudzidwa ndi mlanduwo m'Bwalo lamilandu kumene ikuchokera nkhaniyo ndipo ndi chiweruzo cha pa mlanduwo chimene tsopano chikupita ku Apilo;

b) Pa chifukwa china chilichonse chimene ka Mkulu wa oweruza kapena Bungwe loona ntchito za oweruza zinganenere kuti nzolepheretsa kuti akhale nawo pa udindo wake.

(2) "*Kukhudzidwa pa mlandu*" pa ndime ino kuphatikizanso"

a) Munthu aliyense woweruza pa mlanduwo;

b) Munthu amene adafunsidwa kuti akaime m'malo mwa aliyense pa mlanduwo ngati katswiri wa malamulo; kapena

c) Munthu amene adapempha kuti aziimira okhudzidwa pa mlanduwo ngati katswiri wa malamulo.

108.

(1) Pazikhala Bwalo lalikulu lowruza limene lidzikhala ndi mphamvu zones zozenga ndi kumvera ndiponso kugamula mlandu wolipilitsana kaya mlandu wolakwira Boma malinga ndi malamulo mdziko.

(2) Bwalo limeneli lili ndi mphamvu kufufuza ndi kuona ngati lamulo,chochitika, kapena mfundo ya Boma zikutsatira malamulo ano , kusiya zimene malamulo ano salola,

ndipo lidzakhal ndi mphamvu pa mlandu monga momwe Malamulo ano kapena ena anganenere.

109.

Oweruza m'bwalo lalikulu azakhala monga m'mene Nyumba ya malamulo inagnenere.

110.

(1) Pazikhala ma bwalo a milandu pansi pa Bwalo lalikulu lamilandu monga kungfunikire ndi lamulo ndipo oweruza akhale odziwa malamulo otchedwa Majisitiliti kapena anthu awo si akatswiri ngati Majisitiliti wamba.

(2) Padzakhalanso bwalo la milandu loweruza za pantchito (Industrial Relations Court) lomwe lidzakhala pansi pa bwalo lalikululamilandu limene lidzakhala ndi mphamvu loweruza mikangano ya anthu a pa ntchito ndiponso zina zonse zokhudza pa ntchito ndipo oweruza ake ndi malamulo akaweruzidwe zikhale monga malamulo adzakonzere.

(3) Nyumba ya malamulo itha kupanga kuti pakhale mabwalo oweruza milandu yokhudza miyambo oweruza ake nakhala anthu wamba kapena mafumu.

Koma mphamvu ya oweruza amenewa zikhale pa milandu yolipitsana yokhudza miyambo ndi ina yaing'onoing'ono yokhudza malamulo akale achingerezi ndi malamulo opangidwa mom'muno monga momwe malamulo anganenere

111.

(1) Wamkulu wa oweruza adzasankhidwa ndi Pulezidenti motsimikizidwa ndi 2/3 ya mamembala a Nyumba ya malamulo amene alinawo m'nyumbayo nthawi ya voti.

(2) Oweruza onse adzasankhidwa ndi Pulezidenti motsata zomwe Bungwe loona ntchito za chiweruzo lanena

(3) Mamajisitireti ndiponso onse osankhidwa kuti aziweruza adzasankhidwa ndi Wamkulu wa Oweruza motsata malangizo a Bungwe loona a ntchito za chiweruzo ndipo adzakhala pa mpando mpaka atakwanitsa zaka 70 zakubadwa pokhapokha ngati atachotsedwa motsatira ndime 119.

(4) Pa ndime ino "*mpando wa oweruza*" utanthauza:

a) Owerza pa apilo kapena wogwirizira m’Bwalo lapamwamba la apilo;

b) Oweruza m’bwalo lalikulu la Milandu kapena wogwirizira wake;

c) Mlembi kapena wachiwiri wake wa m’bwalo lapamwamba lachiweruzo cha apilo kapena m’bwalo lalikulu lamilandu.

d) Majisitireti wa mtundu uliwonse; ndiponso

e) Munthu oweruza m’bwalo la miyambo.

(5) Kuti “oweruza” pa ndime ino kutanthauza oweruza m’bwalo lamilandu la pamwamba la apilo, wogwirizura m’menemo, oweruza kapena wogwirizira wake m’Bwalo lalikulu lamilandu.

112.

(1) Munthu sangakhale oweruza m’Bwalo lalikulu la milandu mpaka:

a) Ali, kapena anali, oweruza m’bwalo limene lili ndi mphamvu zonse pamilandu yolipitsana kapena yolakwila Boma; kapena

b) Atha kugwira ntchito yaukatswiri wa malamulo m’bwalo loweruzalo ndipo wakhala ndiufulu wotero pa zaka zosachepera khumi.

(2) Malinga ndi ndime ino, munthu angathe kugwira ntchito ngati katswiri wa malamulo ngati adamuitana, malinga ndi mwambo wake kapena ngati dzina lake lidalowa m’buku kapena mnjira zilizonse atha kugwira ntchitoyo ndipo sadamuletse kapena kumutsekera ufulu wokhala katswiri wa malamulo ngakhale kuti iyeyo:

a) Ali pa mpando kapena akugwira ntchito pa mpando umene umulepheretsa kuti azigwira ntchito yaukatswiri wa malamulo m’bwalo loweruza; kapena

b) Alibe chikalata chomulola kuti azigwira ntchito kapena sanakwanitse zina zofunika kuti aloledwe kugwira ntchito ya ukatswiriwa malamulo.

113.

(1) Ngati pa mpando wa Wamkulu wa Oweruza palibe munthu, kapena wamkulu sangathe kugwira ntchito yake pa chifukwa chilichonse ndiye kuti ntchito zakezo azigwire ndi oweruza amene ngotsatira msinkhu mwamwambo wake mu Bwalo lapamwamba la apilo kapena m'Bwalo lalikulu la Milandu mpaka wina atasankhidwanso ndikuyamba kugwira ntchito pa mpandopo kapena mwini mpandoyo atayambanso kugritsa ntchito yake monga mmene zingachitikire.

(2) Ngati palibe munthu pa udindo uliwonse wawoweruza kapena woweruza wasankhidwa kuti agwirizire mpando wa Wamkulu wa oweruza kapena alephera kugwira ntchito yoweruza pa zifukwa zilizonse, ndiye kuti Pulezidenti, motsata malangizo a Bungwe loona za chiweruzo atha kusankha munthu yemwe aloledwa kuankhiwa pa mpando wa oweruzawo kuti agwirizire udindowo motsata ndime ino.

114.

(1) Wamkulu wa owerza ndi onse oweruza azilandira ndalama pa mwezi chifukwa cha ntchitozo ndipo nthawi yawo ikakwana akhalenso pa penshoni ndikulandira ndalama zapadera kapena chiongoladzanja monga m'mene Nyumba ya malamulo ingagamulire nthawi ndi nthawi.

*(2)* Malipiro a pamwezi ndi ndalama za phoso zina zilizonse zimene amalandira oweruza zisadulidwe mosabvomerezedwa ndi mwini wake pa nthawi imene iwo ali paudindowo ndipo zizionjezeredwa nthawi ndi nthawi kuti zizikhala ndi mphamvu yomwe zidali nayo poyamba pomwepo ndipo zizichokera kuthumba lapadera la *"Consolidated Fund"*

115.

Munthu wokhala pa udindo wachiweruzo saloledwa kuyamba ntchito yake mpaka atalumbira kuti adzagonjera malamulo motsatira mmene malamulo angakonzere.

116.

Pazikhala bungwe loona za Oweruza kuti liziyang'anira kagwiridwe kawo ka ntchito. Bungweli lidzakhala ndi mphamvu zimene malamulo ano kapena malamulo ena amene mosatsutsana ndi malamulo ano.

117.

M'bungwe loyang'anira ntchito za oweruza mudzakhala anthu awa:

a) Wamkulu wa chiweruzo amene ali ndi wapampando;

b) Pampando wa bungwe loona za ogwira ntchito za boma kapena wina aliyense yemwe angamantume m'malo mwake.

c) Oweruza m'Bwalo la Pamwamba la Apilo kapena m'Bwalo lalikulu la milandu yemwe adzasankhidwa ndi Pulezidenti atakambirana ndi mkulu wa oweruza , ndi

d) Katswiri wa malamulo kapena Majisitireti amene angalozedwe pa ntchitoyo ndi Pulezidenti motsata malangizo a Mkulu a Oweruza.

118.

Bungwe loyang'anira ntchito za oweruza lidzakhala ndi mphamvu:

a) Kusankha munthu pa mpando woweruza;

b) Kugwiritsa ntchito mphamvu zokhudza mwambo wa anthu oweruza motsatira malamulo ano;

c) Kupereka maganizo, motsata ndime 119 kuti munthu achotsedwe pa udindo woweruza;

d) Motsata Malamulo ano kupereka maganizo ao kwa Pulezidenti monga momwe malamulo afunira; ndi

e) Kugwiritsa ntchito mphamvuzimene zapatsidwa ku Bungwelo ndi malamulo ano kuti ntchito yao iyende bwino. Koma izi sizitanthauza kuti atsekereze munthu uyo ali pa udindo wa chiweruzo kuchita apilo ku Bwalo logamulira nkhani yomukhudza.

119.

(1) Pokhapokha ngati ndime ino inene munthunuyo ali pa udindo woweruza m'Bwalo lalikulu la milandu atule pansi mpando wake akakwanitsa zaka zobadwa zatchulidwa m'ndime (6);

Koma Pulezidenti atakambirana ndi Bungwe loyang'anira ntchito za oweruza atha kumulola woweruza amene wafika pa msinkhu umenewo kuti apitirire pa udindowo kwa nthawi imene ingafunire kuti adzapereke chiweruzo kapena kapena kuchita

zina zofunikira pokhudza milandu imene idayambidwa iye ali pa mpando asanakwanitse zakezo.

(2) Oweruza m'bwalo lalikulu la milandu atha kuchotsedwa pa udindo chifukwa chakuti akulephera kugwira ntchitoyo kapena wachimwira pa chikhalidwe basi, koma asachotsedwe pokhapokha ndime (3) ndi (4) zakwanitsidwa.

(3) Pulezidenti angathe posindikiza chikalata chodindidwa ndi Boma, atakambirana ndi Bungwe loyendetsa ntchito za oweruza , kumchotsa oweruza ngati mfundo yoti amuchotse chifukwa cholephera kugwira ntchito kapena kutaya chikhalidwe:

a) Yakambidwa m'Nyumba ya malamulo;

b) Yabvomerezedwa ndi mamembala ochuluka malinga ndi chiwerengero cha onse m'Nyumbayo, ndipo

c) Yatulidwa kwa Pulezidenti ngati pempho lapadera kuti woweruzayo achotsedwe;

Ndondomeko yochotsa oweruza pa mpando itsate chilungamo chenicheni.

(4) Ngati uthenga woti pali maganizo wopempha Nyumba ya Malamulo kuti mfundo yochotsa woweruza aikambirane waperekedwa kwa Sipikala, Pulezidenti atakhutira, ndipo atakambirana ndi Bungwe loyendetsa ntchito za oweruza ndikutsimikiza kuti kutero nkokomera anthu, atha kumpumuza oweruzayo pa udindowo.

(5) Kuimitsidwa pa ntchito kwa oweruzayo motsatira ndime yachinayi (4) kutha kuthetsedwa ndi Pulezidenti atakambirana ndi Bungwe loyendetsa ntchito za oweruza, ndipo ngakhale zitatani kuzitha ngati mfundo yoti amchotse yabwezedwa isanakambidwe m'Nyumba ya Malamulo, kapena ngati itakambidwa sidabvomerezedwe ndi aphungu.

(6) Zaka zakubadwa zofunika malinga ndi ndime (1) zidzakhala 65 kapena zaka zilizonse zomwe Nyumba ya Malamulo ingatchule.

Koma lamulo lifuna kusintha zaka zobadwa kuti oweruza amusiyitse mpando silidzakhala ndi mphamvu yokhudza oweruzayo ngati iye adasankhidwa kale ndipo sadalibvomereza.

(7) Pulezidenti atakhutira kuti ndichokomera anthu, mwiniyo atavomera atha kumsintha munthu pa udindo wa oweruza kuti agwira ntchito ina ya Boma kwa nthawi imene pulezidentiyo anganene ndipo pa nthawi imeneypo munthuyo atha kusiya ntchito yake yoweruza, koma:

a) Ntchito inayo isatanthauze kuti wachotsedwa pa udindo wake ngati oweruza malinga ndi ndime (2);

b) Sipadzafunikanso kuti achite chomusankha kuti ayambenso ntchito pa udindo wake woweruza;

c) Kuti zifike poti apume ndi kulandira penshoni zaka zake zakubadwa zikhalebe monga ndime (1) ikutchula pokhudza oweruza.

# <u>MUTU X</u>

# OMBUDZIMANI

120.

Padzakhala mpando wa Boma umene uzitchedwa ombudzimani. Mpandowu udzakhala ndi mphamvu ndi kugwira ntchito ndi zimene udzapatsidwe ndi Malamulo ano kapena malamulo ena.

121.

Pogwira ntchiti yake ombudzimani adzachita mwa iye mwini ndipo asadzasokonezedwe ndi munthu wina aliyense kapena Gawo lina.

122.

(1) Ofuna mpandowu adzatumiza kalata kwa Mlembi wa Nyumba ya Malamulo atalengeza ndipo munthu amene adzapambane adzaikidwa pa mpandowo ndi Komiti yolemba a ntchito za Boma motsata zimene ndime inomikunenera.

(2) Munthu wosankhidwa pa mpando wa Ombudzimani:

a) Azikhala wodziwa malamulo;

b) Akhale munthu amene anthu amkhulupilira kuti angathe kugamula nkhani mosakondera;

c) Akhale wodziwa m'mene Boma limayendera;

d) Asakhale munthu woti adamangidwapo chifukwa chlakwira malamulo a Boma kapena kulowa bankalapu;

e) Akhalenso wodziwa, munthu yemwe angathe kugwira ntchitoyo;

f) Asakhale Pulezidenti, Wachiwiri kwa Pulezidenti, Nduna kapena Nduna yaing'ono wogwira ntchito za Boma yemwe sanapume kapena Phungu wa Nyumba ya Malamulo; ndipo

g) Asakhale pa mpando uliwonse wa ntchito za Boma pokhapokha ngati malamulo ano akulola.

123.

(1) Mpando wa Ombudzimani utha kufufuza nkhani iliyonse ngati munthu akudandaula kuti wazunzika popanda chifukwa ndipo pakuoneka kuti palibe chomwe angachite kuti athandizidwe podzera kubwalo loweruza, kapena pochita apilo kuchokera kwa oweruza kapena ngati palibe chithandizo china chilichonse.

(2) Ngakhale pali zomwe yanena ndime (1) mphamvu za ombudzimani pa ndime ino sizitha kuletsa ufulu umene oweruza ali nawo ndipo zimene agamula Ombudzimani a Bwalo lalikulu lamilandu ali ndi ufulu kuziyang'ananso ngati munthu wakhudzidwayo adandaula pa nkhani yomwe Ombudzimani waigamula.

124. Ombudzimani adzakhala ndi mphamvu:

a) Kuitana aliyense kuti abwere kumilandu mokakamizidwa ngati akhulupilira kuti akukhuzidwa ndi nkhani imene akuifufuza;

b) Kufunsa kuti aulule zonse zimene munthu akuzidziwa pa nkhani ndi kuti abweretse kalata za mtundu uliwonse kuchokera kuzintchito za Boma;

c) Kumufunsa munthu amene akhulupilira kuti akukhudzidwa ndi kafukufuku amene akuchitika;

d) Kuzenga munthu kapena Bungwe lililonse lonyoza Bwalo lalikulu loweruza ngati asanagonjere pa mphamvu zimene ndime ino ipereka.

125. Munthu wokhala pa mpando wa Ombudzimani:

a) Adzapatsidwa chithandizo ndi zipangizo zonse kuti athe kugwira ntchito pa udindo wake;

b) Azilandira chithandizo kuchokera kwa munthu kapena bungwe limene wapemphako chithandizo chokhudzana ndi ntchito ya mpando wake;

c) Akamagwira bntchito yake azilandira chitezo ndi ulemu umene a phungu a Nyumba ya malamulo ali nawo; ndiponso

d) Azilandira malipiro pamwezi kuchokera ku thumba lapadera *( Consolidated Fund)* ndipo ndalamazi sadzazidula popanda mwiniyo kubvomereza.

126.

Ngati kufufuza komwe Ombudzimani wachita kuonetsa umboni ndipo iye wakhutira kuti chilungamo sichinachitike, ombudzimani:

a) Angagamule choti chichitike ndi boma kuti chilungamo chioneke;

b) Angakonze njira kuti otsutsidwanso azikhala ndi chithandizo chokwanira kuti madandaulo athe;

c) Apereke nkhaniyo kwa Wamkulu nwozenga milandu ya Boma ndikumuunikira kuti atsegure mulandu ndipo ngati mkuluyo akana Ombudzimani ali ndi mphamvu yomufunsa zifukwa zokwanira.

127.

Chaka chilichonse Ombudzimani azipereka ndondomeko ku Nyumba ya Malamulo yoonetsa madandaulo amene walandira, zimene iye wachita pa zodandaulazo, chithandizo icho wapereka, komanso maganizo ake pa zodandaula anthu.

128.

(1) Munthu wosankhidwa kukhala Ombudzimani adzakhala pa mpandowo zaka zisanu, koma komiti yolemba a ntchito zaboma itha kumusankhanso kuti apitilire zaka zina zisanu ngati n'koyenera pokhapokha ngati komitiyo ithetse ntchitoyo nthawi isanakwane motsata ndime ino.

(2) Munthu osankhidwa kuti ndi Ombudzimani sadzachotsedwa pa mpando ndi komiti yolemba anthu pa ntchito za boma pokhapokha ngati:

a) Pakhale zifukwa zoonetsa kuti akadapanda kukhala Ombudzimani munthuyo sakadakwanitsa kuti asankhidwe;

b) Walakwa kwakukulu; kapena

c) Wakwanitsa zaka 65 zobadwa

# MUTU XI

# BUNGWE LOTETEZA UFULU WA ANTHU

129.

Padzakhala bungwe loteteza ufulu wa anthu *(Human Rights Commission*) limene ntchito yake yaikulu ndi kuteteza komanso kufufuza ngati ufulu umene wapatsidwa ndi malamulo ano ndi malamulo ena akuponderezedwa.

130.

Bungweli palokha kapena ngati munthu kapena gulu la anthu alipempha lili ndi mphamvu yofufuza ndikupereka maganizo ake pa njira zimene zingathandize kupititsa mtsogolo mokwanira ufulu umene malamulo ano aupereka, koma lisagwire ntchito yoweruza kapena kupanga lamulo ndipo lisapatsidwe ntchito zotero.

131.

(1) M'Bungweli mudzakhala anthu awa:

a) Munthu amene ali pa mpando wofufuzidwa ndi kukonza Malamulo;

b) Munthu amene ali pa mpando wa Ombudzimani;

Koma pokhapokha ngati kuloldwa ndi ndime ino, sipadzakhala membala wina wa Bungweli yemwe alinso wogwira ntchito za boma kapena Pulezidenti kapena wachiwiri kwa pulezidenti, nduna kapena Nduna yaing'ono kapena phungu wa ku Nyumba ya Malamulo.

(c) Enanso omwe paokha adzasznkhidwa ndi mabungwe omwe bungweli likuwaona kuti ngotchuka pa nkhani ya chitetezo cha ufulu wa anthu ndipo ntchito yawo kwakukulu ndikupititsa mtsogolo ufulu ndi mwayi wonse umene malamulo ano adzakhazikitsa.

(2) Wofufuza ndi kukonza malamuloyo ndi ombudzimani mogwirizana atomize maina a anthu olozedwa malinga ndi gawo (c) la ndime (1) kwa Pulezidenti amene adzamsankhe munthuyo kuti akhale membala wa Bungwe loyang,anira za chitetezo cha ufulu wa anthu.

(3) Mamembala a Bungweli, kupatula membala yemwe adasankhidwa malinga ndi gawo (a) kapena (b) la ndime (1), adzapitirira kukhala mamembala a Bungweli mpaka nthawi imene adzachotsedwa pa udindowu pa zifukwa izi:

a) Kusadziwa ntchito yawo;

b) Kulephera kugwira ntchito chifukwa cha zolepheretsa zina; kapena

c) Ngati pachitika zina kotero kuti ndizokaikitsa kwambiri kuti angathe kuchita chilungamoi pa udindo wake.

## MUTU XII

## BUNGWE LOONA CHILONGOSOKO CHA MALAMULO

(Law Commission)

132.

Padzakhala Bungwe limene lizisanthula malamulo ndikuikapo maganizo awo. Bungweli lidzakhala ndi mphamvu zimene malamulo ano kapena malamulo ena adzalipatsa.

133. Bungweli lidzakhala ndi mamembala awa:

a) Wamkulu wa Bungweli yemwe ntchito yake ndi yomweyo basi, wolandira malipiro apamwezi, yemwe adzasankhidwa ndi Pulezidenti atakambirana ndi Bungwe loyang'anira Ntchito za Oweruza, amene ndi katswiri wa malamulo kapena munthu amene angathe kukhala woweruza; ndiponso

b) Anthu angapo amene wamkulu wa Bungweli mogwirizana ndi Bungwe loona ntchito za Oweruza, angasankhe nthawi ndi nthawi kuti agwire ntchito monga kufunikira malinga ndi ukatswiri wawo pa malamulo amene akusanthulidwa ndi Bungweli kapena chifukwa cha ukatswiri wawo pa lamulo limene likusanthulidwanso.

134.

Pulezidenti angathe kumchotsa wamkulu wa Bungweli kapena aliyense wosankhidwa m'bungweli ngati bungwe loyang'anira ntchito za oweruza latsimikiza kuti munthuyo sadziwa ntchito yake kapena sangathe kugwira ntchitom pa udindowo pazifukwa zina.

135. Bungwe Loona Dongosolo la Malamulo lidzakhala ndi mphamvu izi:

a) Kusanthula malamulo ndi kupereka maganizo ake pa nkhani iliyonse yokhudza malamulo ano kapena malamulo okhudza maiko onse;

b) Kusanthula ndi kupereka maganizo ake pa nkhani yokhudza malamulo ano;

c) Kulandira maganizo a munthu aliyense kapena bungwe pa nkhani ya malamulo a m'dziko muno kapena malamulo ano, ndi

d) Kupereka zimene apeza pa nkhanizi kwa nduna ya chilungamo amene adzafalitsa maganizowo ndi kuwatumiza ku Nyumba ya Malamulo.

136.

Bungweli lidzagwira ntchito yake palokha popanda kuganizira za wina kapena kusokonezedwa ndi munthu kapena bungwe lililonse.

# MUTU XIII

# BWALO LOONA ZA CHIPEPESO

137.

Padzakhala bwalo loona za chipepeso lomwe lidzaunika madandaulo a anthu pa zomwe boma lidali muno m'Malawi lisanakwane tsiku lokhazikitsa malamulo ano lidawachimwila anthuwo. Bwaloli lidzakhala ndi mphamvu zimene malamulo ano kapena malamulo adzalipatse.

138.

(1) Palibe munthu yemew adzaimba mlandu Boma limene lidzakhalapo malamulo ano akayamba kugwira ntchito ngati nkhani yake ikukhudza dandaulo loti boma lakale lidamulakwira posagwiritsa bwino mphamvu kapena udindo wake, pokhapokha ngati atayamba watula dandaulo ku Bwaloli, limene lidzamve chidandaulo cha munthu wokhudzidwayo.

(2) Bwaloli lidzakhala ndi mphamvu yonse yofufuza kuti ithe kupeza zoona zenizenipa nkhaniyo.

(3) Ngakhale ndime (1) yanena moter, Bwaloli lili ndi mphamvu yotumiza nkhaniyi kumabwalo amilandu kuti mabwalo amilanduwo achitepo kanthu ngati Bwaloli lakhutira kuti lilibe mphamvu pa mlanduwo kapena laona kuti ndi chilungamo kutero.

139.

(1) Padzakhala wa pampando wa Bwaloli yemwe ndi oweruza m'Bwalo lalikulu lachiweruzo yemwe:

a) Adzasankhidwa pa udindowo ndi wamkulu wa oweruza atalozedwa ndi bungwe loyang'anira za oweruza komanso:

b) Adzakhala wapampando wa Bwaloli pa zaka zosapitilira  zitatu kapena mpaka nthawi imene adzasiye mpando wa oweruza;malinga ndi chomwe chingayambire kuchitika paziwirizi.

(2) Wapampando wa Bwaloli adzathandizidwa ndi anthu awiri opima nkhani, amene adzakhala:

a) Katswiri wa ntchito yowerengera chuma wosankhidwa ndi Bungwe  lolemba antchito za boma kuti azilondoloza  ndondomeko ya  chuma cha bwaloli, ndikupereka maganizo ake ku bwaloli pa ndalama za chipepeso chimene chingaperekedwe kwa odandaula  ataganizira  kuchuluka kwa madandaulo omwe aperekedwa  m'bwalolo, ndi ndalama zomwe zilipo m'chaka chimenecho.

b) Katswiri wa malamulo yemwe adzasankhidwa nthawi ndi nthawi pa ntchitoyi ndi komiti yolemba antchito za Boma kuti azithandiza anthu odandaula  m'bwalolo ngati alibe katswiri wa malamulo.

(3) Wopima nkhani angachotsedwe ntchito ndi komiti  yolemba antchito za boma ngati sangathe kugwira ntchito, ngati sadziwa ntchito ya udindo wake kapena ngati aononga ntchito yake kotero kuti sangathe kuchita chilungamo pa udindo wake.

140.

(1) Nyumba ya Malamulo idzakhazikitsitsa ndondomeko ya momwe Bungweli lingalondolere nkhani zonse mwansanga kuphatikizapo ndondomeko ya momwe angayendetsere chiweruzo mongogwiriziza pofuna kuti anthu ayanjane.

(2) Ngakhale pali zomwe zanenedwa mu ndime (1) dongosolo la kagwiridwe ka ntchito ya Bwaloli:

a) Ligwirizane ndi m'mene bwalo la milandu  limafunira pa umboni wakuti munthu apezeke ndi mlandu wochimwira mzake ndipo

b) Litsate dongosolo kuti chilungamo chichitike motsata malamulo ano komanso zioneke poyera kuti chilungamo chenicheni chikuchitika.

141.

Ngati munthu wapadera akutsutsa zodandaulazo kapena akukhudzidwa ndi ndalama kapena chuma chimene akuchikambira nkhaniyo m'Bwalomo:

a) Waderayo auzidwe za nkhaniyo m'nthawi yokwanira;

b) Ali ndi ufulu kuti katswiri wa malamulo amuimire pa nkhaniyo; ndipo

c) Ngati wapampando wa Bwaloli akhutira kuti munthu alibe mwayi wopeza katswiri wa malamulo womuimira , ampezere katswiri wolipidwa ndi Boma kuti amuthandize.

142.

(1) Bwalo lalikulu lamilandu sililetsedwa kugwapo kuti litsimikize ngati chilungamo chatsatidwa pa maganizo a bwalolo, komanso Bwalo lona za chipepeso likagamula nkhani sindite kuti litsekereze mlandu wopempha malipiro kapena kuti wina alangidwe m'bwalo la milandu kwa nthawi imene thumba la chipepeso likugwirabe ntchito.

(2) Kumene kuti "Munthu Wamba" pa ndime ino kutanthauza munthu amene adali m'boma kapena wotumikira ntchito ya boma malamulo ano asakhazikitsidwe, amene malinga ndi malamulo a pa nthawoyo akadakhala ndi mlandu payekha chifukwa chakuchita zinthu zodzetsa mlandu woti alipire kapena kuti amangidwe.

143.

Kuti pakhale chithandizo pa nkhani yofika ku bwaloli komanso pa mlandu umene uli pa ndime 142(2) bwaloli kapena bwalola milandu lililonse litha kuyamba laiwala za malamulo otseka mlandu chifukwa chakuti nthawi idatha, ngati kuteroko kungathandize kuti chilungamo chenicheni chichitike.

144.

(1) Padzakhazikitsidwa Thumba la ndalama zapadera la chipepeso limene lizisungidwa ndi Boma m'malo mwa anthu.

(2) Thumbali lidzagwiritsidwa ntchito pa nkhani zokhazo zonse zingafike malingandi malamulo ano ndipo;

a) Ndalamazo zidzasamalidwa kuti zithandize anthu okhawo omwe adandaula ku Bwalo loona za chipepeso omwe chiweruzo cha bwalolo chawapatsa ndalama, penshoni kapena chiuongoladzanja cha mtundu uliwonse motsata dongosolo la kayendetsedwe ka zinthu m'bwalolo;

b) Lisungidwe padera kuti banki yaikulu ya Malawi (Reserve Bank of Malawi) ndipo

c) Lisungidwe ndondomeko zonse komanso za ndalama zokhudza ntchito ya m'Bwalolo ndikuzisamala kuti zisataike kapena kubedwa.

(3) Motsata ndime ino ndalama zochotsa kapena kapena kulipira kuchokera ku Thumba la Bwalo zikhale zolamulidwa ndi:

a) Bwalo Loona za Chipepeso;

b) Gulu lokhazikitsidwa kuti lisunge Thumbalo m'malo mwa bungwelo ngati ndalama zochotserazo ndi zofunika kuti thumbalo ligwire ntchito yake bwino motsata chifukwa chimene chikutchulidwa pa ndime ino.

(4)

Pazikhala gulu la anthu asachepera anayi osunga Thumbali limene lidzasankhidwa nthawi ndi nthawi ndi komiti yolemba a ntchito za Boma motsata malangizo a Bungweli.

(5) Anthu osunga Thumbali adzagwira ntchito yao mpaka Thumbalo litatha ntchito yake pokhapokha ngati atachotsedwa ndi komiti yolemba a ntchito za Boma malinga ndi malangizo awo ngati:

a) Sakutha ntchito;

b) Sangathe kugwira ntchito; kapena

c) Pachitika china kotero kuti sangathenso kukhulupirika pa nkhani ya ndalama.

(6) Komiti yosunga Thumba la Bungwe idzagwira ntchitoyo payokha popanda kusokonezedwa ndi munthu kapena bungwe lililonse pokhapokha ngati ndime ino italola.

(7) Wamkulu wofufuza za kayendetsedwe ka Ndalama za Boma (Audito General) adzapereka ndondomeko ku Nyumba ya Malamulo yolongosola za m'mene

Thumbalo lagwira ntchito chaka ndi chaka ndipo ndondomeko idzathandiza Nyumba ya Malamulo pogawa ndalama zoti zigwire ntchiti ya Bwaloli.

(8) Nduna ya zachuma idzapereka maganizo ake ku Nyumba ya malamulo pa za ndalama zofunika ku thumba la Bwaloli pasanafike chaka chatsopano cha kayendetsedwe ka ndalama za Boma kwa nthawi imene Thumbali lizigwira ntchito.

(9) Chaka ndi chaka malinga ndi kayendetsedwe ka ndalama za boma bwaloli lidzagawa nthawi yosabzyolera miyezi m'chaka chimenecho kuti pakatha nthawiyo asalandirenso pempho kapena dandaulo lofuna chithandizo kuchokera ku Thumbali m'chaka chimenecho.

145.

(1) Thumbali silidzakhudzidwa ndi madandaulo atsopano opempha chithandizo zikadzatha zaka khumi kuchokera pamene malamulo ano adzakhala akugwira ntchito ndipo Bwaloli adzalithetsa ikadzangokwana nthawi imeneyo.

(2) Ngati chaka chitakakha ndipo m'chaka chachiwiri pali madandaulo ochepera pa khumi opita ku Bwaloli adzalithetsa ikadzangokwana nthawi yomwe yatchulidwa pa ndime (1) wapampando wa Bwaloli atha kufunsa nduna ya zachuma kuti apereke bilo m'Nyumba ya Malamulo;

a) Kuthetsa Bungwe Loona za Chipepeso; ndi

b) Kupatsa mphamvu zofanana ndi za Bwalolo ku Bwalo lalikulu la milandu kuti lizithandiza pa madandaulo ofuna chipepeso ku Boma monga momwe mutu uno ukunenera

*(3)* Ngati bwaloli lathetsedwa , kwa nthawi yotsalayo malinga ndi mmene ndime (1) ikunenera , ndalamazokhalako kuthumbalo zisungidwebe padera m'chiwerengero cha Thumba la Boma lapadera (*Consolidated Fund)* limene nduna ya za chuma ingathe kutapamo kuti ilipire anthu omwe anadandaula ku Bwalo la Pamwamba la Milandu pa nkhani yomwe ikadakambidwa ndi Bwalo loona za chipepeso.

*(4)* Thumbali lidzapitirira mpaka ndalamazo zitatha kugwira ntchito.

# MUTU XIV

# MABOMA AANG'ONO

146.

(1) Padzakhala mabungwe a maboma aang'ono amene adzakhala ndi mphamvu zopatsidwa ndi malamulo ano kapena malamulo ena.

(2) Mabungwe adzakhala ndi udindo woimira anthu amene ali m'madera mwawo pa nkhani za chitukuko chawo ndipo adzakhala ndi udindo wa:

a) Kupititsa mtsogolo ntchito za misewu ndi milatho, komanso zonse zokhudza chitukuko cha chuma pokonza ndikugwiritsa ntchito chikonzero cha chitukuko komanso polimbikitsa pa ntchito za malonda ndi zamanja;

b) Kutula ku Boma ndondomeko ya chitukuko m'madera ndikuona kuti anthu akudziwitsa boma zofunika m'madera mwao;

c) Kulimbikitsa ndi kupititsa mtsogolo mabungwe athandiza anthu kuti azidzichitira mogwirizana komanso akhale ndi mchitidwe woti anthu osiyana maganizo azigwirizana ntchito pamodzi; ndi

d) Kuchita ntchito zina zilizonse kuphatikizapo kaundula wa ana wobadwa ndiponso wa anthu omwalira, komanso kugwapo pa ntchito zothandiza anthu kuti akhale ndi zinthu zowathandiza m'madera mwawo monga malamulo anenera

(3) Nyumba ya Malamulo ngati kungatheke ikonze mfundo kuti nkhani zokhudza madera ndi m'mene zingayendere zizikambidwa ndi kugamulidwa ndi anthu eni m'madera awo motsata chithandizo cha mabungwe a maboma aang'ono;

(4) Nyumba ya Malamulo ionetsetse kuti mkati mwa nthumwi za mabungwe amaboma aang'ono mudzikhalanso mafumu a m'madera a maboma aang'ono ndi kuti nthumwi zake zither kupatsa anthu mwayi wokwana kuti awaimire m'madera mwawo ndipo malire amaderawo akhazikitsidwe ndi bungwe loyendetsa chisankhom motsata ndime 148.

147.

(1) M’mabungwe a maboma aang’ono muzikhala makhansala amene adzasankhidwa mwaufulu pa chisankho chakadziwamwini chokhudza anthu onse omwe ali mkaundula wa voti, motsata malangizo a Bungwe loona za chisankh, m’dera limene bungwelo lili ndi mphamvu.

(2) M’mipando ya maboma aang’ono muzikhalanso mfumu za mizinda  ndi matauni ang’onoang’on, ndiponso makhansala m’madera onse ndipo akuluakuluwa azikhala ndi ntchito, mphamvu ndi udindo monga momwe malamulo anenera.

(3) Pa bungwe lililonse la maboma ang’ono padzakhalanso ogwira ntchito za Boma oansi pa akuluakuluwo monga momwe zingafunikire, kuti atendetse ndi kukonza ntchito zochitika  ndiponso mfundo zimene akuluakuluwo angagwirizane.

(4) Padzakhala Bungwe loyang’anira ntchito za Maboma aang’ono. Nthumwi za Bungweli ntchito, mphamvu ndi kayendetsedwe kache, zonsezi zidzalongosoledwa ndi malamulo.

148.

(1) Padzakhala malire amadera  a maboma aang’ono amene adzalembedwa motsata malangizo a Bungwe Loona za Chisankho pansi pa Malamulo ano kapena malamulo ena okhudza chisankho cha anthu onse;

(2) Malirewo adzakhudza mitunda basi osaganizira za mtundu wa munthu kapena khungu, kapena kumene munthuyo adachokera.

149.

(1) Padzakhala komiti ya Dziko yoona za Ndalama za Maboma Aang’ono imene idzalandira mapempho kuchokera ku maboma aang’ono okhudza ndalama zogwirira ntchito yawo kapena ntchito zapadera ndipo idzakhalanso ndi udindo umene ingapatsidwe ndi Malamulo ano kapena malamulo ena.

(2) Komoti idzakhala ndi mphamvu:

a) Kulandira dongosolo la ndalama zofunika komanso zimene zingafunike kuchokera kumaboma aang’ono;

b) Kuyang’anira ndi kuona ngati mabuku a ndalama za maboma aang’ono akusungidwa bwino motsata malamulo komanso mogwirizana ndi malangizo amkulu woona chilongosoko cha ndalama za boma.

c) Kupereka maganizo ake pakagawidwe ka ndalama ku maboma aang'ono, komanso kusintha m'mene ndalamazo zikugawidwira poganizira za chuma, mitunda ndikuchuluka kwa anthu;

d) Kukonza ndondomeko ya ndalama zofunika ndi maboma aang'ono onse, itakambirana ndi a ku Unduna wa za Chuma kuti Nduna ya Maboma Aang'ono izitumiza ku Nyumba ya Malamulo chaka cha ndalama chisanayambe, ndi

e) Kupempha chionjezero cha ndalama kwa Ndunayo ngati n'kofunika.

150.

Boma lili ndi udindo kuonetsetsa kuti pali chikonzero cha ndalama chokwanira kuti maboma aang'ono agwire ntchito yawo bwino ndipo maboma aang'ono aloledwe kusunga gawo lina la ndalama zomwe amazipeza monga momwe komiti ya za chuma cha maboma aang'ono ingakonzere.

151.

(1) Nthumwi zakomiti yoona ndalama za maboma aang'ono ndi:

a) Munthu m'modzi wosankhidwa nthawi ndi nthawi kuti aimire Boma pa msonkhano wa maboma aang'ono;

b) Mlembi wa Unduna wa Maboma aang'ono;

c) Munthu m'modzi yemwe ndi katswiri pa ntchito yowerengera ndi kufufuza za ndalama wosankhidwa ndi komiti yolemba ntchito anthu a m'Boma motsata malangizo a Nduna yoyang'anira Maboma Aang'ono.

d) Wapampando wa Bungwe lolemba a ntchito ya Boma kapena membala m'modzi wa Bungweli amene adzasankhidwa ndi wapampandoyo kuti azimuimira nthawi ndi nthawi; ndiponso

e) Munthu m'modzi wosankhidwa ndi Bungwe Loona za chisankho nthawi ndi nthawi.

(2) Kupatula anthu amene ali membala kapena amene angakhale membala wa komitiyichifukwa cha mpando wa mlembi wa Maboma ang'ono kapena wa pa mpando wa bungwe loona za Ogwira ntchito za boma mamembala a komiti ya za chumawo adzasiya ntchito zaw:

a) Patapita zaka zitatu kuchokera pamene membalayo adasankhidwa;

b) Atachotsedwa ndi Pulezidenti potsata malangizo a Komiti Yolemba Antchito za Boma koma palibe membala yemwe adzayang'anire; kuti amchotse ntchito motsata ndime iyi pokhapokha Komiti Yoona Ogwira Ntchito za Boma ikhutire kuti:

   (i) Munthuyo sakukwanitsa kugwira ntchito paudindo wake;

   (ii) Pali zina zolakwika kotero kuti sangakhulupirikenso pankhani ya ndalama, kapena

   (iii) Sangathe kugwira ntchito pa zifukwa zina.

# MUTU XV

# APOLISI

152.

Pazikhala gulu la a Polisi lokhazikitsidwa ndi malamuloamene adzalongosola magawo osiyanasiyana ndi ntchito zawo m'gulu la a Polisi

153.

(1) Gulu la a Polisi lidzakhala ndi nthambi yoima payokha ya gawo la mutu wa Boma ndipo lidzakhala ndi ntchito yachitetezo ndikuona kuti anthu pamodzi ndi zinthu zawo zonse akukhala pamtendere monga m'mene Malamuklo ano ndi ena akunenera.

(2) Gulu la a Polisi lidzakhala ndi mphamvu zokhazo zimene ndi zofunika kuti atetezere nazo ufulu pansi pa Malamulo ano ndiponso kuti bata ndi mtendere zipitirira motsata zomwe malamulo ano komanso malamulo ena anenera.

(3) Pogwira ntchito yawo mamembala a Gulu la a Polisi adzakhala pansi pa ulamuliro waoweruza ndipo adzamvera ulamulirowo

(4) Udindo woyang'anira gulu la a Polisi kun dale udzakhala m'manja mwa Nduna ya Boma imene idzaonetsetsa kuti luntha ndi mkhalidwe wa gulu la a Polisi zikugwirizana ndi m'mene malamulo ano komanso malamulo ana akunenera.

154.

(1) Padzakhala wamkulu oyang'anira a Polisi amene adzakhala Mutu wa Gulu la a Polisi m'Malawi ndipo ntchito yake idzakhala yotumikira boma. Iyeyo adzayang'aniridwa ndi Nduna yoyang'anira a Polisi yemwenso adzakhala wotumikira Boma.

(2) Wamkulu woyang'anira a Polisi adzasankhidwa ndi Pulezidenti ndikubvomerezedwa ndi Nyumba ya Malamulo motsata anthu amene achuluka pa voti ya nthumwi izo zilipo ndipo zachita nawo voti koma komiti yolemba antchito za boma ingathe nthawi ina iliyonse, kufufuza ngati munthu wosankhidwayo angathedi kugwira ntchito ya udindowo ndikufunsa zina zimene zikhudzana ndi kagwiridwe ka ntchito pa udindowo.

(3) Mpando wa Wamkulu Woyang'anira a Polisi udzakhala opanda munthu ngati mwini mpandowo wagwira ntchito zaka zisanu, koma athabe kusankhidwa kachiwiri kuti agwirenso ntchitoyo pa zaka zpsapitirira zisanu zina monga momwe Pulezidenti angafunire.

(4) Wamkulu Woyang'anira a Polisi atha kuchotsedwa ndi Pulezidenti pa zifukwa zokha zoti munthuyo:

a) Sakukwanitsa kugwira ntchito ya udindo wake;

b) Paoneka kapena pachitika zina kotero kuti nkokaikitsa kwambiri ngati angathe kugwiritsa ntchito mphamvu za udindo wake mosakondera;

c) Sangathe kugwira ntchito pazifukwa zina, ndi kuti

d) Wakwanitsa nthawi ya kuti azilandira penshoni.

(5) Motsata ndime (4) pogwira ntchito ndi kugwiritsa ntchito udindo wake wamkulu woyang'anira a polisi adzagwira ntchitoyo mwayekha ndipo saloledwa kulamulidwa ndi munthu kapena bungwe lina kupatula mmene malamulo ano kapena malamulo ena anganenere.

(6) Wamkulu Woyang'anira a Polisi angathe kupereka ku Bungwe, kapena kwa munthu wina aliyense,m'polisi momwemo, mphamvu zimene iye ali nazo, malinga ndi malamulo ano,monga momwe angaganizire.

(7) Pogwiritsa ntchito mphamvu zonse malinga ndi ndime ino, Wamkulu Woyang'anira a Polisi adziwitse Bungwe Loyang'anira Ogwira Ntchito ya Polisi kuti wapereka mphamvuzo ndipo Bungwelo likonze ndondomeko zofunika pakayendetsedwe ka ntchitoyo kuti igwirike bwino motsata ndime ino ndiponso mogwirizana ndi malamulo,

155.

(1) Pazikhalanso Bungwe Loyang'anira Ogwira Ntchito Polisi omwe likhale ndi mphamvu komanso ntchito yopatsidwa ndi malamulo ano kapena malamulo ena opangidwa ndi Nyumba ya malamulo.

(2) Kupatula m'mene malamulo ano anganenere, mphamvu yosantha anthu pa maudindo kapena kugwirizira m'Gulu la Polisi, (kupatula udindo wa wamkulu woyang'anira apolisi) kuphatikiza kukhazikitsa munthu pa ntchitozo, komanso mphamvu yochotsa munthu pantchitoyo, idzakhala m'manja mwa Bungwe Loyang'anira za Ogwira Ntchito za Polisi.

(3) Bungweli lili ndi udindo wokhazikitsa mwambo pa onse wogwira kapena kugwirizana ntchito zimene zikhudzidwa ndi ndime ino, koma motsata malamulo ano kapena malamulo ena.

156.

(1) Bungweli lingathe motsata zomwe zingafunike ndi malamulo kupereka mphamvu zimene malamulo ano kapena malamulo ena apereka mchikalata kwa munthu aliyense m'Bungweli kapena kwa anthu ogwira ntchito ya Boma kapena ku bungwe la Boma.

(2) Pamene munthu kaya ndi bungwe akugwira ntchito motsata ndime (1) yaing'ono m'malo mwa bungwe Loyang'anira Ntchito za Poliisi Bungweli.

a) Lidzaonetsetsa kuti munthuyo kapena bungwelo akutumiza malipoti monga momwe bungwelo lingafunire m'chikalata chimene chidapereka mphamvuzo ndiponso;

b) Lidzamva madandaulo kapena apilo kuchokera kwa anthu amene akhudzidwa ndi momwe mphamvuzo akuzigwiritsa ntchito malinga ndi ndime ino, ndipo lidzakhala ndi mphamvu:

(i) Kuchotsa mfundo imene munthu wopatsidwa ntchito adaigamula pogwira ntchitoyo;

(ii) Kugwiritsantchito yokhazikitsa mwambo kukhudza munthuyo kapena bungwelo, motsata mmene malamulo angafunire; ndiponso

(iii) Kulanda munthuyo kapena bungwelo mphamvu zimene adapatsidwa; koma palib chilichonse pa ndime ino chimene chingaletse ufulu wa munthu amene wakhudzidwa ndi zimene za lamulidwa kapena kuchitika mdzina la Bungweli kuti achite apilo ku Bwalo Lalikulu la milandu kapena kuchotsa ufulu wa munthu amene akukhuzidwa ndi mfundo ya bungweli kuti apemphe bwalo lalikulu la milandu kuti liunikenso ngati mfundoyo igwirizana ndi chilungamo chenicheni.

157.

(1) M'bungweli mudzakhala mamembala awa:

a) Owerza m'Bwalo Lalikulu la Apilo kapena m'Bwalo Lalikulu la Milandu angasankhidwe m'nthawiyo ndi Bungwe  Loona za chiweruzo, amene adzakhala Wapampando wa Bungwelo;

b) Membala wa Bungwe  Loona za Ogwira Ntchito za Boma amene wasankhidwa pa nthawiyo ndi Bungwelo kuti aziimilira;

c) Wamkulu woyang'anira a polisi kapena Wamkulu wina aliyense m'Gulu la a Polisi amane angatchulidwe ndi Wamkulu woyang'anira aPolisi kuti azimuimira;

d) Ombudzimani; ndi

e) Katswiri wamalamulo amene angathe kusankhidwa nthawi ndi nthawi ndi Pulezidenti natsimikizidwa ndi komiti yolemba ogwira ntchito za boma.

(2) Anthu atatu aliwonse ndiwo angathe kuyamba zokambirana m'Bungweli.

(3) Munthu yemwe ndi Pulezidenti, nduna kapena Nduna yaing'ono, Phungu wa Nyumba ya Malamulo, kapena wamkulu m'Polisi saloledwakusankhidwa ngati membala wa Bungweli.

(4) Kupatula momwe ndime ino inganenere mpando wa membala wa Bungweli udzakhala wopanda munthu:

a) Pakatha zaka zitatu kuchokera pa tsiku limene munthuyo adamusankha pokhapokha ngati wasankhidwanso kwa zaka zina zitatu.

Koma ndime ino sidzagwira ntchito ngati membalayo akadali pa mpando wa Wamkulu Woyang'anira a polisi kapena wa Ombudzimani kapena mpando wina ulionse ukamthandiza munthuyo kuti asankhidwekukhala m'Bungwe loyang'anira Ogwira Ntchito za Polisi, kapena

(c) Pakachitika zina ndi kuti ngati munthuyo sakadakhala membala wa Bungweli ndiye kuti sakadaloledwa kuti asankhidwe choncho.

158.

(1) Mamembala a Gulu la a Polisi aonetsetse kuti akugwira ntchito yawo, komanso kuti akugwiritsa ntchito mphamvu ndi udindo wawo, mosakondera popeza iwowa ndi a ntchito za Boma otumikira anthu wamba ndiponso Boma limene lingakhalepo.

(2) Membala wa Gulu la a Polisi saloledwa kuchita nawo ndale za dziko:

a) Koma membala aliyense wa Gulu la a Polisiali ndi ufulu kutula pansi ntchito yake kuti azichita nawo za ndale;

b) Palibe chilichonse pa ndime ino chimene chingakhale chosayenera kwa membala wa Gulu la Polisi yemwe ali ndi ufulu wonse kuti achite voti motsata malamulo ano; ndipo

c) Sitchimo kumbali ya membala wa Gulu la a Polisi ukhala pampando kapen membala wa Bungwe lililonse, gulu kapena gulu la anthuamene amagwira ntchito ya ukatswiri, ngati cholinga chake chenicheni ndi kuimira zofuna za mamembala za mmene aziwasamalira panthitopo kapena kungokhala nawo pagululo ngati m'modzi mwa a katswiri kuti zao zipite mtsogolo; koma sikuloledwa kulowerera pa ndale za zipani, kapena kampeni kapena kupititsa mtsogolo maganizo otsutsana ndi ntchito za Gulu la a Polisi.

(3) Palibe Boma kapena chipani chimene chiloledwa kuuza membala wa Gulu la a Polisi kuti agwiritse ntchito, mphamvu kapena udindo wake popititsa mtsogolo kapena kupondereza zofuna kapena zochitika za chipani cha ndale kapena za munthu aliyense mchipanicho ndiponso sikuloledwa kuti membala wa Gulu la a Polisi, ngati

msilikali, azichita zokondera kapena zopysinja chipani, kapena membala wa chipani chilichonse.

(4) Palibe Boma kapena chipani cha ndale chomwe chingauze membala wa Gulu la a Polisi, pa udindo wake ngati msilikali, kuti agwiritse ntchitochuma cha Boma, ndalama, katundu kapena anthu amene kuti apititse mtsogolo kapena kupysinja chipani cha ndale chilichonse kapena membala wake kapena Gulu, ndipo sikuloledwa kuti membala wa gulu la a Polisingati msilikali agwepo pa nkhani yotere:

Koma malinga ndi ndime ino, sikulakwa ngati wa polisi pa udindo wake agwapo poteteza, kapena kutchinjiriza ufulu wa zipani zonse za ndale, anthu kapena magulu mosakondera, mosaopa, motsatira malamulo ano kapena malamulo ena.

(5) Membala wa Gulu la a Polisiyemwe alakwira ndime ino adzalandira chilango chomwe Bungwe Loona za Gulula Polisi liganize kuti ndichoyenera mogwirizana ndi kukula kwa nkhaniyo koma motsatamala,mulo amene adzakhazikitsidwa ndi Nyumba ya Malamulo.

(6) Ngati Bungwe Loyang'anira za a Polisi likhutira kuti Boma kapena chipani cha ndale kapena membala wa chipani cha ndale walakwira ndime (3) Bungwelo lingathe kutsegula mlandu ku Bwalo Lalikulula Milandu kuti wolakwayo alandire chilango ndipo ngati nkhani yake ikhudza ndime (4) kuti abweze chuma kapena ndalama zofanana ndi zimene adagwiritsa ntchito kuchokera ku Boma, chipani cha ndale kapena membala wa chipani chandale amene wapeza thandizo mosayenera monga momwe nkhaniyo ingakhalire.

# <u>MUTU XVI</u>

# GULU LA NKHONDO

159.

Sikuloledwa kukhala ndi gulu lankhondo lina muno m'Malawi kupatula Gulu la Asilikali a nkhondo la Malawi limene lidzakhala motsata mutu uno.

160.

(1) Gulu la Asirikali a Nkhondo lidzagwira ntchito nthawi zonse motsata malamulo a Boma la anthu wamba amene apatsidwa mphamvu ndi Malamulo ano; ndipo

a) lidzaonetsetsa kuti Malawi ndi dziko palokha ndi malire akeake ndipo lidzateteza nzika zake ku chiopsezo ndi zida za nkhondo kuti nzikazo zizikhala pa mtendere;

b) lidzasunga ndi kuteteza ulamuliro wa dziko la Malawi ndi kuthandiza mabungwe aulamuliro kuti agwire ntchito zawo bwino motsata Malamulo ano;

c) lidzapereka ukatswiri ndi zonse zothandiza ku mabungwe a anthu wamba posunga ntchito zofunikira nthawi yoti zinthu zagwa mwadzidzidzi; ndipo

d) lidzagwira ntchito kunja kwa dziko la Malawi monga kungafunikire malinga ndi pangano limene Boma libvomereza motsata malamulo obvumerezedwa ndi mayiko onse.

(2) Palibe munthu kapena bungwe limene lingalamule kapena kutula gulu la Asilikali Ankhondo kuti lichite chinthu motsutsana ndi malamulo ano

161.

(1) Udindo waukulu pa Gulu la Asirikali a nkhondo muno m'Malawi udzakhala m'manja mwa Pulezidenti amene adzakhala wamkulu wolamulira.

(2) Mphamvu zonse zimene zili ndi Pulezidenti malinga ndi mutu uno zidzagwiritsidwa ntchito molangizidwa ndi Bungwe la Asilikali Ankhondo *(Army Council)* linene lidzakhazikitsidwa motsata malamulo ndipo m'Bungwemo mudzakhala nduna ya Zachitetezo ndiponso Akuluakulu olamulila Asirikali m'Malawi *(High Command)* ndipo lidzakhala ndi:-

a) mphamvu zogamula mmene gulu la nkhondo lingagwiritsidwire ntchito m'Malawi;

b) mphamvu zosankha kapena kuchotsa pa mpando akuluakulu ankhondo ndi mamembala a gulu la a nkhondo m'Malawi; ndiponso

c) mphamvu zina ndi udindo monga m'mene malamulo anganenere.

(3) Mphamvuzonse zopatsidwa ndi ndime (2) zidzagwira ntchito mounikidwa

ndi komiti ya chitetezo yomwe idzakhazikitsidwa ndi nyumba ya malamulo monga momwe ndime (162) ikunenera.

(4) Bungwe la Asirikali an Nkhondo lingathe, polemba m'chikalata, koma motsata mfundo zimene zingapatsidwe ndi lamulo kapena kukhazikitsidwa ndi nyumba ya Malamulo molangizidwa ndi Komiti ya Chitetezo, kupatsa membala aliyense wa Gulu la Ankhondo mphamvu zimene zapatsidwa ku Bungweli ndi malamulo.

(1) Padzikhala Komiti ya Nyumba ya Malamulo yoona za, chitetezo imene idzaimira zipani za ndale moyerekeza kuchuluka kwawo m'Nyumbayo, ndipo idzakhala ndi mphamvu ndi ntchito monga momwe angapatsidwe ndi malamulo ana kapena malamulo ena.

(2) Komiti yoona za chitetezo itha kuitanidwa kuti ikumane nthawi ina iliyonse ngakhale kuti Nyumba ya Malamulo siikukumana, ndipo ngati Nyumbayo adathetsa, Komiti iyi idzapitirirabe Mpaka Nyumba ya Malamulo yatsopano idzakumane ndipo Komiti yatsopano yoona za chitetezo idzasankhidwenso, koma kupatula apo, palibe membala yemwe adzakhala pa mpando kubyzolera chaka chimodzi.

# MUTU XVII

# NDENDE ZA BOMA

163. Gawo la Ndende za Boma ndi malo ena onse osungira akaidi, malo ogwiritsa anthu chibalo, sukulu zapadera zophunzitsirako ndi malo ena osungirako anthu olakwira malamulo, koma siliphatikiza malo amene amasungira anthu amene asanawaimbe mlandu ku Polisi.

164.

(1) Padzakhala Wamkulu Woyang'anira Ndende yemwe adzayendetsa ntchito za ndende ndipo adzakhala wa ntchito za Boma nakhala ndi mphamvu ndi udindo wogwirira ntchito zimene adzapatsidwe ndi . Malamulo ana komanso malamulo ena.

(2) Udindo waukulu wa Wamkulu woyan'gani Ndende udzakhala kuonetsetsa kuti ndende za Boma zonse zikugwiritsidwa ntchito bwino ndi moyenera motsata:-

a) chitetezo chaufulu ndiponso za m'Malamulo ana kapena zopezeka m'malamulo ena;

b) malangizo a Bungwe Loona za Ndende z a. Boma, komanso a Woyang'anira ndi kuyendera Ndende monga momwe malamulo
akufunira; ndiponso

c) malamulo a oweruza anthu amene apezeka ndi mlandu m'bwalo nalamulidwa kuti akasungidwe ku ndende,' kapena asungidwe ndi bwalolo mpaka chilango chitaperekedwa, kapena wodikira kuti bwalo la milandu ligamule mlanduwo, kapena omwe asanazengedwe mlandu ndipo ali m'dende kukasungidwa m'malo mwa ndende ndi a Polisi monga mwa lamulo lililonse.

(3) Kupatula zimene ndime inn inena, pogwiritsa ntchito udindo kapena
mphamvu zimene Malamulo ana kapena malamulo ena apereka, Wamkulu Woyang'anira Ndende za Boma sadzamvera munthu aliyense kapena Bungwe lina lililonse, koma Malamulo ana ndi malamulo ena.

I

165.

(1) Wamkulu oyanganira ndende angathe kupereka mphamvu zimene
zapatsidwa kwa iye ndi malamulo ana kapena malamulo ena kubungwe kapena kwa munthuwina aliyense mmene angaonere, ngati munthuyo kapena bungwelo ndi mbali imodzi ya anthu ogwira nchito za ndende.

(2) Pokhudza mphamvu zopatsidwa kwa wina malinga nid ndime (1 ):-

a) Wamkulu Woyang'anira Ndende awauze a Bbungwe loona za ndende za boma komanso Woyang'anira ndi Kuyendera Ndende nkhani yoti wagawirako ena nchitoyo; ndipo

b) Sungwe Loona za Ndende kapena woyang'anira ndikuyendera Ndende monga zingakhalire angathe:-

c) Kukonza ndondomeko zimene aganiza kuti ndi zothandiza pa mmene apatsidwa mphamvuwo adziperekera malipoti; ndipo

ii) akhazikitsenso malire omwe angafunike omwe poonetsetsa kuti mphamvu zopatsidwazo aziyendetse bwino.

166.

(1) Wamkulu Woyang'anira Ndende za Soma adzasankhidwa ndi President,
koma Komiti yolemba Anchito za Soma ili ndi ufulu nthawi ina iliyonse, wofufuza ngati munthu wasankhidwayo angathedi kudgira nchitoyo kapena kufunsa zina zomwe zikukhudzana ndi kagwiridwe kanchito malinga ndi udindowo.

(2) Mpando wa Wamkulu Woyanganira Ndende za Soma udzakhala
wopanda munthu ngati munthuyo wagwira nchito zaka zisanu, koma atha

kumusankhaso munthuyo kuti apitilize kwa zaka zina zosabzyola zisanunso monga momwe Pulezidenti angafunire.

(3) Munthu yemwe ndi Wamkulu Woyang'anira Ndende za Soma angathe kuchotsedwa ndi Pulezidenti pazifukwa izi basi:-

a) Ngati munthuyo sadziwa nchito;

b) Ngati pataoneka kapena ~uchitika china, kotero kuti anthu sangakhulupilire kuti n'kutheka kugwira nchito yake mosakondwera;

c) Ngati sangathe kupiliza pazifukwa zina; kapena

d) Ngati wakwanitsa zaka zoti apume pa nchito.

167.

(1) Padzikhala bungwe loona za ndende Iza boma limene Iidzakhala ndi mphanvu ndi nchito zopatsidwa ndi malamulo ano ndiponso malamulo ena.

(2) Bungwe lidzakhala ndi mphamvu yosankha anthu oti akhale pa maud indo a ndende za Boma, kupatula Wamkulu woyang'anira ndende za Boma, mphamvu zimene zikuthandizanso kuti angathe kukhazikitsa munthu pa udindo waake ngati nthawi yongoyembekezera yatha, komanso kumchotsa pa udindo.

(3) Bungvve Iidzagwira ntchito yosungitsa mwambo pa anthu omwe akugwira nchito monga ndime ino inenera motsata Malamulo ano ndi Malamulo ena.

4) Bungwe lingathe, mosamala momwe Malamulo angatsimikizire, mphamvu zimene zili nazo malinga ndi mmene ndime ino inenera, mchikalata, kwa membala wa Bungweli, kapena Wamkulu wantchito za Boma kaya Bungwe lina, ngati amenewa ali mbali imodzi ya gawo la Ndende za Boma

5) Ngati munthu kapena bungwe ligwira nchito potsata ndime m'malo mwa Bungwe Loona Ndende za Boma, nthawi ndi nthawi mogwirizana ndi ndime (4) yaing'ono, Bungweli:-

a) Lionetsetse kuti munthuyo kapena Bungwelo, akupereka malipoti monga momwe bungwe lidanenera mchikalata chomwe lidaperekeramo mphamvuzo;

b) Lilandire dandaulo kapena apilo yochokera kwa munthu aliyense akhudzidwa ridi mphamvu zopatsidwa ndi ndime ino, ndipo lidzakhala ndi mphamvu:-

i) yochotsa zimene munthu kapene bungwe lagamula pogwiritsa nchito mphamvuyo;

ii) yokhazikitsa mwambo pamunthuyo kapena Bungwelo motsata Malamulo;

iii) yolandanso mphamvu zomwe zidapatsidwa kwa munthuyo kapena bungwelo.

Koma, palibe chilichonse mundime ino chimene chingamuletse munthu yemwe wakhudzidwa ndi nkhani imene yagamulidwa mopatsidwa mphamvu ndi bungwe kuti achite apilo kubwalo lalikulu la milandu kapena kulanda ufulu wa munthu wokhudzidwa kuti apite ku Bwalolo ndi kupempha kuti aunikenso nkhaniyo ndikuona ngati adaigamula motsata chilungamo chenicheni.

168.

(1) Bungwe loona za ndende zabomalidzakhala ndi mamembal awa :

a) Oweruza mbwalo lapamwamba la apilo kapena oweruza m'bwalo lalikulu la milandu amene azisankhidwa ndi bungwe loona za loweruza, yemwe adzakhala wapampando;

b) Membala wa bungwe loona anchito za boma wasankhidwa ndi bungwe lawolo, kuti aziwaimila;

c) Katswiri wa malamulo wosankhidwa ndi president ngati wovomerezedwa ndi komiti yolemba anthu anchito za boma ;

d) Munthu yemwe azasankhidwa nthawi ndi nthawi ndi bungwe loyendera ndende kuti aziwaimila ndipo

e) Wamkulu ayang'anira ndende kapena munthu wosankhidwa ndi wamkuluyo kuti amuimire yemwe ndi mmodzi mwa akulu akulu agwira nchito mndende za boma.

(2) Munthu saloledwa kusankhidwa ngati membala wa gawo loona za anthu ogwira nchito za ndende za boma ngati ndi presiden, wachiwiri wake, nduna nduna yaing'ono, kapena phungu wa nyumba yamalamulo.

(3) Kupatula monga momwe ndime ino inganenere, udindo wa membala wa bungweli udzatha.

a) Pakatha zaka zitatu kuchokera patsiku Iimene adasankhidwa,pokha pokha ngatiwasankhidwaso kwa zaka zina zitatu, kapena:-

b) Ngati paoneka kapena kuchitika china kotero kuti akadakhal kuti si membala, munthuyo sakadatha kusankhidwa ngati membala, wa bungwe loona zanchito za ndende:-

Koma ndime (a) siizagwira nchito ngati membalayo akadali pampando wa wamkulu wamkulu oyanganira za nchito za ndende za boma ndipo ngati anasankhidwa mbungwemo chifukwa cha mpandowo.

169.

(1) Padzakhala Bungwe Loyendera Ndende limene lidzakhala ndi mphamvu, nchito ndi udindo zokhudza ogwira nchito m'Bungwe la za Ndende monga m'mene Malamulo ana kapena Malamulo ena akunenera.

(2) Bungwe lidzagwiritsa ntchito mphamvu, ndi udindo wake mwa ilo lokha mosatumikira munthu wina kapena bungwe lina.

(3) Bungweli-

a) Lidzaonetsetsa kuti zinthu ndi kagwiridwe kanchito kapena kayendetsedweka ndende zikuchitika potsatira mmene mayiko ena amamchitira pa nchito ya mtundu womwewo ;

b) Lidzakhala ndi mphanvu zimene zingachitike kuti lifufuze nkhani ndipo lidzakhala ndi mphamvu kuitanitsa munthu aliyense kuti ayankhe nkhani zimene zikukhudzana ndi zofufuzidwazo;

c) Lidzakhala ndi mphamvu loyendera ndende zonse kapena za ndende ngakhale palibe uthenga uliwonse ku ndendeko, ndipo wlna asawaletse; ndipo

d) Lidzagwira nchito iltyonse imene malamulo angafune kuti ligwire.

(4) Bungwe Loyendera Ndende Iilone kuti lapereka ku Nyumba ya Malamulo malipoti amene ilo lalemba ndipo malipotiwo azidzera kwa Nduna yoona za Ndende ngati mfundo yoti ivomereze malangizo operekedwa ndi bungwe loyendera ndende.

(5) Ngati malangizowo ngofuna kuti malamulo asinthidwe, ndunayo ipereke mfundoyo mokonza bilo.

(6) Mphamvu zapatsidwa kwa Oyendera Ndende mu ndime inozizagwiritsidwa nchito pokhudza malo osungiramo anthu ku Polisi asanawaimbe mlandu.

170.

(1) Bungwe Loyendera ndende lidzakhala ndi mamembala awa:-

a) Oweruza m'Bwalo la pamwamba la Apilo kapena Oweruza m'Bwalo Lalikulu la Milandu amene azasankhidwa ndi bungwe Loona za oweruza,amene azakhala Wapampando.

b) Wamkulu Woyang'ganira Ndende za boma kapena munthu 'M:>sankhidwa ndi wamkuluyo kuti azimuimila, yemwe ndi mmodzi wa akulu akulu ogwira nchito za ndende ;

c) Membala wa Bungwe loona za Ndende, kupatula wmkulu woyag'anira ndende nthawi ndi nthawi kuti aimire Bungwelo;

d) Wozenga Mlandu *(Magistrate)* yemwe adzasankhidwa nthawi ndi nthawi ndi bungwe loona oweruza kuti aziwaimira; ndi

e) Ombudzimani.

(2) Oyendera Ndende ali ndi mphamvu kusankha anthu kuti aziimira mabungwe a muno m'Malawi kapena akunja awo akugwira nchito kuno za ali ndi chidwi kuona za mmene ufulu wa anthu akutetezedwera kapena amene ali ndi chidwi ndi miyoyo ya anthu ochimwira malamulo monga momwe Oyendera Ndende angaonere.

## MUTU XVIII

## ZACHUMA

171. Palibe msonkho wa mtundu uliwonse umene udzakhazikitsidwa kapena kugwira ntchito ya Boma kapena ya makhonsolo popanda kuloledwa ndi malamulo.

172. Ndalama zonse zosonkhedwa mdzina la boma zidzasungidwa ku Thumba lapadera lotchedwa (Consolidated Fund) pokha pokha ngati Malamulo ano, kapena Malamulo ena akunenera mwina.

173.

(1) Palibe ndalama zimene zizatulutsidwe kuthumba lapadera pokhapokha ngati-

a) Ndi zofunika kuti alipire kuchoka ku Thumba lapaderalo motsata Malamulo ana kapena Malamulo ogwirizana ndi Malamulo ano.

b) Ngati kuloledwa kuti ndalamazo ziperekedwe ndi Lamulo lotchedwa *"Appropriation':* kapena loonjezera apo, kapena ndi lamulo lopangidwa motsata ndime (5), kapena ndime izi: 178, 179, 180, 181, kaya 182, kapena motsata mfundo ya nyumba ya malamulo monga momwe ndime 177 ikunenera:

Koma ndime ino sidzagwira nchito ndi ndarama zimene zachulidwa mundime

(2) Ngati ndalama zilizonse zifunika ku Thumba lapadera motsata mmene Malamulo ana kapena Malamulo ena anganenere, ndalamazo ziperekedwe kuchokera kuthumbalo ndi nduna ya zachuma kwa munthuyo kapena kubungwe kofunikirako.

(3) Palibe ndalama zitulutsidwe kuchokera ku Thumba la padera kupatula m,njira imene nyumba ya malamulo yagamulira.

(4) Ngati ndalama zisungidwa kubanki kapena kwina kwina kuchokera ku Thumba lapadera mobvomerezedwa ndi Nyumba ya Malamulo sindiye kuti zatulutsidwa kUchokera kuthumba lapadera monga mmene Malamulo ana akunenera ayi.

(5) Ngakhale ndime 1 ikunena izo, chikonzero chatha kupangidwa ndi nyumba ya malamulo kuti ndalama zitulutsidwe kuchokera ku thumba lapadera monga kungafunikire komanso potsata lamulokuti alipire anthu kapena mabungwe amene si a Boma;

*Malingana kuti-*

a) Palibe ndalama zitulutsidwe kuchokera njira yobwereka ku Thumba lapadera motsata ndime ino pokhapokha ngati zidzabwezedwe ndi munthuyo kapena bungwe limene labwerekalo.

b) Ndime ino siizagwira nchito mokhudza:-

(i) Ndalama zobwezedwa kuboma zimene adakongola pazifukwa zokwanira motsata Malamulo;

(ii) Ndalama kapena chiongoladzanja,zimene Boma lingalandire kuri zisamalidwe kapena zisungidwe;

(iii) Ndalama zoperekedwa nthawi yake isanakwane kapena kubwezedwa nthawi isanakwane monga momwe Nyumba ya Malamulo ingalamulire, ndi

(iv) Ndalama zapadera malinga ndi malamulo ana ngati ndime ino siloledwa kugwira nehito pa ndaramazo.



(1) Kuthumba lapaderali kusungidwe ndalama kuphatikizapo ndalama zongopatsidwa, malipiro kapena ndalama zina zomwe malamulo ana kapena malamulo ena anganenere:-

a) Ndalama zonse zobwezera ngongole za boma;

b) mapensioni onse, komanso ndalama zaehipepeso ngati munthu waehotsedwa panehito ndi ndalama zolipilira anthu opuma pa nehito ngati liyenera kugwapo.

c) Ndalama zolipilira mlandu wotsutsa boma woweruzidwa ndi bwalo loweruza, kapena bungwe lililonse, kupatula ndalama zomwe zapatuludwa ku Thumba Laehipepeso limene likhudza dziko lonse; ndiponso.

d) Ndalama zonse kapena ndalama zobwezera ngongole zimene ziyenera kulipidwa ndi thumba la Boma pa tsiku lomwe Malamulo ana adayamba kugwira nehito.

*(2) "Ngongo/e* za *boma"* zikuphatikizapo ehiongola dzanja, *(Sinking fund Charge),* ndalama zobwezela ngongole ya ndalama yeniyeniyo nthawi yoibweza ikakwana komanso ndalama zimene zimalipidwa pang'onopang'ono kuti ngongoleyo ithe.

175.

(1) Nduna ya za Chuma idzapereka ku Nyumba ya Malamulo ndondomeko malisiti ndi ya ndalama zimene boma lagwiritsira ntchito mchakacho kupatula ndalama zochulidwa mu ndime (3).

(2) Ndondomeko iperekedwe ku Nyumba ya Malamulo kukhudza ehaka ehiliehonse ndipo iperekedwe ehisanayambe chaka ehimene ndalamazo zigwire *nchito.*

(3) Ngati nyumba ya malamulo ifuna kuti ndondomekoyo aikambirane mpaka ehaka eha ehuma chitayamba ndondomeko ya umo ndaramazo zigwilire nchito atha kuipereka nthawi ina iliyonse kukambilanako kusanayambike.

(4) Ndondomekoyo idaonetsa paderapadera:-

a) Ndalama zonse zofunika kuti zigwire nchito kuchokera ku thumba lapadera; ndi

b) Ndalama zofunika kuti zigwiritsidwe nchito pa mitu ya ndalama zogwirira nchito kuchokera kuthumbalo.

(5) Pandalama zoti zioneke m'ndondomeko ya malisiti komanso zoti . azigwiritse nchito asaphatikizepo:-

a) Ndalama zolowa kuchokera kungongole ya boma kuti igwire nchito zofunika ndiponso motsata Malamulo obvomeleza kuti ngongoleyo aibwereke.

b) Ndalama kapena chiongoladzanja zolandilidwa ndi Boma koma zoti zisamalidwe m'malo mwa ena kuti zisamalidwe kapena zigwiritsidwe nchito mosamala eni akewo.

c) Ndalama zimene zabvomerezedwa kuti akongoze kuchokera ku Thumba la padera motsata Malamulo komanso ndalama zobwezedwa pa ngongoleyo.

d) Ndalama zimene zingalandilidwe kuti zigwire nchito ku Thumba lapadera lililonse kapena kutulutsidwa ku thumba limene linakhazikitsidwa ndi Malamulo ana kapena Malamulo ena ngati Malamulowo agamuliratu kuti ndime (1) ndi (4) zisagwire ntctlito kuthumbalo.

176.

Ngati ndalama zoti azigwiritse nchito kuchokera ku Thumba lapadera zabvomerezeka ndi Nyumba ya Malamulo, Bilo ya *'Appropriation'idzatulutsidwa* m'Nyumba ya Malamulo, kuti ndalama zofunikazo azazitulutse kuchokera ku Thumba lapaderalo ndi kuti zigawidwe pa zinthu zosiyasiyana zomwe zabvomerezedwa mwakuchita voti kuti zigwire nchito yochulidwa mu Biloyo.

177.

(1) Ngati papezeka, m'chaka china chilichonse chandalamazo, kuti:-

a) Ndalama zoti zigwire nchito iliyonse n'zochepa kapena kuti kwaoneka zina zofuna ndalama pamene ndalamazo sizinaperekedwe mu 8ilo yogawa ndalamayo; kapena kuti

b) Ndalama zalowa zambiri kunchito mobzyola zimene adavomereza kuti zigwire nchito malinga ndi malamulo la *"Appropriation"* pakonzedwe masamu ena oonjezera ndi kupita kwina nawo ku nyumba ya malamulo, ndipo aonetse ndalama zofunikazo kapena zimene zagwira nchitozo, ndiponso mitu yofuna kuonjezerapoyo iyikidwe m'kati momwemo kapena mkati mwa mfundo yobvomereza ndalama zofunikazo.

(2) Ngati ndalama zoonjezerapozo zabvomerezedwa pachakacho ndi mfundo ya nyumba yamalamulo motsutsa ndime (1) 8ilo yoonjezera ndalamaaipereke kunyumba ya malamulo mofulumira chikango yambika chaka china kuti ndalama zimene zavomerezedwazo athe kuzitulutsa.

(1 ) Nyumba ya Malamulo itha kukonza mfundo zothandiza kuti Nduna

ya za

Chuma igamule zoti ndalama zitulutsidwe kuchokera ku Thumba lapadera kuti zigwire nchito za Boma zofunika, ngati Ndunayo iona kuti lamulo logawa ndalama silitha kugwira nchito pamene chaka chizayamba, miyezi inai kuchokera pamene chakacho chiyambe kapena mpaka Bilo yogawa chumayo iyambe kugwira nchito, motsata chimene chiyambe pa ziwirizi.

Koma chikonzero cha ndalama zotulutsidwazo chikhalemo mu Bilo yotulutsila ~dalamayo, pansi pa mitu yake.

(1 ) Nyumba ya Malamulo itha kukonza mfundo zothandiza kuti Nduna

ya za

Chuma igamule zoti ndalama zitulutsidwe kuchokera kuhumba lapadera kuti zigwire nchito za boma zofunika, ngati ndunayo iona kuti lamulo logawa ndalama silitha kugwira nchito pamene chaka chiziyamba, miyezi inai kuchokera pamene chakacho chiyambe chiyambe mpaka Bilo yogawa chumayo iyambe kugwira nchito, motsata chimene chiyambe pa ZIWlZI.

(2) Ngati ndalama zituluka kuchokera kuthumba limeneli chikonzero

chakuti

paonjezeke ndalama chiperekedwe ku Nyumba ya Malamulo mwamsanga kuti ikabvomereze kuonjezeraku,' ndipo Bilo yakuti ponjezeke ndalama kapena mfundo yoonjezereka ikonzedwe monga momwe ikunenera ndime 176 kuti palowe ndalama zina pa ndalama zotulukazo.

(1) Boma lingathe kukongola ndalama motsata lamulo lopangidwa ndi nyumba ya Malamulo, apo ayi.

(2) Pogwiritsa ntchito lamulo lobvomerezeka kuti akongole ndalamazo, I kapena lamulo lina, Nyumba ya Malamulo, ingathe kugamula kuti ndarama za ngongole zigwire nchito yomwe aichula ndiponso kuti ndalama za ngongole azilowetse ku thumba lapadera kuti zigwire nchitoyo.

(1) Lamulo lopangidwa ndi Nyumba ya Malamulo lingate, mosalakwira

ndime

182, kukonza kuti pakhale matumba apadera a ndalama oti azigwirc

ntchito m'kati mwa Thumba ndi kukonza ndondomeko za momwe matumba otero'NO aziya ng'aniridwa.

(2) lamulo lopangidwa ndi ndime (1) Iingathe kugamula kuti ndime 175 (1) ndi 175 (4) zisagwire nchito ku Thumba Iililonse.

(3) Nyumba ya Malamulo ingathe kukonza ndondomeko ya momwe igwiritsire nchito ndalama zimene Boma likusamala m'malo mwa ena.

182.

(1) Padzikhala Thumba linanso mkati mwa Thumba la padera, lotchedwa Thumba la Ndalama Zochitira ChitukuKO kuti lizigwira ntchito ya chitukuko m'dziko muno. Thumbali likhudza ndalama zomwe sanaziike mu dongosolo limene lili mu ndime 175, ndipo chikonzero cha malisiti ndi cha ndalama zotuluka mmenemo cchiperekedwe ndi Nduna ya za Chuma m'Nyumba ya Malamulo kosachepera kamodzi pa chaka.

(2) Nyumba ya Malamulo ikabvomereza dongosolo la ndalama zofunika kuti zikhale ku Thumba zochitira chitukuko, bilo yochedwa *"Appropriation"* (Development Fund) aipereke m'Nyumba ya Malamulo kubvomereza zoti ndalama zofunika zitha kutulutsidwa ku Thumbalo kuti zigwire nchito ya chitukuko.

183.

(1). Padzakhala Thumba lina m'kati mwa Thumba lapadera m'mene muzichokera ndalama zotetezedwa ..

(2). Nduna ya za Chuma, chisanayambe chaka, idzakonza njira mu Bilo ya *Appropriation* yosungira ndalama zotchulidwa pa ndime (1) ndipo chikonzero chimenechi chivomerezedwe ndi Nyumba ya Malamulo popanda kuchotsera kapena kuonjezera, pokha pokha ngati sichingakwane kugwira nchito yake pamenepo nyumba ya malamulo ingathe kukonzanso Biloyo kuti ndalama zake zikwanire.

(3). Palibe ndalama zoti zitulutsidwe kuchokera kuthumba lapadera kuti zigwire nchito kupatula izi

a) Ndalama zolipila president ndi wamkulu woweruza.

b) Ndalam zolipilira Ombudzimani.

c) Ndalama zogwiritsa nchito kuti nyumba ya malamulo ikumane.

184. (1 )Padzakhala wamkulu ounikira m'mene ndalama za boma zikugwirira nchito (Auditor General) yemwenso azidzaunika ndi kupereka lipoti la m'mene ndalama za Boma zagwirira nchito, ndipo iyeyu adzakhala ndi mphamvu zina zilizonse zounikira ndalama za Boma kapena za mabungwe a boma ndi ena monga momwe lamulo linganenere, ngati kuteroko kugwirizana ndi nchito yake.

(2) Wamkuluyo adzapereka malipoti ku Nyumba ya Malamulo kudzera mwa Nduna ya za Chuma kamodzi koma kapena kangapo pachaka komatu kosalephera pamene Nyumbayo ikukumana koyamba ndipo adzalemba lipotilo Nyumbayo isanakumane

(3) Wamkuluyu adzasankhindwa ndi Pulezidenti ndi kubvomerezedwa ndi Nyumba ya Malamulo kudzela awo angachuluke pa voti ya nthumwi izo zilipo, koma Komiti Yolemba Antchito za Boma ingathe, nthawi ina iliyonse kufufuza ngati munthuyo angathedi kugwira ntchito za pa udindowo ndiponso ngati munthuyo ndi wokhulupirika pa ndalama mongokhudza mmene zingathandizire pa udindo wake.

(4) Mpando'NU udzakhala wopanda munthu mwiniyo akayigwira ntchitoyi kwa zaka zisanu ndipo angathe kusankhidwanso kwa nthawi, yosabzyolera zaka zisanu zina monga momwe Pulezidenti angaganizire.

(5) Mpandowu udzakhala wa ntchito za Boma.

(7) Wamkuluyo angathe kuchotsedwa ndi Pulezidenti pa zifukwa izi basi

a) ngati sadziwa ntchito kapena udindo wake;

b) ngati wachita chinthu chosayenera pantchitoyo kapena pa udindowo kotero kuti n'kokayikitsa ngat,i angathe kuchita chilungamo pa nkhani ya ndalama;

c) sangathenso kugwira ntchito pa zifukwa zina; kapena:-

d) Wakwanitsa zaka zoti apume pa ntchito yake.

(7) Kupatula zonenedwa pa ndime (6), akamagwira ntchito imene Wamkuluyu wapatsidwa munthu wokhala pa mpando umenewu sadzauzidwa chochita ndi ena kapena kukhala pansi pa munthu wina kaya bungwe lina.

(8) Palibe munthu amene aloledwe kumutchingatchinga Wamkuluyu akamagwira ntchito yake poyendetsa undindo wake.

## MUTU XIX

**NYUMBA YAIKULU YOSUNGILAMO NDALAMA ZA BOMA (RESERVE BANK)**

185. (1)
Malamulo adzakhazikitsa banki yaikulu mdziko muno yotchedwa Rizevu Banki ya Malawi imene idzagwira ntchito ya Boma yoona kuti pali dongosolo la ndalama ndipo sizikusowa, ndi kuyang'anira mabungwe a ndalama ndipo idzagwira ntchito zonse zimene banki yaikulu imagwira m'dziko.

(2)
Bankiyi idzakhala pansi pa Bungwe limene lidzakhala ndi Wapampando ndi mamembala amene malinga ndi Malamulo ana adzasankhidwa motsata Malamulo okhazikitsa Bankiyo.

# MUTU XX
# OGWIRA NTCHITO ZA BOMA

186. (1) Padzakhala Bungwe Loona za Ogwira Ntchito za Boma limene lidzakhala ndi mphamvu komanso undindo wopatsidwa ndi Malamulo ana kapena Malamulo ena, ndipo lidzakhala ndi wapampando, wachiwiri wake, komanso mamembala osachepera 6 koma osaposera 10.

187. (1)' Motsata Malamulo ano, mphamvu yosankha anthu ogwira ntchito za Boma kapena kukhala pa udindo wantchito za Boma kuphatikizapo kutsimikizira kuti akhazikike pa pandowo, komanso kuwachotsa athuwo pa ntchito, idzakhala m'manja mwa Bungwe loona za anthu ogwira ntchito za Boma.

(2) Motsata Malamulo ana ndi Malamulo ena, Bungwe Loona za Ogwira Ntchito za Boma lidzakhazikitsa mwambo pa anthu ogwira ntchitowo, kapena kukhala pa mpando umene ukukhudzidwa ndi Mutu uno.

188. (1) Bungweli lingathe kupatsa mphamvu zili pa ndime inozi kwa membala wake kapena kwa munthu aliyense wogwira ntchito za Boma kapena bungwe lina, kudzera m'chikalata koma motsata mfundo zimene Malamulo adakhazikitsa.

(2) Ngati munthu kapena bungwe apatsidwa mwayi wogwiritsa ntchito mphamvu motsata ndime ino m'malo mwa Bungweli, mogwirizana ndi ndime (1), Bungweli:-

a) lifunse munthuyo kapena bungwelo kuti apereke lipoti monga momwe adagamulira m'chikalata chimene ampatsira mphamvuzo;

b) Lilandirenso madandaulo kaya apilo kuchokera Kwa anthu okhudzidwa ndi

momwe akugwiritsa ntchito mphamvuzo motsata ndime ino ndiponso lili ndi mphamvu.

c) Kulamula kuti kugamula kumene munthu kapena bungwe limene likugwiritsa ntchito mphamvuyo kunachitika kulibe mphamvu;

ii) Kugwiritsa ntchito mphamvu zosungitsa mwambo pa munthuyo kapena pa bungwelo; molondoloza zonse zofunika ndi Nyumba ya Malamulo;

iii) Kubweza mphamvu zimene zidapatsidwa kwa munthu aliyense kapena bungwe.

82

Koma palibe chilichose m'ndime ino chimene chidzaletsa munthu yemwe akhudzidwa ndi mfundo yopangidwa ndi, kapena m'malo mwa, Bungweli kugwiritsa ntchito ufu1u wochita apilo ku Bwalo Lalikulu la Milandu, kapena kuchotsa ufulu wa munthu amene akukhudzidwa ndi chiweruzocho kuti adandaule ku Bwalo pa nkhaniyo ndi kukhutitsidwa ngati Bungwelo lachita chilungamo chenicheni pa chiweruzocho.

189. (1) Mutu uno sudzagwira ntchito ngati Malamulo ana alongosola za momwe ogwira ntchito za Boma kapena aliyense wosankhindwa pa mpando wa Boma adzamusankhila kapena kumchotsera, ndipo siukukhudza ntchito zimene amagwila a Bungwe Loona za Oweruza, Bungwe Loona za a Polisi, Bungwe Loyendetsa Ndende za Boma, kapena zolongosoledwa ndi malamulo okhudza kasankhidwe ka mipando ya Asirikali a Nkhondo muno m'Malawi, ndipo mutu uno sudzakhudzanso:-

a) Wamkulu wa Oweruza, Wamkulu wa Malamulo kapena Wamkulu Wozenga Milandu ya Boma;

b) Anthu ogwira ntchito kwa Pulezidenti amene angafune koma mobvomerezedwa ndi komiti yolemba za anthu ogwira ntchito za Boma, kapena mmene Malamulo anganenere;

c) Mlembi wa Kabineti;

d) Akazembe ndi akulu ena otumikira Boma ku mayiko akunja monga ndime 190 (1) ikunenera;

e) Atsogoleri a Nkhondo akuluakulu;

f) Wamkulu Woona za a Polisi;

g) Wamkulu Woona za Ndende za Boma;

h) Mpando wa Mlembi mu unduna;

i) Mpando uliwonse wapamwamba monga Malamulo anganenere.

(2) Pokhapokha ngati Malamulo ana kapena Malamulo ena anganenere. Mphamvu yosankha anthu pa mipando ya m'boma imene yatchulidwa pa ndime (a) mpaka (I) ya ndime (1) idzakhala m'manja mwa Pulezidenti.

(3) Bungwe Loona za Antchito za Boma pamene ligwilitsa ntchito mphamvu yosankha Mlembi wa Nyumba ya Malamulo kapena Seniti kapena wachiwiri wake, lisanagwiritse ntchito mphamvuyo likambirane ndi Sipikala wa Nyumba ya Malamulo kapena wa Seneti.

190. Akazembe ndi' akulu ena oimira Boma ku mayiko a kunja monga lamulo linganenere adzasankhidwa ndi Pulezidenti ndi kutsimikizidwa ndi Komiti Yolemba a Ntchito za Boma imene ingathe kufunsa anthuwo ngati angathedi kugwira kapena kuona za kukhulupirika kwawo pa ndalama.

Mamembala a Bungwe Loona za Antchito za Boma adzasankhidwa ndi Pulezidenti Komit Yolemba Antchito za Boma ikhutire kuti angathe kugwira ntchito pa udindo wa membala wa Bungwelo.

Palibe munthu yemwe angathe kudzasankhidwa ngati membala wa Bungwe Loona za Antchito za Boma ngati ndi Pulezidenti, Wachiwiri kwa Pulezidenti, Nduna, Nduna yaing'ono, Membala wa Nyumba ya Malamulo, kapena wogwira ntchito za Boma ngati sanapume.

Kupatula mmene ndime ino ikunenera mpando wa membala wa Bungwe Loona za Ogwira Ntchito za Boma udzakhala wopando munthu:-

a) pakatha zaka zisanu kuchokera pa tsiku limene munthuyo adasankhidwa, pokhapokha ngati wasankhidwanso kuti apitirire kugwira ntchitoyo kosabzyolera zaka zina zisanu, kapena

b) Ngati paoneka kapena kuchitika china choti, kukadakhala kuti sanali membala wa Bugwelo ndiye kuti munthuyo sakadakwanitsa kusankhidwa pa udindowo.

(4) Membala wa Bungweli angathe kuchotsedwa ntchito ndi Pulezidenti ngati komiti Yolemba a Ntchito za Boma ikhutira kuti membalayo sakukwanira' pa udindo wake:-

Koma palibe chinthu chilichonse m'ndime ino chimene chingaletse ufulu wa membala wochotsedwayo kuti achite apilo ku Bwalo Loweruza Lalikulu Potsutsana ndi maganizo oti amchotse.

192. (1) Ngati Wapampando wa Bungwe Loona za Ogwira Ntchito za Boma palibe kapena wapampando sangathe kugwira ntchito yake pa chifukwa chilichonse, ndiye kuti Wachiwiri wake agwire ntchitoyo mpaka Wapampando watsopano atasankhindwa, kapena mwini mpandoyo atayambanso kugwira ntchito yake.

(2) Ngati Wapampando kapena Wachiwiri wake sangathe kugwira ntchito yake ndiye kuti mmodzi wa mamembala a Bungwelo yemwe angasankhindwe ndi mamembala otsalawo agwirizire mpandowo.

(3) Ngati pa nthawi ina iliyonse papezeka mamembala ochepera 7 a Bungweli, ndipo Komiti Yoona Olemba Anthu Antchito za Boma sangathe kukumana chifukwa chakuti Nyumba ya Malamulo idathetsedwa kapena pa chifukwa china, Pulezidenti angathe kusankha mamembala ena a Bungweli monga mmene kungafunikire kuti agwire ntchito m'Bungweli;

Koma nthawi yakungogwirizira yaosankhidwa ngati membala wa Bungweli monga momwe kuloledwa ndi ndime ino idzatha ngati munthuyo amusankha ngati membala payekha monga ndime 191 (1) ikunenera, kapena ngati pa mpando umene

akugwirizirawo papezeka munthu nthawi yakuti komiti yolemba ogwira ntchito za Boma yayambanso kugwira ntchito.

193.

(1)Ogwira Ntchito za Boma azionetsetsa kuti zochitika ndi iwo pa ndale zisawalepheretse kugwiritsa ntchito mphamvu pa undindo awo ngati otumikira anthu mosakondera ndiponso mosagwedezeka.

(2)
Nyumba ya Malamulo ingathe kukhazikitsa ndondomeko ya Ogwira Ntchito ya Boma malinga ndi udindo wawo pa ntchito za Boma omwe asamachite nawo za ndale poyera;

*Koma*

a) Ogwira ntchito amenewo ali ndi ufulu kutula pansi mipando yawo kuti azichita nawo zandale poyera;

b) Palibe chilichonse pandime ino chimene chingamuletse munthu wogwira ntchito za Boma kuchita voti monga momwe Malamulo ana akunenera.

c) Ngakhale ndime (1) ikutera munthu wogwira ntchito za Boma amene undindo wake sukugwapo pa kupanga mfundo kapena kuyendetsa mfundo za Boma asakhudzidwe ndi zoletsa zili pandime ino; ndipo

d) Palibe chilichonse chomWb chidzamuletsa wogwira ntchito za Boma kukhala pa mpando kapena membala wa gulu, kapena bungwe kapena lokhudza ukatswiri pantchito ngati cholinga chake ndi kuimira mamembala awo pa zowakomera pantchito monga kungakhalire kapena ngati akuyendetsa ukatswiri wawo kapena kupititsa mtsogolo zina zosakhudzana ndi zofuna za chipani chake kapena momwe chipanicho chimachitira kampeeni yake.

(3) Palibe Boma, kapena chipani cha ndale chilichonse, limene lidzagwilitsa ntchito munthu wogwira ntchito za Boma kuti ali pa mpandopo agwiritse ntchito mphamvu kapena undindo wake ndi cholinga choti apititse mtsogolo kapena abwezere m'mbuyo ndale za chipani chilichose kapena mmodzi m'chipanimo, ndipo sikuloledwa kuti munthu wogwira ntchito za Boma agwiritse ntchito mpando wake ndi cholinga chopititsa mtsogolo kapena kubwezera m'mbuyo chipani cha ndale kapena membala wa chipanicho, pokhapo ngati zochitikazo zikugwirizana ndi ino.

(4) Boma kapena chipani chanda Ie zisamchititse munthu wogwira ntchito za Boma kuti aononge chuma, ndalama, zida kapena kuti agwiritise ntchito m~nthu ndi cholinga choti apititse mtsogolo kapena kubwezera m'mbuyo chipani cha ndale, membala wa chipani kapena guli lina, ndipo palibe wogwira ntchito za Boma amene adzagwiritsa ntchito mpando wake motero, pokhapokha ngati Malamulo ana atero kapena ngati Lamulo limene ligonjera ndime (7) likulola.

(5) Munthu wogwira ntchito za Boma yemwe alakwira ndime ino atha kulandira chilango monga monga momwe Bungwe Loona Ogwira Ntchito za Boma lingaganizire, ndipo Bungweli lichite moganizira kuopsya kwa cholakwacho, koma motsata ndondomeko zimene Malamulo ana angazibvomereze.

(6) Ngati Bungweli Iikhutira kuti Boma kapena chipani chandale kapena membala wa chipani chandale walakwira ndime (3) kapena (4) Bungweli lith a kuimba mlandu woti wolakwayo amulipitse kokwana, ndipo ngati adalakwira ndime (4) kuti abweze ndalama kapena zimene anagwiritsa ntchitozo mofanana ndi mmene zinathandizira, kuchokera ku Boma, chipani cha ndale kapena membala monga momwe zingakhalire.

194. Ngati lamulo lipatsa mphamvu yosankha bungwe, bwalo, khonsolo, komiti kapena china chofanana, ndi mphamvu kuti asankhenso kapena kukhazikitsa wa pampando wache palibe munthu adzasankhindwa kapena kulolezedwa ngati wapampando wamabungwe, komiti, mankhonsolo kapena mabwalo awiri, koma akhale pa mpando umodzi wokha.

# <u>MUTU XXI</u>

# KUSINTHA MALAMULO OYENDETSERA BOMA

195.Nyumba ya Malamulo ingathe kusintha Malamulo ana motsata Mutu uno.

196. (1) Kupatula momwe Malamulo ana anganenere. Nyumba ya Malamulo ingathe kusintha Mutu uno ndime za Malamulo ana zimene zili mu mlozo (Schedule) koma pokhapokha ngati:-

a) Mfundo yoti isinthidweyo ndiponso mfundo ya kasinthindweyo aipereka kwa anthu kuti aibvomereze kapena kuikana pa voti ya Liferendamu, ndipo ambiri a anthu atsimikize ndi voti yawo kuti mfundoyo isinthikedi; ndipo

b) Bungwe loona za Chisankho latsimikizadi kwa Sipikala kuti votiyo ndimo yayendera.

(2) Nyumba ya Malamulo ingathe kupereka Bilo yosintha lamulo limene ndime (1) yakhwanitsa pa voti ngati obvomereza m'Nyumbamo ndiwo achuluka kuposa otsutsa.

(3) Ngakhale ndime (1) ikutero, Nyumba ya Malamulo ingathe kubvomereza Bilo momwe muli ganizo losintha zomwe ndimeyo ikunena posagwiritsa ntchito Liferendamu ngati

a) kusinthako sikukhuza mfundo zenizenizo m'Malamulo ano;

b) Sipikala watsimika kuti ndi choncho, ndipo;

c) Biloyo yabvomerezedwadi ndi anthu osachepera 2/3 ya mamembala onse amene ayenela achita nawo voti m'Nyumba ya Malamulo.

197 Mosamala ndime 196, Nyumba ya Malamulo ingathe kusintha Mitu ndi ndime za Malamulo ana zimene sizikutchulidwa mu mlozo pokhapokha ngati Bilo yoti pakhale kusinthayo ibvomerezedwa ndi 2/3 ya kuchuluka kwa mamembala orise a Nyumbayo omwe ali ndi ufulu wochita voti.

# MUTU XXII

## ZINA NDI ZINA MALINGA NDI KUSINTHAKU

198.

Dziko la Malawi, magawo a Boma ndiponso mipando imene yatchulidwa mu Malamulo ano, zonsezi adzazilongosola ndi kuzikhazikitsa motsata Malamulo ano.

199.

Malamulo ana adzakhala ndi mphamvu ya Malamulo kuposa Malamulo ena onse; ndipo sipadzakhala olamula kapena mphamvu ya ndale kupatula amene Malamulo ana akhazikitsa.

200.

Pokhapokha ngati atsutsana ndi Malamulo ano, Malamulo onse opangidwa ndi Nyumba ya Malamulo, Malamulo a kale komanso a miyambo ya anthu omwe adalipo patsiku limene Malamulo ana adayamba kugwira ntchito adzapitirira kukhala ndi mphamvu ya malamulo, ngati kuti adapangika kapena adakhazikitsidwa motsata, koman~o mosamala Malamulo ana

Koma Malamulo alionse amene pakali pano akugwira ntchito atha kusinthidwa kapena kuchotsedwa ndi lamulo lopangidwa ndi Nyumba ya Malamulo kapena kukanidwa kuti lisagwire ntchito chifukwa choti likutsutsana ndi mphamvu ya ulamuliro.

201.

Malinga ndi Malamulo ana m'Nyumba ya Malamulo yoyamba kuchokera tsiku limene Malamulo yoyamba kuchokera tsiku limene Malarriulowa adzayamba kugwira ntchito mudzakhala anthu opambana pa chisankho cha aphungu a Nyumba ya Malamulo motsata Malamulo amene analikugwira ntchito kukhudza chisankho cha mamembala a ku Nyumba ya Malamulo.

202.

Malinga ndi Malamulo ano, Pulezidenti woyamba, Malamulowa akadzayamba kugwira ntchito, adzakhala munthu amene adzapambane pa chisankho motsata Malamulo amene adzakhala akugwira ntchito pokhudza chisankho cha munthu woti akhale Pulezidenti.

203.

Bwalo Loweruza Lalikulu lizidzasengabe milandu, komanso Iidzakhala ndi mpharrwu ndi ndondomeko monga zidalili Malamulo asanayambe kugwira ntchito, koma motsata kusintha kwa mphamvuzo kumene Malamulo angachite molondoloza Malamulu ano.

204.

(1) Milandu yonse imene idzakhala ili m'mbwalo la milandu nthawi imene Malamulo ana adzayambe kugwira ntchito, kupatula m'Bwalo la Pamwamba la Apilo, m'Bwalo Lalikulu la Milandu, m'Bwalo la Majisitireti, m'Bwalo la Apilo pa Miyambo, mbwalo la miyambo pa Boma m'Bwalo la Giredi A la Miyambo kapena Giredi B la miyambo, idzayamba kapena kupitirira m'Bwalo la milandu la pamwamba, kapena m'Bwalo la Majisitireti, Lamiyambo la apilo pa Boma, la Miyambo pa Boma, lamiyambo la Giredi A kapena Giredi B monga Kalembera wa m'Bwalo lalikulu la milandu anganenere.

(2) Milandu yonse yomwe ili m'Bwalo la Majisitireti pa nthawi imene Malamulo ana adzayambe kugwira ntchito idzasengedwa m'bwalo lomwe lidali ndi mphamvu ndi dongosolo lofanana nalo isanafike nthawi yomwe Malamulo ana adayamba kugwira ntchito, koma mphamvuzo zingathe kusinthidwa ndi Malamulo ana kapena ndi malamulo opangidwa ndi Nyumba ya Malamulo.

(3) Milandu yonse yomwe ili m'bwalo lomwe lidzakhala ndi mphamvu ndi dongosolo la mtundu womweyo Malamulowa asanayambe kugwira ntchito, koma mphamvuzo zingathe kusinthidwa ndi lamulo lopangidwa ndi Nyumba ya Malamulo.

(4) Apilo zochokera ku Bwalo la Miyambo la Apilo, pa Boma kapena Bwalo la miyambo pa Boma zidzakhala ku Bwalo lalikulu la Milandu limene lingathe kugwiritsa ntchito munthu wopima mlandu wosankhindwa motsata Malamulo potero.

205. Chiweruzo chimene chidaperekedwa koma sichinayambe kugwira ntchito chidzagwiritsidwa ntchito monga ngati kuti chiweruzocho chidapatsidwa mogwirizana ndi Malamulo ano:

Koma ngati Malamulowa apereka ufulu wochita apilo pa zifukwa zoonjezerapo, apiloyo ikhale ngati kupempha kuti chiweruzocho chisayambe kugwira ntchito Bwalo lalikulu la milandu ndilo lilandire chidandaulo cha apiloyo.

206. (1) Kupatula mmene Malamulo ana anganenere, aliyense wogwira ntchito pa mpando malinga ndi malamulo amene adalipo Malamulo ana asanayambe kugwira ntchito adzapitirira pa mpandowo mpaka:-

a) munthuyo atatsimikizidwa pa mpandowo;

b) wina wapatsidwa mpando womwewo, ndiye kuti woyamba uja wachokapo koma motsata Malamulo ano;

c) munthuyo watula pansi mpando kapena wakwanitsa zaka zopuma motsata Malamulo ano.

Koma ngati Malamulo ana akhazikitsa mpando wa mtundu wina ndipo ntchito za mpando ngati omwewo akugwira ndi wina yemwe alipo pa nthawi imene Malamulo ana adayamba kugwira ntchito, ndiye kuti munthu ali pa mpando kaleyo agwiritse ntchito mphamvu ndi udindo umene wakhazikitsidwawo kuyambila pomwe malamulo ana ayamba kugwila ntchito.

(2) Pokhudza ndime 51 (2) ndi 80 (1), osati pachifukwa china chilichonse, munthu yemwe panthawi imene Malamulo ana anali atayamba kugwira ntchito pa mpando wa Wamkulu wa Oweruza adzakhala wosankhidwa pa mpando womwewo monga ngati wosankhindwa ndi Malamulo ano.

207. Motsatana ndi Malamulo ana malo onse ndi dziko lonse m'Malawi muno zidzasungidwa ndiBoma la Ripabuliki.

208. Boma lidzakhala ndi mphamvu zonse pa malo amene adzakhala m'manja mwa Boma la Malawi patsiku limene Malamulo ana adzayamba kugwira ntchito kupatula ngati ndime 209 (2) inganenere mwina, komanso palibe malo a Boma amene adachotsedwa m'manja mwa Boma popanda Nyumba ya Malamulo kubvomereza.

209. (1) Onse amene ali ndi ufulu wokhala ndi chuma nthawi imene Malamulo ana adzayamba kugwira ntchito adzapitirira kukhala ndi ufulu omweo pansi pa Malamulo ana nqi malamulo ena.

(2) Ndime ino ilibe mphamvu pa ufulu umene Boma liH nawo pa chuma chimene lachipeza kapena kuchithandizo ngati chumacho adachipeza nthawi yina iliyonse atapita 6 Julayi 1994 kapena ngati chumacho chidali cha nzika kapena anthu awo amakhala m'dziko mom'muno.

a) Mosatsata Malamulo a m'dziko muno;

b) Mogwira ntchito lamulo kupatula lamulo lokhudza mlandu wolakwira Boma limene silidakonze chipepeso chokwana; kapena

c) Ngati chumacho chidangosiyidwa chifukwa choopsyezenda ndi zifukwa zina.

(3) "Boma" malingana ndi ndime ino, litanthauza Pulezidenti, Kabineti, Maunduna, ndi Mabungwe a Pulezidenti ndi Kabineti ndi onse otumidwa ndi iwo kuphatikiza anthu wamba ndi magulu ena otumidwa ndi Pulezidenti, Kabineti ndi Maunduna.

(4) Mphamvu zimene sizizindikiridwa pa chuma malinga ndi ndime ino zidzakhala m'manja mwa Bungwe Loona za Chipepeso ndipo chumacho chidzagawidwa motsata malamulo ndi ndondomeko za Bungwe la Chipepeso.

(5) Anthu amene akugwiritsa ntchito chuma cha Bungwe la Chipepeso apitirire kutero, monga ngati zinthuzo zili kusamalidwa m'manja mwawo mpaka Bungwe la Chipepeso litagamulira mwina.

210. (1) Seneti siidzakhazikitsidwa mpaka pa mapeto a mwezi wa Meyi mchaka cha 1999.

(2) Mpaka Seneti idzakhazikitsidwe ndikuti mamembala ake asankhidwa.

a) Malamulo adzakhazikitsidwa ndi Nyumba ya Malamulo monga ngati kuti Malamulo ana sadzakhazikitse Seneti, ngatinso kuti GaVlO lopanga Malamulo ndi Nyumba ya Malamulo yogwira ntchito payokha mphamvu za Seneti, ndipo;

b) Malamulo ana adzagwiritsidwa ntchito ngati kuti Seneti siidapatsidwe ntchito;

Koma palibe chilichonse chimene wina aganizire kuti chakhudza malamulo olembedwa pa Mutu VI.

211. (1) Pangano lililonse lomwe Boma Iidagwirizana ndi mayiko akunja ndipo Iidabvomerezedwa ndi Nyumba ya Malamulo lidzakhala gawo la Malamulo a Boma Iino ngati zidalembedwa choncho mumalamulo okhazikidwa ndi Nyumba ya Malamulo amene adakhazikitsa mgwirizanawo.

(2) Mapangano omwe Boma Iidagwirizana ndi maiko ena Malamulo ana asanayambe kugwira ntchito ndipo ali ndi mphamvu m'Malawi muno

adzakhala gawo la Malamulo a dzik01ino pokhapokha ngati Nyumba ya Malamulo idzabwezera mwina kapena ngati panganolo latha nthawi yake yogwira ntchito.

(3) Malamulo a miyambo amene amagwira ntchito pakati m'mayiko ena Adzapitirira kugwira ntchito pokhapokha ngati akutsutsana ndi Malamulo ana kapena Malamulo ena.

# MUTU XXIII

# ZINA NDI ZINA

212. (1) Malamulo ana adzayamba kugwira ntchito mogwirizana pa 18 Meyi, 1994 limene ndi tsiku lokhazikitsa malamulowa ndipo adzagwira ntchito motero ngati Malamulo Oyendetsera Soma la Malawi kwa nthawi yosachepera kapena kuposa miyezi 12 kuchokera tsiku limenelo (tsiku limene pa ndime ino lizitchedwa (nthawi yogwiritsa ntchito Malamulo mogwirizira).

(2) M'nthawi imene Malamulo ana adzagwira ntchito mogwirizana, Nyumba ya Malamulo ingathe kukonza zina kapena kuthetsa Malamulowa malinga ndi mmene ndime ino ikunenera, koma motsata ndime 196.

(3) Pasanathe masiku 14 kuchokera pa tsiku limene Nyumba ya Malamulo idzakumane Malamulo ano atayamba kugwira ntchito, Nyumbayi idzasankha Komiti Yoona Malamulo Oyendetsera Soma yomwe idzakhala ndi Sipikala wa Nyumba a Malamulo ngati Wapampando ndi mamembala a Nyumba ena 10 'M:>sankhindwa ndi Nyumba ya Malamulo.

(4) Ntchito ya Komiti Yoona Malamulo ano idzakhala:-

a) Kuphunzitsa anthu, komanso kufufuza maganizo awo, pa Malamulo ano;

b) Kukonza msonkhano wokhudza dziko lonse ndiponso wa anthu oimira mbali zonse za chikhalidwe chathu;

c) Kupempha ndi kulandira maganizo a anthu a m'Malawi mmene Malamulowa angasinthidwire kapena kuona mmene Malamulo ena angathe kulow m'malo mwake;

d) Kulola Amalawi, motsata ndondomeko yake, kuti alembe maganizowo ndikuwatumiza ku Komitiyo kapena kuti adzawafotokoze okha;

e) Kulemba zonse zokudza maganizo amene alandiridwa ndikuwafalitsa kokwana;

f) Kutula malipoti ku Nyumba ya Malamulo pa nthawi yosachepera masiku 30 Nyumbayo isanawagwiritse ntchito malinga ndi ndime (g) monga momwe kungafunikire kuti apereke

maganizo awo pa nkhaniyo; ndiponso

g) Kukonza 8i10 kapena ma8ilo osintha Malamulo ano, monga ndime (5) ikunenera, 8ilo ya Malamulo yothetsa ndi kulowa m:malo mwa Malamulo ano, ndipo 8ilo iliyonse yotere idzakhala 8ilo payokha, yotchedwa 8ilo yosintha Malamulo a Soma, ndikupereka 8ilo imeneyo kapena ma 8ilo amenewo ku Nyumba ya Malamulo ngati mfundo yapadera.

(5) Ngati maganizo osintha Malamulowa akhudza mwambiri Nyumba ya Malamulo ingathe kuthetsa ndi kulowetsa m'malo mwake Malamulo oyendetsera 80ma ena m'nthawi imene Malamulo ano adzagwira ntchito lJ1ongogwirizira, koma zolowa m'malo mwakezo siziloledwa pasanachitike, kapena ngati zitsutsana ndi mfundo ya msonkhano wa dziko lonse umene ukutchulidwa pa ndime (4) (b).

(6) M'kati mwa masiku 30 nthawi yogwira ntchito mogwirizana isanathe, Nyumba ya Malamulo idzakhazikitsa Lamulo limene lidzakhazikitsa kotsiriza Malamulo ano (kuphatikizapo zosintha izo zingakhalepo m'kati mwake motsata ndime ino) kapena Malamulo oyendetsera 80ma ena kulowa m'malo mwa Malamulo ano, ndipo Malamulowo adzayamba kugwira ntchito pakutha pa nthawi imene Malamulo ano adzagwira ntchito mogwirizana.

(7) Bilo yopangidwa motsata ndime ino kuti isinthe kapena kuthetsa ndi kulowa m'malo mwa Malamulo ana idzakhala Lamulo pokhapokha ngati itabvomerezedwa ndi anthu osachepera 2/3 ya mamembala onse a Nyumba ya Malamulo ndipo siidzasinthidwa ndi Seneti.

(8) Pokhapokha ngati Malamulo ana akusinthidwa kapena kuchotsedwa kuti ena alowe m'malo mwake ndime ino siloledwa kusinthindwa, koma idzakhala yopanda mphamvu pakutha pa nthawi yomwe Malamulo ana adzakhala akugwira ntchito mogwirizana, kupatula mmene kungafunikire kuti Malamulo ana akhazikitsidwe ngati ndime (9) ingagwiritsidwe ntchito.

(9) Ngati Nyumba ya Malamulo sigwira ntchito monga ndime 6 ikunenera, Malamulo ana adzangokhazikitsidwa kotsiriza pakutha pa nthawi imene Malamulowa adzagwire ntchito mogwirizana.

213. Malamulo ana omwe ndi oyendetsera Boma la Malawi angathe Kungotchulidwa kuti "Malamulo ano"

214. Malamulo ano, pokhapokha ngati pangakhale zonena zina:-

"Tsiku lokhazikitsidwa" litanthauza 18 Meyi, 1994 tsiku limene Malamulo ana

adzayamba kugwira ntchito;

"Zaka zokwana kuti munthu apume pa ntchito" ndi zaka zakubandwa zimene lamulo lingakhazikitse kuti ndi zomwe zizikwana kuti munthu Wogwira ntchito za Boma apume pampandowo.